


# KUVUNDUKULIDWA

## KWA MULUNGU

 Tiyeni tikhalebe chiimire mphindi chabe pamene ife tikuveramitsa mitu yathu ku pemphero.

<sup>2</sup> Ambuye wathu Wachisomo, ife ndithudi tiri oyamikira lero chifukwa cha mwayi uwu umene ife tiri nawo wa kudzisonkhanitsa tokha pamodzi pa dziko lapansi kusanati Kudza kwa Ambuye. Mulole ife tiifufuze mitima yathu lero, ndi Mawu Anu, ndipo tiwone ngati ife tiri mu Chikhulupiro, kuti ife tikakhoze kukhala okonzekera, ora, lija la Kuwonekera Kwake. Kuti ife tikakhoze kukhala monga Lemba lanenera kuti ife tidzakhala, “Kukwatulidwira mmwamba limodzi, ndi iwo amene akugona, ndi kukakomana naye Ambuye mu mlengalenga, ndi kukakhala ndi Iye kwanthawizonse.”

<sup>3</sup> Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Mzimu woona wa Chikhristu umene ukadalipobe pa dziko lapansi, pakati pa anthu, kuti iwo akukukhulupiriranibe Inu ndi Mawu Anu. Kotero ife tikupempha madalitso Anu pa ife lero, kuti Inu muvumbitsire pa wina aliyense wa ife icho chimene ife tikuchisowa, kuti ife tikathe kuthiridwa ndi Mawu, kuti ife tikakule kukakhala zida zogwiritsidwa ntchito mmanja Anu, kwa tsiku lotsiriza lino. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, M’busa wathu wamkulu, yemwe ife tikumuyembekezera kuti awonekera. Amenii.

Mukhoza kukhala.

<sup>4</sup> Ndipo ine ndikufuna kunena kuti ndikuwutenga uwu ngati mwayi wopambana mmawa uno wa kudzakhhalanso pano. Ndipo ndikupepesa kuti ife tiribe malo okwanira okhalapo. Ndipo ife tiyesera, usikuuno, tsopano kuti tikhale ndi pemphero la odwala; lero, mmawa uno, izo zikhala zovutirapo pang’ono.

<sup>5</sup> Ndipo—ndipo ine ndinali woti ndijambula Uthenga uwu lero. Ine... Ambuye zimawoneka kuti amachita nane ine mokhudzana ndi izo, o, mwezi kapena iwiri yapitayo, ndipo iwo ndi wautali. Ndipo ine sindimakhala ndi nthawi uko mu misonkhano, chifukwa ife timailola iyo kuti izikhala misonkhano ya maminiti sate, forte. Ndiyeno ife... Chifukwa choti anthu amayenera kupita ku ntchito ndi zinthu, ine ndinawona kuti zizikhala bwino nditawapanga Mauthenga anga kukhala aafupi. Ndipo iwo analibe nthawi uko kuti ajambule iwo, kotero ine ndinaganiza ine ndingodikirira mpaka ine ndidzafike ku kachisi kuno ndiyeno nkudzajambula iwo kuchokera kuno. Ndipo iwo ndi wautali pang’ono,

ndipo ine ndikudziwa kuti inu mwaimirira, ndipo ine—ine ndifulumira mwaliwiro momwe ine ndingathere. Ndipo, tsopano, inu simundisokoneza ine ngati inu mungamasinthane pokhala, kapena chirichonsecho, zi—zimenezo zikhala zabwino mwangwiro ndi ine chifukwa ili ndi tsiku lapadera limene ife tikungopanga kujambula uku.

<sup>6</sup> Ndipo kotero ife talandira maripoti apamwamba kuchokera pa zimene Ambuye achita kunja uko, koma ife mwinamwake tinena zochuluka za izo usikuuno pamene ife tidzapereke nthawi yochuluka kwa izo, tidzakhala ndi nthawi yochuluka yoti tiipereke.

<sup>7</sup> Ndipo tsopano ife tikudalira kuti Ambuye adalitsa mmodzi aliyense wa inu. Ine ndikudziwa kuti mitima yanu yadzaza ndi chimwemwe, kuyembekezera Kudza kwa Ambuye. Wanganso, ukubwatamuka, poziwona zinthu zikuchitika mwanjira yomwe izo zikuchitikiramu. Ndi—ndi kumenyana kwa fuko, ndi mpingo mu chikhalidwe chimene iwo ulimo, ndi kuwona zizindikiro za Kudza Kwake, zonse ziwiri mwathupi ndi mwauzimu, ndi kuzindikira kuti nthawi ino ya Kuwonekera Kwake ili pafupi zedi, izo zimangodzazitsa mtima wathu ndi chisangalalo kuti ife tidzasinthidwa limodzi la masiku awa. Ife tidzasinthidwa kuchoka kwa zolengedwa izi zomwe ife tiri.

<sup>8</sup> Tsopano, ine ndikukhulupirira, ngati ine ndamvetsa, iwo ali ndi kulumikiza kwa lanya kwina kwake, kuti Uthenga uwu ukufika ku Phoenix ndi ku—ndi ku zigawo zosiyanasiyana, pa lanya. Ndipo kotero tsopano ife tikudalira kuti ngati izo ziri chomwecho. . . Ine sindikudziwa; basi ndimawuzidwa zimenezo ndisanabwere kuno. Ndipo—ndipo anthu onse kunja uko ndithudi akusangalala ndi thanzi labwino ndi—ndi Ulemerero wa Ambuye pa iwo.

<sup>9</sup> Ndipo tsopano—tsopano ife titsegula Mawu a Ambuye. Ndipo chimene ife tonse tadzera pano ndi kuti tidzasangalale ifeeni ndi kudzasamalitsa ku chimene ife tiri. . . Ife—ifesitimabwera nkomwe kuno ndipo ndife. . . Palibe yemwe ali pano sakudziwa kuti munthu aliyense sangakhale mu kutentha uku monga chonchi, ndipo basi pa chifukwa chakuti adzangokhala pano. Ife tiri pano kwa cholinga chimodzi, ndipo ndicho, “kuyenda pafupi ndi Mulungu.” Ndizo zonse zimene ife tingathe kuchita, ndi kukhulupirira kuti Ambuye Yesu ali ndi ife. Ndipo ife tiri pano kuti—kuti tiziyenda chifupi ndi Iye.

<sup>10</sup> Tsopano kutentha uku kukundipweteka pang’ono ine. Ine ndinakhala ngati ndinazolowera kutentha kowuma kuja uko mu Tucson, komwe kuli. . . Nkhungu kuno tsopano; kutentha kwathu kumeneko ndi kotentha kwambiri kuposa uku, koma iko ndi kowuma. Nkhungu yathu nthawizina imakhala wani pa twente wa wani peresenti, mwinamwake, chinachake monga choncho, basi pafupifupi ngati kukhala pansu pa hema ya mpweya. Koma kuno iko kumakhala ndi chi—chi—chinyontho

mwa iko, ndipo izo zimakupangitsa iwe kumamverera ngati “ukuwawuka,” monga ife tinkakonda kumadzitchulira izo. Kotero izo zimakhala zokuvuta iwe, kotero ine ndikudziwa zimenezo, ndipo amayi inu ndi ana onse ndi inu anthu omwe mwaimirira, achikulire ndi achichepere, ndipo mwaikidwa pamodzi monga inu mwachitiramo. Ndipo tsopano ife tiri—ife tikudalira kuti Mulungu akulipirani inu molemera chifukwa cha kudzipereka nsembe kwanuko.

<sup>11</sup> Ine ndamva kuti M’bale Roy Borders ali muno penapake. Ine ndinamva iye akulengezedwa, koma ine ndikuganiza mwinamwake iye walephera kuti alowe mkati. Chabwino. Ameneyo ndiye manenjala wa misonkhano.

<sup>12</sup> Kotero tsopano ife tikufunanso kuti tilengeze kuti mmodzi yemwe amakhala pakati pathu wapita kuti akakhale ndi Ambuye mmawa uno, bambo, M’bale Jackson wochokera ku Sturgis, Michigan. Palibe amene akudziwa momwe iye wapitira kapena momwe zachitikira. Iye anali bwino bwino basi, ndipo iye basi. . . ine ndikuganiza iwo angomupeza iye atafa, kapena chinachake. I—ine sindinapeze tsatanetsatane wake wa zimenezo. Ndipo ife tiri othokoza kwambiri kwa Mulungu kuti M’bale Jackson anali Mkhristu. Ine sindinamuwone iye kwa zaka zingapo, koma iye amakhala pakati pathu ndipo iye ndi mmodzi wa ife. Mulungu apumitse moyo wake wolimbawo! Kupita monga choncho, ife tikukhulupirira kuti mwinamwake izo zinali chinachake, kuti iyo inali nthawi yakuti iye azipita. Ambuye sanatichenjeze ife za izo, kapena iye za izo, iye wangopita. Umo ndi mmene izo zachitikira. Ndipo ine ndikufuna kuti ndidzawaimbire akazi awo mwamsanga mmene ine ndingadzathere, ndi kudzawauza iwo za chisoni chathu. Ndipo ife tonse tikufuna kupereka mathokoza kwa Mulungu chifukwa cha moyo wake wolimba wa Chikhristu, ndi chimene iye amathanthauza kuno pa dziko lapansi, ndipo makamaka kwa ife kuno mu gulu ili la osonkhana.

<sup>13</sup> Tsopano usikuuno, ine ndalengeza kuti pakhala pemphero la odwala usikuuno, ndipo ine ndidzalankhula mochuluka kwambiri pa za odwala usikuuno.

<sup>14</sup> Koma kwa nthawi ino, tiyeni tipite molunjika ku Mawu tsopano, chifukwa mwathinana ndiponso mukutentha. Ife tipita molunjika ku Mawu. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera ku magawo awiri a Lemba mmawa uno, aatali, ndi cholinga chakuti iwo andipatse ine maziko pang’ono a chimene ine ndikufuna kuti ndilankhulepo.

<sup>15</sup> Ndipo, tsopano, ine ndikukhumba kuti iwo aisunge tepiyo, M’bale Sothmann ndi iwo, asanaigulitse iyo, ngati kungatheke, ndipo ine—ine ndikufuna kuti ndidzamvetsere kwa iyo ife tisanati. . . iyo isanapite kwa anthu.

<sup>16</sup> Tsopano mu...ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera ku Afilipi, mutu wa 2, 1 mpaka 8; ndi Akorinto Wachiwiri 3, kuyambira ndi 6, ndipo kuwerenga mpaka mu mutu wa 4 wa Akorinto Wachiwiri, basi ngati maziko. Tsopano mu Afilipi, mutu wa 2, ine ndiwerenga poyamba.

Tisanawerenge, tiyeni tipemphere.

<sup>17</sup> Ambuye Yesu, Mawu Anu ali Choonadi. Ndipo mu ora lovuta ili limene ife tiri nkukhalamo, fuko kulimbana ndi fuko, zowawitsa, zivomezi mu malo ambiri, mitima ya anthu ikulephera, ndi mantha, ife tikuwona cholembedwa pakhoma. Tsopano, zimenezo ziri mu dera la chirengedwe, kuti dziko lonse liziwone izi. Koma tsopano liripo dera lauzimu, aponso, ndipo ife tikuwona zochitika zazikulu, ndipo ife tikufuna kuti tilankhule za izo lero.

<sup>18</sup> Muwadalitsire Mawu Anu ku mtima wathu. Ife tikudziwa kuti kulibe munthu Kumwamba kapena pa dziko lapansi ali woyenera kuti atenge Bukhu ili, kumasula Zisindikizo, kapena kuyang'anapo pa Ilo, nkomwe. Koma analipo Mmodzi amene anawonekera, Mwanawankhosa wophedwa, wamagazi, amene anabwera ndipo anadzatenga Bukhulo, ndipo anali woyenera ndi wokhoza kuti alitsegule Ilo. O Mwanawankhosa wa Mulungu, muwatsegulire Mawu Anu ku mitima yathu lero, kuti atitonthoze. Ife ndife antchito Anu. Mutikhulukire machimo athu, Ambuye. Ndi chirichonse chimene chingawalepheretse Mawu kuti azipita ndi mphamvu yaikulu ndi chikoka lero pa miyoyo yathu, muzichotsepo izo, Ambuye, cholepheretsa chirichonse, kuti ife tikakhoze kukhala nako kufikira kwathunthu ku madalitso onse amene analonjezedwera kwa ife kudzera mu Mawu Anu. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>19</sup> Afilipi 2.

*Ngati muli chitonthozo chirichonse mwa Khristu, ngati kumva bwino kulikonse kwa chikondi, ngati chiyanjano chirichonse cha Mzimu, ngati phamphu iliyonse ya chifundo,*

*Kwaniritsani inu chimwenwe changa, kuti inu mukhale amalingaliro ofanana, okhala ndi chikondi chomwecho, kukhala mu chigwirizano chimodzi, ndi—lingaliro limodzi.*

*Musalole chirichonse chichitidwe mokanganira kapena mwa ulemerero wopanda pake; koma mwa kudzichepetsa kwa malingaliro lolani aliyense amuyese mzake ngati womposa iyemwini.*

*Asayang'ane aliyense pa zinthu za iyemwini, koma munthu aliyense pa zinthu za ena.*

*Mulole lingaliro ili likhale mwa inu, limene linalinso mwa Khristu Yesu:*

*Amene, pokhala mmawonekedwe a Mulungu, sanachiyese cholanda kukhala wofanana ndi Mulungu:*

*Koma anadzipanga yekha kukhala wosatchuka, nadzitengera pa iye mawonekedwe a wantchito, ndipo anadzipanga kukhala mofanana ndi munthu:*

*Ndipo popezeka mmawonekedwe monga a munthu, iye anadzichepetsa yekha, ndipo anakhala womvera kwa imfa, ngakhale imfa ya pa mtanda.*

<sup>20</sup> Tsopano ngati ife tingatsegule tsopano ku Akorinto Wachiwiri, mutu wa 3, ife tiyamba ndi ndime ya 6, ndipo tiwerenga iyi mpaka ku ya 18, ndipo titsika mpaka ku gawo la mutu wa 4.

*Amenenso anatipanga ife kukhala atumiki okhoza a chipangano chatsopano; osati a lemba, koma a mzimu: pakuti lemba limapha, koma mzimu umapatsa moyo.*

*Koma ngati utumiki wa imfa, wolembedwa ndi kuzokotedwa pa miyala, unali wa ulemerero, kotero kuti ana a Israeli sakanatha mokhazikika kuyang'anitsitsa nkhope ya Mose chifukwa cha ulemerero wa nkhope yake; ulemerero umene unali woti udzatha:*

*Ulekeranji utumiki wa mzimu kukhala wa ulemerero koposa?*

*Pakuti ngati utumiki wa chitsutso unali wa ulemerero, kochulukanso ndi momwe utumiki wa chilungamo kuti upambana mu ulemerero.*

*Pakuti ngakhale icho chimene chinapangidwa kukhala cha ulemerero chinalibe ulemerero pamenepa, pa zifukwa za ulemerero umene uli wopambana.*

*Pakuti ngati icho chimene chinadzatha chinali ulemerero, mopitirira kwambiri chiri...chotsaliracho chiri ulemerero.*

*Powona ndiye kuti tiri ndi chiyembekezo chotere, ife tiyenera kwakukulu...mmalankhulidwe ophweka, tizigwiritsa ntchito malankhulidwe ophweka kwambiri.*

*Ndipo simonga Mose, amene anaika chophimba pa nkhope yake, kuti ana a Israeli asayang'anitsitse mpaka kutha kwake kwa icho chimene chinathetsedwa:*

*Koma malingaliro awo anachititsidwa khungu: pakuti mpaka lero chophimba chomwecho chikadalipo chosachotsedwa mkuwerenga kwa chipangano chakale; chophimba chake chomwe chinachotsedwa mwa Khristu.*

*Koma ngakhale mpaka lero, pamene Mose awerengedwa, chophimba chiri pa mitima yawo.*

*Komabe pamene atembenuzidwira kwa Ambuye, chophimba chidzachotsedwapo.*

*Tsopano Ambuye ndiye Mzimu umenewo: ndipo komwe Mzimu wa Ambuye . . . kumeneko kuli ufulu.*

*Koma ife tonse, ndi nkhope zowonekera tikuyang'ana ngati mu kalilole ulemerero wa Ambuye, kusintha kumka ku chifanizo chomwecho kuchokera ku ulemerero kumka ku ulemerero, ngakhale monga mwa Mzimu wa Ambuye.*

*Chifukwa chake popeza tiri nawo utumiki uwu, monga ife talandira chifundo, ife sitifooka ayi;*

*Koma takaniza zinthu zobisika ndi zamanyazi, osayendayenda mochenjera ndi kuchita nawo mawu a Mulungu mwachinyengo; koma ndi mawonetseredwe a choonadi kudziweruza tokha ku chikumbumtima cha anthu onse pamaso pa Mulungu.*

*Koma ngatinso uthenga wathu ubisika, ubisika kwa iwo amene ali otayika:*

<sup>21</sup> Ambuye atawonjezera madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu Ake!

<sup>22</sup> Tsopano, phunziro langa mmawa uno, ine ndikudalira kuti Mulungu awulula izi. Ndipo nthawi iliyonse, ngati inu amene mumatenga matepi ndi kumakawamvetsera, ndipo ine ndikuyembekeza ndi kudalira kuti—kuti inu mwakhala muli nako kumvetsa kwauzimu kwa chimene Mulungu ameneyo wakhala akuyesetsa kuti abweretse ku Mpingo mopanda kuchinena icho mwachindunji. Mukuona? Ndi chinthu, nthawizina, ife timayenera kuti tinene zinthu mwanjira yakuti izo zikhoze kuchepetsa, zikhoze kupangitsa kuti ena atulukepo, ena achokepo, ndi ena kuti—kuti—kuti azisinkhasinkha. Koma zimenezo zimachitidwa ndi cholinga. Izo zimayenera kuchitidwa mwanjira imeneyo.

<sup>23</sup> Ndiye izo zikhoza kukhala kuti ena akhoza kunena kuti, “Inu mukutanthauza kuti Mulungu angachite chinthu ndi cholinga monga choncho?” Iye ndithudi anatero. Iye akadachitabe.

<sup>24</sup> Iye ananena tsiku lina, pamene Iye anali nawo zikwi atamuzungulira Iye, Iye anati, “Kupatula inu mutadya Thupi la Mwana wa Mulungu, kapena Mwana wa munthu, ndi kumwa Magazi Ake, inu mulibe Moyo mwa inu.”

<sup>25</sup> Inu mukuganiza kuti ndi neno la mtundu wanji limenelo kuti dokotala wa zamankhwala kapena namwino, kapena munthu aliyense wabwino waluntha angaganize za neno ngati limenelo, kwa Munthu yemwe anali ndi utumiki wonga umene Iye anali

nawo? Bwanji, iye amakhoza kunena kuti, “Mudye thupili? Ameneyo ndi wodya amzake! Kuti azimwa magazi a munthu? Ameneyo ndi mthakati! Mwakulankhula kwina, Iye akufuna kuti ife tikhale ody a mzathu komanso athakati.” Ndipo gulu lonse lo linamuchokera Iye.

<sup>26</sup> Ndipo apo panali gulu la azitumiki ndi Iye, la sevente, amene anali atasankhidwa. Ndipo Iye anapotolokera kwa iwo, ndipo Iye anati, “Kodi inu mudzaganiza chiani pamene muti mudzamuwone Mwana wa munthu akukwera kupita kumene Iye anachokerako?” Tsopano, Iye sanafotokoze zimenezo. Iye sanafotokoze konse kuti zidzakhala *motani*; Paulo anadzachita zimenezo mtsogolo mwake. Iye anangonena Izo. Mukuona? Ndiyeno pamene izi, Iye anati, “Kodi inu mudzanena chiyani,” kwa atumiki awa, “pamene inu mudzamuwone Mwana wa munthu akukwera kumwamba kumene Iye anachokerako?”

<sup>27</sup> Sindikukaika anthu amenewo anati, “Tsopano, mphindi chabe. O, ife timadya naye Iye. Ife timawedza naye Iye. Ife timagona naye Iye. Ife—ife tikudziwa kumene Iye anabadwira. Ife tinawona chikuta chimene Iye—Iye analedweramo. Ndipo zingatheke bwanji kuti Munthu uyu... Awa ndi maneno olimba.”

<sup>28</sup> Ndipo Baibulo linati, “Iwo sanayende nayenso Iye.” Iwo anamuchokera Iye.

<sup>29</sup> Ndiye Iye anatsala ndi khumi ndi awiri. Iye anali atasankha khumi ndi awiri, ndipo mmodzi wa iwo anali mdierekezi, Iye anatero. Kotero Iye anatembenukira kwa iwo.

Ndipo panalibe aliyense amene akanafotokoza zimene Iye anali atangonena. “Momwe iwo ati adzadyere Thupi Lake ndi kumwa Magazi Ake? Ndi kuti zinachitika motani kuti Iye anachita kutsika, pamene Iye anabadwira ku dziko lapansi komwe kuno?” Mukuona? Iwo samatha kumvetsa Izo.

Ndiyeno Iye anapotolokera kwa atumwiwo, ndipo Iye anati, “Kodi inunso mukufuna kuti muzipita?”

<sup>30</sup> Ndipo ndi pamene Petro Mtumwi ananena neno lopambana lija, “Ambuye, ife tingapitenso kwa ndani?” Mukuona? “Pakuti ife takhutitsidwa. Ife tikudziwa ndithudi kuti Inu, ndipo Inu nokha, muli nawo Mawu a Moyo a ora lino.” Mukuona? “Ndipo ife takhutitsidwa ndi zimenezo.” Mwaona, iwo samatha kuzifotokoza Izo. Iwo. . .

Inu simungathe kuchifotokoza chikhulupiriro. Icho ndi chinachake chimene iwe umakhulupirira, ndipo icho chimakhala chokhazikika mwakuti palibe china chirichonse chimene chingatenge malo ake.

Choncho, iwo ankadziwa kuti Mawu amene analembedwera m’badwo umenewo umene iwo anali nkukhalamo, m’badwo wa Umesiya, kuti Iye amakwanira malo amenewo ndendende.

Ndipo iwo akadachita chiyani kuti abwererensho ku matchalitchi ozizira, ofunda awo amene iwo anali atachokamo? Anati, “Kodi ife tipitanso kuti?” Mukuona? “Ife tiri okakamizidwa kwathunthu kuti Inu muli nawo Mawu a Moyo.” Mukuona? Ndipo iwo—iwo sanathe kuzifotokoza Izo, koma iwo anakhulupirira Izo. Mukuona?

<sup>31</sup> Ndipo Yesu ananena zimenezo kuti achepetse gulu Lake, mwaona, kufikira Iye atalibweretsa gulu lakelo pamodzi. Ndipo kuchokera mwa anthu amenewo, iwo, khumi ndi mmodzi okha a iwo pamenepo anamvetsa kwenikweni Yemwe Iye anali. Iwo anadziwa kuti Iye anali Mulungu, ndipo Mulungu yekha. Tsopano, a. . .

<sup>32</sup> Phunziro langa mmawa uno ndiro kumuwulula, kapena, kumuvundukula Mulungu ameneyo.

<sup>33</sup> Mulungu wakhala nthawizonse, mu m’badwo uliwonse, wakhala akubisala kuseri kwa chophimba, mibadwo yonse, koma Iye wakhala ali Mulungu nthawi zonsezo. Mukuona? Koma Iye wakhala akuziika Yekha wobisika kwa dziko lapansi, ndi kumadziulula Yekha kwa Osankhidwa Ake, monga atumwi tsiku lijalo. Tsopano, ameneyo anali Mulungu akulankhula mwa Khristu.

<sup>34</sup> Tsopano, munthu nthawizonse, chakhala chiri chikhaliidwe cha munthu, iye wakhala akufunafuna atamuwona (mwathupi) Mulungu ameneyo. Iye nthawizonse wakhala akufuna atamuwona Iye. Munthu wakhala akupanga zolengedwa zowaneka ngati Iye. Iwo amaganiza za. . . Amwenye amapembedza dzuwa. Ndipo—ndipo ife tikupeza, mu Afrika, mawonekedwe osiyanasiyana a zinyama, ndi zina zotero. Ndipo mpaka. . . zosemedwa mu Alaska, ndi—ndi mawonekedwe osiyanasiyana amene iwo amaganizira kuti Mulungu uyu ali mwa izo. Monga Paulo analankhulira uko ku Atene nthawi ijayi, pa phiri la Mars, ndipo anawauza iwo kuti iwo anali akupembedzetsa mu zinthu za Mulungu wosadziwika uyu, kuti, iwo ankadziwa kuti Iye analipo komabe iwo samamudziwa Iye.

<sup>35</sup> Ndipo kotero ife tikupeza ngakhale mmbuyo mpaka kwa Yobu. Yobu ankadziwa kuti kunali Mulungu. Iye ankadziwa zimenezo. Ndipo palibepo mu—mu—munthu, woganiza bwino, koma yemwe amadziwa kuti kuyenera kuti kuli Chinachake kwinakwake. Ndipo, tsopano, Yobu ankafuna kulankhula naye Iye.

Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzindikire mawonekedwe amene Mulungu anasankha kuti alankhule naye Yobu. Mulungu anali ataphimbidwa pamene Iye ankalankhula ndi Yobu. Iye anaphimbidwa mu kamvulumvulu, anabwera mu kamvulumvulu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akumabwerabe mu kamvulumvulu akhoza kubwera pamene inu muli chipenyere? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]



<sup>36</sup> Alipo ambiri amene akhala pano, angapo, amene anali ndi ife tsiku lina lija pamene Iye anabwera mu kamvulumvulu. Anatiuza ife cha dzana lake, M'bale Banks Wood ndi iwo, pamene Iye anati, "Tola mwala uwu, uwu ponyere iwo mmwamba, ndipo unene kuti, 'PAKUTI ATERO AMBUYE! Iwe uziwona izo pomwepo.'" Ndipo ine ndinatola mwalawo, uko pamwamba pa phirilo, ndinawuonyera iwo mmwamba, ndipo. . . inde, ukutsika pansu, iwo unayambitsa kamvulumvulu, mwaona, kuvundula kwake.

<sup>37</sup> Iwe umayenera kuti uchite chinachake choti chipangitse chinachake kuti chitsatire izo. Yesu anatenga chidutswa cha mkate ndipo anaunyema iwo, kenako anawuchulukitsa kuchokera pa chidutswa icho cha mkate. Iye anatenga madzi, anawatsanulira iwo mu mtsuko. Eliya anatenga mchere, anawuika iwo mu supa; anadula ndodo, anaiponyera iyo mmadzi. Ndi chinachake choti chiphiphiritse.

Ndipo ndinatola mwala uwu ndipo ndinawuonyera iwo mmwamba, ndipo ukutsika pansu zinayambitsa kamvulumvulu.

<sup>38</sup> Tsiku lotsatira, bwanji, kunali mtumiki limodzi nafe pa ulendo wokusaka. Iye anali kuima pafupi, ndipo iye ananena kwa ine, "Kodi Ambuye akumaperekabe masomphenya monga chonchi, M'bale Branham?"

<sup>39</sup> Ine ndinati, "Inde, koma ine kawirikawiri ndimabwera kuno kuti ndidzapume." Ndipo basi pomwepo masomphenya anabwera.

<sup>40</sup> Ndipo M'bale Borders, ine ndikuganiza iye ali panja tsopano, iye tinali naye limodzi. M'bale Banks Wood, ine ndikuganiza, ndi, o, angapo anali kumtunda kumeneko, eyiti kapena teni. Ndipo M'bale Banks Wood amapenyera izi. Pa phiripo, basi kuchokera, ndendende, pafupi theka limodzi la mailosi kumene Angelo asanu ndi awiri anawonekera, chimene ine ndinachokera kuno ndi kupita kumeneko, ndikubwerera ndi kudzanena. . . zokhudza Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Pafupi theka la mailosi kuchokera kumeneko.

<sup>41</sup> Ndiyeno tsiku lotsatiralo, pamene izi zinali kuchitika, bwanji, a. . . ine ndinanena kwa m'bale, m'bale uyu, ine ndinati, "Vuto lako ndi chiyani, iwe uli ndi chokuvutitsa mu diso lako. Madokotala ayesetsa kwa zaka zingapo kuti achiletse icho ndipo iwo akulephera kuti atero. Iwo amanena kuti. . . icho chidya diso lako." Ndipo ine ndinati, "Koma usadandaule, Ambuye Yesu alemekeza chikhulupiro chako." Ndipo iye anangogwetsa mfuti yake. Ndipo ine ndinati, "amayi ako," ndi chimene iwo anali ndipo ndi vuto limene anali nalo.

Ndipo iye anati, "Izo ndi zoonu."

<sup>42</sup> M'bale Roy Roberson wochokera pa mpingo pano, ataima pamene, ine ndikuganiza nonse a inu mukumudziwa iye. Podziwa kuti iye anali wankhondo wakale, ndipo podziwa

zimene zinali zoti zichitike, ine ndinaika dzanja langa pa phewa lake; ine ndinati, “M’bale Roberson, musamalitse, mupenyetsetse, chinachake chikukonzekera kuti chichitike.”

<sup>43</sup> Ine ndinabwerera mmbuyo kupita kumene ine ndimayenera kuti ndiime, ndipo kuchokera mu mlengalenga munabwera kamvulumvulu, akutsika kudutsa ka mpita, kuchokera pamwamba, ameneyo anali wamphamvu kwambiri mpaka iye anang’amba miyala, kupyozza ma inchesi asanu ndi atatu kapena khumi, kuchokera pamwamba pa phiri, ndi kukaiponyera iyo mayadi mazana awiri mkati. Ndi kuwomba katatu monga choncho, ndipo Liwu linabwera kuchokera mmenemo. Mukuona?

<sup>44</sup> Ndipo onse anali ataima pamenepo. M’bale Banks, ali pompano, anabwerapo ndipo anati, “Zimenezo ndi zimene inu munandiuzza ine dzulo?”

Ine ndinati, “Inde, bwana, ndi zimenezo.”

Iye anati, “Tsopano, kodi Izo zanena chiyani?”

<sup>45</sup> Ine ndinati, “Tsopano, zimenezo ndi zakuti ine ndidziwe ine ndekha, M’bale Banks, mwaona, chifukwa izo zinali. . . Izo zikanawawopsyeza anthu.”

<sup>46</sup> Koma Izo zinapitirira, izo zinakachitika pang’ono chabe. . . kuyenda kupita chakumpoto. Pang’ono, masiku pang’ono kenako Izo zinakagunda mu nyanja, ndipo inu munawona zimene zinachitika cha ku Fairbanks. Icho chinali chizindikiro cha chiweruzo. Tsopano ife tikupeza kuti—kuti Mulungu panobe. . . Inu mukuona, izo zikanawaponyera anthu kuti achite mantha. Ndipo kotero ndiye iwo anali. . . Izo zinkayenera kuti zichitike, mwaona. Izo ziyenera kuti zichitike basi. Zinthu zimene ziyenera kuti zichitike ziyenera kuchitika, mulimonse. Mwaona, izo zichitika, mulimonse.

<sup>47</sup> Mose nthawi ina ankafuna kuti amuwone Mulungu, ndipo Mulungu anamuwuzza iye kuti akaima pa thanthwe. Ndipo, pa thanthwe, Mose anakaimapo ndipo iye anamuwona Mulungu akudutsa, ndipo nsana Wake unawoneka ngati nsana wa munthu. Mulungu anali mu kamvulumvulu, ndipo Mulungu. . . pamene Mose anali ataima pa thanthwe.

<sup>48</sup> Ine ndikuganiza inu nonse munachiwona chithunzicho kunja uko tsiku lina, ife tinaima pafupi ndi thanthwe lomwelo. Ndipo Kuwala kuja ndi uku, Mngelo wa Ambuye, pomwe apo pamene Iko kunawomba. Nditaima. . . Izo ziri pomwe apo pa bolodi lolengezera tsopano, kenanso.

<sup>49</sup> Zindikirani, Yehova wa Chipangano Chakale ndi Yesu wa Chipangano Chatsopano. Mukuona? Iye ali Mulungu yemweyo, amangosintha mawonekedwe Ake.

<sup>50</sup> Tsopano, winawake ananena tsiku lina, m—m—mtumiki wa Baptisti uko mu Tucson, “Inu munganene bwanji kuti—kuti Yesu ndi Mulungu angakhale Munthu mmodzi yemweyo?”

<sup>51</sup> Ine ndinati, “Chabwino, ndi zophweka kwambiri ngati inu mutangololeza kuganiza kwanu kuchokepo, ndi kumaganiza mwa Baibulo za izo. Iwo ndi Chinthu chomwe chomwecho. Mulungu ndi Mzimu; Yesu ndi thupi limene Iye anaphimbidwiramo. Mukuona?” Ine ndinati, “Monga m’banja langa. Kwa mkazi wanga, ndine mwamuna wake. Ndipo ine ndiri ndi mwana wa mkazi wamng’ono, Rebekah, ndine bambo wake. Ndipo ine ndiri ndi mdzukululu wa mwamuna, ndipo dzina lake ndi Paul, ndine agogo ake aamuna. Ndine mwamuna wapabanja, bambo, ndi agogo aamuna. Ndipo mkazi wanga sangakhale ndi chodzinenera pa ine ngati bambo kapena agogo aamuna; iye ali ndi chodzinenera chokha pa ine ngati mwamuna wake. Ndipo mwana wanga wamkazi alibe chodzinenera pa ine ngati mwamuna wake kapena agogo aamuna; iyeyo ndi mwana wanga. Mukuona? Komabe anthu atatu onse awa ndi munthu yemwe yemweyo. Mukuona? Ameneyo ndi Mulungu; Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, izo ndi zodzinenera chabe za kam’badwo.” Mulungu ndi yemweyo, Mulungu yemwe yemweyo.

<sup>52</sup> Mulungu anadzisintha Yekha, amasintha mawonekedwe Ake. Ngati inu mungazindikire apa mu Afillipi, Iye anati, “Sanachiyese icho cholanda, koma anatenga *mawonekedwe* a munthu.”

<sup>53</sup> Tsopano, mawu a Chigriki pamenepo a *mawonekedwe* amenewo, ine ndakhala ndikuyang’ana pa iwo tsiku lonse dzulo, kuyesera kuti ndiganizire chomwe iwo anali, ine ndapeza, ndinabwerapo ndi mawu awa akuti “en morphe.” Iwo amalembedwa e-n m-o-r-p-h-e. Ndikuyang’ana mu Chigriki, kuti ndipeze chimene en morphe ali. . . Ine ndikhoza kuwatchula iwo molakwika, koma chifukwa chimene ine ndatchulira kalembedwe kake, ndikuti pamene tepiyo iti idzatulutsidwe, anthuwo adza, ophunzira adza, adzadziwe chimene ine—ine ndikutanthauza ponena izi. Iye, pamene en morphe, izo zikutanthauza kuti Iye anadzisintha Yekha. Iye, Iye anabwera kuno. Tsopano, mawu a Chigriki pamenepo amatanthauza, kuti, “Chinachake chimene sichikadawoneka, komabe chiri pamenepo, ndiyeno icho chasinthidwa ndipo diso likutha kuchiwona icho.” Mukuona?

<sup>54</sup> Monga Eliya anali, ku Dotani. Mwaona, wa—wantchitoyo samatha kuwawona Angelo onse awo anali kumeneko, ndipo Mulungu anangosintha; sikuti anawatsitsira Angelowo pansu, koma Iye anasintha mawonedwe a wantchitoyo. Ndipo pamenepo panali mapiri atadzadza ndi Angelo, ndi moto, ndi akavalo a moto, ndi magaleti a moto, zonse zitamuzungulira mneneri Wake. Mwaona, iwo, Iye anasintha mawonedwewo. Chi—chinthucho chinali kale pamenepo.

<sup>55</sup> Kotero, ndi chimene ine ndikuyesera kuti ndinene, kuti Mulungu ameneyo yemwe nthawizonse anali ali kuno. Chinthu chokhacho chimene Iye anachita pamene Iye anadzakhala munthu, Iye anasintha chigoba Chake. Mukuona? Iye—Iye, en morphe uyu, Iye—Iye anadzisintha Yekha kukakhala chimene Iye anali kupita ku chimene Iye ali, kapena chigoba Chake, kuchita kwina.

<sup>56</sup> Monga mu seweru lalikulu. Monga ine ndimalankhulira mmawawu, ndimakhala ngati ndimatenga izi za Shakespeare. Izo zakhala ziri nthawi yaitali. Koma pamene Shakespeare ankalemba se—se—sewerolo, ku... kumulembera King James waku England, pamene iye... khalidwe la Macbeth. Mwaona, Shakespeare sankakhulupirira mu za ufiti; koma mu sewerolo, chifukwa mfumuyo inkakhulupirira mu za ufiti, kotero iye anayenera kuwonjezera afiti. Mukuona? Ndipo tsopano, pofuna kuti achite izi, iwo amasintha chigoba.

<sup>57</sup> Becky apa, mu *Carmen*, iwo anachita seweru limenelo ku—ku sukulu kumene iye wangotsiriza kumene masabata pang’ono apitawo. Tsopano, mwinamwake munthu mmodzi amasewera magawo atatu kapena anai. Pofuna kuti achite zimenezo, iye—iye amasintha chigoba chake. Nthawizina iye amatulukira, iye amakhala munthu *uyu*; ndipo nthawi inayo iye akamatulukira, iye amakhala munthu wina. Koma ndi munthu yemwe yemweyo nthawi zonse.

<sup>58</sup> Ndipo ameneyo ndi Mulungu. Iye anadzisintha Yekha kuchokera—kuchokera ku Lawi la Moto, kudzakhala Munthu. Kenako anadzisintha Yekha kuchokera ku chimenecho, anabwereranso mu Mzimu kachiwiri, kuti Iye adzathe kudzakhala mwa munthu. Mulungu kuchita seweru mwa munthu chimene Iye anali kwenikweni. Yesu Khristu, anali Mulungu akuchita seweru mwa Munthu, mwa Munthu. Mwa Munthu, ndicho chimene Iye anali. Iye anali atasintha kuchokera ku Lawi la Moto, ndipo kenako anali atabweramo; chimene chinali chopimba mu chipululu, chimene chinali kumubisa Mulungu kwa Israeli. Mose anawona mawonekedwe a thupi Lake, koma kwenikweni Iye anali akubisala nthawi zonsezo kuseri kwa Lawi la Moto ili, limene linali Logos limene linapita kuchokera kwa Mulungu.

<sup>59</sup> Tsopano ife tikupeza apa, tsopano chichitikireni Pentekoste, Mulungu sakuchita seweru *mwa* munthu, kapena kuchita... tsopano Iye akuchita seweru *kudzera* mwa munthu. Mukuona? Iye anali akuchita seweru *mwa* Munthu nthawi imeneyo, Yesu. Tsopano Iye akuchita seweru *kudzera* mwa munthu yemwe Iye wamusankha kwa cholinga ichi. Mulungu, mmawonekedwe a munthu, Iye anadzisintha Yekha kuchoka ku mawonekedwe a— a . . . a Mulungu, kupita ku mawonekedwe a munthu.

<sup>60</sup> Iye anabwera mmaina atatu, maina a ana atatu. Iye anabwera mwa Mwana...dzina la Mwana wa—wa munthu, Mwana wa Davide, ndi Mwana wa Mulungu; maina a ana atatu.

<sup>61</sup> Tsopano, Iye anabwera koyamba mwa Mwana wa Da... Mwana wa munthu, chifukwa Iye anali Mneneri. Tsopano, Yehova Mwiniwake ankamutcha Ezekiele ndi aneneri, “mwana wa munthu, ukuwona chiyani iwe?” Yesu sanadzitchule Yekha ngati Mwana wa Mulungu; Iye anadzitchula Yekha ngati Mwana wa munthu, chifukwa m—Malemba sangathe kuswedwa.

Palibe chirichonse chingathe kusweka mu Malemba. Mawu aliwonse ayenera kukhala chomwecho. Umo ndi momwe ine ndimakhulupirira izo. Umo ndi momwe Iwo ayenera kukhalira, sikuti chifukwa ine ndikuzikhulupirira izo, chifukwa Izo ndi Mawu a Mulungu.

<sup>62</sup> Tsopano ngati inu mungazindikire pachiyambi, Mawu amodzi, tsamba loyamba mu Baibulo, mu Genesis 1, ife tikupeza kuti lonselo...Matenda onse, chisoni chonse, kupweteka kwa mtima konse, ndi chirichonse chimene chinayamba chachitikapo kwa anthu, zinabwerapo chifukwa munthu *mmodzi* sanawakhulupirire Mawu *amodzi*, zinapangitsa zonsezi. Kumeneko ndiye koyambirira kwa Baibulo. Kotsirizira kwa Baibulo, Chivumbulutsa 22, Mulungu yemweyo anati, “Aliyense amene adzachotsere Mawu amodzi kuchokera Umu, kapena adzawonjezere mawu amodzi kwa Ilo.” Mwaona, iwo ayenera kukhala Mawu pa Mawu, basi momwe Ilo lirili.

<sup>63</sup> Kotero, choncho, ndipo tingotenga kanthu kakang’ono ngati kuti ine...winawake nthawizonse amabwera kwa ine pa zokhudza akazi kudula tsitsi lawo. Tsopano, kwa ine, ngati iye akuchita zimenezo, ine ndiribe nazo ntchito kaya iyeyo akuchita moyera chotani ndipo iye akudziwa mochuluka bwanji, iye akulakwitsabe. Iye akumavala makabudula ndi zovala izi monga choncho; ine sindikusamala kuti iye akuchita chiyani, amaimba mochuluka bwanji, amatha kulalikira bwino bwanji, chirichonse chimene iye amatha kuchita, ndi moyo wa mtundu wanji umene iye akukhala, Mawu amodzi amenewo aswedwabe. Mukuona? Mwaona, izo ziyenera kukhala Mawu onse. Osati chiganizo; Mawu, Mawu amodzi! Kotero, Baibulo liribe kutanthauzira kwa mseri. Ilo liyenera kukhala Mawu pa Mawu, momwe Ilo linalembedwera. Ife tiyenera kuwakhulupirira Iwo.

<sup>64</sup> Ndipo osati kungowakhulupirira Iwo, koma kuwakhala moyo Iwo. Ngati ife sitimawakhala moyo Iwo, ndiye kuti ife sitikuwakhulupirira Iwo; ife timangonena kuti ife timatero. Monga ine...Pokhazikika mmbuyo pa zimene ine ndinanena, ophunzira awo samatha kuwafotokoza Iwo, koma iwo amawakhulupirira Iwo, mulimonse, ndipo iwo amapanga chivomerezo chawo ndipo amakhala moyo wa icho. Pamene ena onse a iwo anachokapo kwa Iwo, iwo anakhala nawo Iwo! Iwo ankawakhulupirira Iwo! Umo ndi mmene ife timachitira.

Umo ndi mmene inu muyenera kumachitira izo. Ziribe kanthu zimene wina aliyense akuchita, ife timawakhulupirira Iwo ndipo tikatero ife timachitapo pa Iwo. Ngati inu simukuchita izo, ndiye kuti inu simukuwakhulupirira Iwo.

<sup>65</sup> Tsopano zindikirani tsopano pamene Iye ankabwera, Iye ankayenera kubwera ngati Mwana wa munthu, chifukwa Lemba Loyera limanena kuti Iye akanadzatero, “Mulungu adzadzutsa Mneneri kwa iwo.” Koteru Iye sakanabwera ndi kumadzitcha Yekha Mwana wa Mulungu, chifukwa kanyengo kake sikanali kameneko. Iye anali Mwana wa munthu akulosea, kuti adzakwaniritse, ndi kudzawulula kwa iwo zinthu zonse zimene zinali zitachitidwa, ndi kufanizira zimene Iye anali. Ndiye Iye anali pa dziko lapansi ngati Mwana wa munthu.

<sup>66</sup> Tayang’anani pa mkazi wachi Surofonisia uja anathamangira kwa Iye, ndipo anati, “Inu Mwana wa Davide, ndichitireni ine chifundo!” Iye sanadzutse nkomwe mutu Wake. Iye analibe zodzinenera pa Iye ngati Mwana wa Davide. Iye anali wa Amitundu.

Chimodzimodzinsu palibe mwana wamkazi wanga angakhale ndi zodzinenera pa ine ngati mwamuna wake; kapena, mkazi wanga, ngati mwana wamkazi. Komabe, iye ndi mwana wanga wamkazi ndi mkazi wanga, iye ndi mwana wanga wamkazi mu Uthenga. Koma, padziko lapansi lino, iye alibe ufulu wonditcha ine b—bambo. Mukuona?

Tsopano zindikirani, mkazi wa Amitundu uyu analibe zodzinenera pa Iye ngati Mwana wa Davide. Koma Bartimeyo wakhungu anatero, mwaona, iye anali Myuda. Tsopano, Iye anabwera ngati Mwana wa munthu.

<sup>67</sup> Iwe umayenera kuwadziwa mawu awa ndi zinthu izi. Tamuwonani Hattie Wright nthawi ijayi, pamene Chikoka Chachitatu. Inu mukukumbukira izo. Mwa zonsezo, mkazi ameneyo ananena chinthu cholondola. Iwe umayenera kunena mawu olondola awo, chinthu cholondola kwa Mulungu.

<sup>68</sup> Zindikirani tsopano, Iye anabwera poyamba ngati Mneneri, ndipo iwo anamupachika Iye. Ake Omwe anamupachika Iye. Iye anabwera ngati Mwana wa munthu.

<sup>69</sup> Kenako Mzimu Woyera utatha kubwera, Iye anali pamenepo Mwana wa Mulungu. Mulungu ndi Mzimu. Iye anali Mzimu Woyera, Mwana wa Mulungu. Iye amakhala kudutsa mibadwo ya mpingo ngati Mwana wa Mulungu.

<sup>70</sup> Tsopano, mu Zakachikwi, Iye adzakakhala Mwana wa Davide, akukhala pa Mpandowachifumu wa atate Ake, Davide. Iye ndi Mwana wa Davide, tsopano.

<sup>71</sup> Ndipo, kumbukirani, pakati pa Mwana wa Mulungu . . . Mu m’badwo wa mpingo wa Laodikaya, iwo anamuika Iye panja. Ndiye mu Luka, Iye anati Iye adzaulidwanso ngati Mwana

wa munthu, Mneneri, kukwaniritsa zonse za izo. Mukuona? Malemba amamangirira pamodzi mwangwiro. Mwana wa munthu, Mwana wa Mulungu, Mwana wa Davide. Zinali chiyani izo? Ndi Mulungu yemwe yemweyo nthawizonse, kumangosintha mawonekedwe Ake basi, en morphe. Iye amangosintha iwo. Ilo ndi sewero lalikulu kwa Iye. Iye akuchita sewerolo.

<sup>72</sup> Iye anabwera ngati Mwana wa munthu, Mneneri. Anadzachita ndendende. Ngakhale mkazi wamng'ono uja mu tchimo lake lonse, kuja pa chitsime, iye anamuzindikira Iye. Iye anati, "Ife tikudziwa kuti Mesiya akubwera, amene akutchedwa Khristu, ndicho chimene Iye ati adzachite." Mwaona, iye anazindikira chifukwa iye anali Mbewu yokonzedweratu. Ndiye iye. . .

Pamene, ena onse a iwo sanazindikire Izo. Iwo analibe choti azindikire nacho. Iwo anali mu tchimo, kuyamba ndi kuyamba.

<sup>73</sup> Kuti, kuti achite Zakezo, Iye amasintha mawonekedwe Ake. Kenako Iye anadzakhala mawonekedwe a Mwana wa munthu.

Kwa m'badwo wa okonzanso, Wesley, Luther, ndi onse kudutsa, kenako ife tikupeza kuti iwo anangozimanga izo mtolo, chimodzimidzi basi monga a Israeli anachitira, mpaka kuti pamene Iye akudzawonekera mu masiku otsiriza, mu m'badwo wa pentekoste, ngati Mzimu Woyera, iwo anawukana Iwo. Iwo anachita chinthu chomwecho chimene Israeli anachita.

Ndipo kodi Iye akuchita chiyani tsopano? Akubwerera ngati Mwana wa munthu. Ndiyeno, kuchokera pamenepo, Mwana wa Davide. Mukuona momwe ife tayandikirira? Mwana wa munthu, Mwana wa Davide, Mwana wa Mulungu. Iye akuwululidwa mu masiku otsiriza ngati Mwana wa munthu, molingana ndi Malaki 4, mauneneri ena onse ogwirizana ndi ora lino. Sakuchitanso ndi mpingo zitachitika kuti Iye. . . Iwo anamutulutsa Iye panja; ali kunja, akugogoda pa khomo. Muli Mbewu ina yokonzedweratu mmenemo, apobe. Iye ayenera kuti afikire kwa iwo.

<sup>74</sup> Ndipo Mulungu, mwa munthu, anali atadzikhuthula Yekha. Yoweli 2:28, ife tikupeza, Iye anati, "Ine ndidzatsanulira, mmasiku otsiriza, Mzimu Wanga." Tsopano, ngati inu mungazindikire mawu pamenepo, mawu Achigriki. Ine ndikhoza kulakwitsa apa, koma amodzi amene ine ndinawapeza. . .

<sup>75</sup> Inu muyenera kuwapenyetsetsa mawuwo. Chingerezi nthawizina chimatanthauza matanthauzo apawiri. Chimodzimidzi ndi mawu amene ife timati, "mulungu." Mulungu analenga miyamba ndi dziko lapansi, Genesis 1. Koma tsopano, mu Baibulo, Ilo limati, "Pachiyambi Elohim." Tsopano, Elohim, Chingerezi chimati "mulungu," koma izo kwenikweni sizinali *Elohim*. . . Chirichonse chikhoza kukhala mulungu, kwa mawu akuti *mulungu*; inu mukhoza kupanga mulungu wa

fano; inu mukhoza kulipanga limba ilo mulungu; inu mukhoza kuchipanga chirichonse mulungu.

<sup>76</sup> Koma izo siziri chomwecho mu mawu akuti *Elohim*; Iwo amatanthauza, “Iye wokhalapo-yekha.” Mukuona? Limba limenelo silingakhalepo lokha, palibe kanthu kalikonse kangakhale kokhalapo-kokha. Kotero, mawu akuti *Elohim*, amatanthauza, “Iye amene nthawizonse amakhalapo.” *Mulungu* chikhoza kutanthauza chirichonse. Mukuona kusiyana kwake mu mawu? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>77</sup> Tsopano, pamene Ilo linanena apa kuti Iye anadzikhuthulira Yekha, kapena *anadzitsanulira*, tsopano, ife tingaganizire monga chonchi, kuti Iye “anasanza,” mawu a Chingerezi akuti *anadzikhuthulira*, kapena *anadzitsanulira* kuchokera mwa Iye, mwaona, chinachake chinatuluka kuchokera mwa Iye chimene chinali chosiyana ndi Iye. Koma mawu akuti *kenos*, mu Chigriki, samatanthauza kuti Iye “anasanza,” kapena china. . . nkono Wake unachokapo, kapena diso Lake linachokapo, munthu wina.

<sup>78</sup> Zimenezo ndi zakuti, Iye anadzisintho Yekha, Iye “anadzitsanulira Yekha mmenemo,” (Ameni!), kupita mu chigoba china, kupita mmawonekedwe ena. Osati kuti munthu wina anachoka kwa Iye, wotchedwa Mzimu Woyera, koma Izo anali Iye Mwiniwake. Inu mukumvetsa zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye Mwiniwake anadzitsanulira Yekha mwa anthu. “Khristu mwa inu!” Ndi zokongola bwanji, ndi zodabwitsa bwanji, kuziganizira, Mulungu kudzitsanulira Yekha mwa munthu, mwa wokhulupirira. “Anadzitsanulira!” Ilo linali gawo la sewero Lake, kuti achite zimenezo.

Mulungu, chidzalo chonse, Umulungu wonse mu thupi unali mwa Munthu uyu, Yesu Khristu. Iye anali Mulungu, ndipo Mulungu yekha. Osati munthu wachitatu kapena munthu wachiwiri, kapena munthu woyamba; koma Munthuyo, Mulungu anaphimbidwa mu mnofu wa munthu.

<sup>79</sup> Timoteo Woyamba 3:16, “Popanda kutsutsana chinsinsi cha umulungu ndi chachikulu; pakuti M-u-l-u-n-g-u, Elohim,” chilembo chachikulu M-u-l-u-n-g-u, mu Baibulo. Mufufuzire izo mmbuyo, aliyense. Izo zimafuluzira ku, pachiyambi, Ilo linati, “Elohim.” “Pachiyambi, Elohim.” Mukuona? “Ndipo, Elohim, popanda kutsutsana chinsinsi cha Elohim ndi chachikulu; pakuti Elohim anasandulika thupi, ndipo ife tinamugwira Iye.” Elohim, anaphimbidwa mu mnofu wa munthu! Yehova wamkulu yemwe anaphimba danga lonse, nthawi, ndi paliponse, anasandulika munthu. Ife tinamugwira Iye, Elohim. “Pachiyambi, Elohim. Ndipo Elohim anasandulika thupi, anadzakhala pakati pathu.”

<sup>80</sup> Chiyani? Iyi ndiyo njira Yake, zigawo za sewerolo. Umu ndi mmene Iye ati alisewerere ilo, njira Yake yodziululira



Yekha kwa ife ngati munthu winawake. Ife ndi achivundi, ndipo Iye amadziwa zimenezo. Ndipo ife timangomvetsa ngati zivundi. Ife timangodziwa ngati zivundi. Ife timangodziwa momwe zokhudzira zathu zingatidziwitsire ife, ndipo zina zonsezo ife timayenera kungokhulupirira mwa chikhulupiro. Ife timayenera kunena kuti alipo Mulungu; kaya ife tikumuwona Iye, kapena ayi, ife timakhulupirira zimenezo, mulimonse. Mukuona? Kaya alipo kapena ayi, ife timakhulupirirabe izo chifukwa Mulungu ananena chomwecho.

<sup>81</sup> Monga Abrahamu, samatha kumuwona mwana ameneyo, panalibe zizindikiro, panalibe kutenga pakati kwa—kwa Sarah, panalibe ngakhale kusintha kwanyengo kulikonse kapena chirichonse, komabe Mulungu ananena choncho. Ziyembekezere zonse, ngakhale iyeyo—chiberekero chake chinali chakufa, ndipo moyo wake mwa iyeyo unali utapita, ndipo—msempha wa moyo wake unali utawuma, ndipo wake—moyo wake unali utauma mkati mwake. “Ndipo komabe iye sanadzandime pa lonjezo la Mulungu mu kusakhulupirira, koma anali wamphamvu, akupereka matamando, akudziwa kuti Mulungu anali wokhoza kuchita chirichonse chimene Iye anati Iye akanadzachita.”

Iliipo njira yomwe ife tiyenera kuwakhulupirira Mawu amenewo lero. Kodi izo zikhala motani? Ine sindikudziwa. Mulungu anati izo zidzakhala mwanjira imeneyo, ndipo zikhazikika motero.

<sup>82</sup> Kodi Munthu wamkulu wosawoneka uyu ndi ndani? Kodi Uyu ndi ndani yemwe Abrahamu anamuwona mu masomphenya? Ngakhale pamapeto, pake, Iye anadzawonetseredwa mu thupi, mwanayo asanabwere. Mulungu Mwiniwake anabwera kwa Abrahamu mmawonekedwe a munthu, pa nthawi ya kumapeto. Anawonetseredwa! Iye anamuwona Iye mu Kuwala kwakung’ono nthawi ina; iye anamuwona Iye mmasomphenya; iye anamva Liwu Lake; mavumbulutso ambiri. Koma asanati mwana wolonjezedwayo, iye anamuwona Iye mmawonekedwe a munthu, ndipo analankhula naye Iye, ndipo anamudyetsa Iye nyama ndi chakumba. Mukuona? Zindikirani, Mulungu Mwiniwake ataphimbidwa mu nfnofu wa munthu.

<sup>83</sup> Ili ndi gawo la njira Yake. Iyi ndi njira imene Iye amadziwonetsera Yekha kwa ife, amawonetsera Mawu Amuyaya, Mulungu, Yehova kusandulika thupi. Monga mu Yohane Woyera 1, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo. . . Pachiyambi panali Elohim, ndipo Elohim anali. . . anadzakhala Mawu, ndipo Mawu anali Elohim. Ndipo Mawu anasandulika Elohim.” Mukuona? Ndi chinthu chomwe chomwecho, kumangofutukuka basi.

<sup>84</sup> Monga chikhumbo, mwaona, izo ziri mwa Mulungu. Chikhumbo ndi lingaliro lako. Mulungu pachiyambi, Wamuyayayo, Iye sanali Mulungu nkomwe. Iye anali

Wamuyayayo. Iye sanali Mulungu nkomwe; Mulungu ndi chinthu chopembedzedwa, kapena chinachake. Mukuona? Kotero Iye sanali nkomwe chimenecho. Iye anali Elohim, Wamuyayayo. Koma mwa Iye munali malingaliro Iye ankafuna kuti adzakhale chomagwirika. Ndipo kodi Iye anachita chiyani? Kenako Iye analankhula Mawu, ndipo Mawuwo anasandulika chogwirika. Ndicho chithunzi chonsecho, kuyambira ku Genesis mpaka Chivumbulutso. Palibe cholakwika. Ameneyo ndi Elohim akukhala chogwirika kuti Iye adzakhoze kumagwiridwa, kumakhudzidwa. Ndipo mu Zakachikwi, ndi ameneyo Elohim atakhala pa Mpandowachifumu, mwaona, izo nzoona, ali ndi anthu Ake onse atamuzungulira Iye, amene Iye anawakonzeratu asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi.

<sup>85</sup> Ziri chimodzimodzi ndi munthu amene akumanga mabelu kapena akupanga mabelu, wosula. Belu lirilonse limayenera kuti lizilira mosiyana ndi limzake. Zipangizo zomwezo, koma chitsulo chochuluka chonchi, chitsulo chochuluka chonchi, mkuwa wochuluka chonchi, zoti zizipangitsa ilo “kumalira.”

<sup>86</sup> Umo ndi mmene Mulungu amachitira. Iye anabala ichi kuchokera kwa icho, ichi kuchokera kwa icho, ichi kuchokera kwa icho, mpaka Iye anapeza ndendende chimene Iye ankachifuna. Umo ndi mmene Iye anadzera kuno. Mulungu anadzivundukula Yekha mu Lawi la Moto kutsika kudzera mwa aneneri, kenako anadzalowa mwa Mwana wa Mulungu, chimene, Iye anali Mulungu. Mukuona, ndi Mulungu yemwe yemweyo akutulutsa ndendende, kuchokera ku ungwiro mpaka ku ungwiro, kuchokera ku ulemerero kupita ku ulemerero. Umo ndi mmene Mpingo ukuyendera.

<sup>87</sup> Zindikirani, kudutsa mmibadwo, mwanjira yomweyo, mwa aneneri Ake, Iye wadziulula Yekha. Iwo sanali ndendende aneneri, iwo anali milungu. Iye ananena choncho. Chifukwa, zimene iwo ankalankhula zimakhala Mawu a Mulungu. Iwo anali thupi limene Mulungu amaphimbidwamo. Iwo anali milungu. Yesu anatero, Iyemwini, anati, “Inu mukunditsutsa Ine bwanji pamene Ine ndikuti Ndine Mwana wa Mulungu, ndipo lamulo lanu lomwe limanena kuti iwo amene Mawu a Ambuye amabwerako anali milungu?” Mukuona?

<sup>88</sup> Kotero amakhala Mulungu atawumbidwa mwa munthu wotchedwa mneneri. Mukuona? Ndipo Mawu a Ambuye amabwera kwa munthu ameneyu, kotero samakhala mneneriyo; mneneriyo amakhala chophimba, koma Mawu amakhala Mulungu. Mawu a munthu sangathe kuchita monga choncho. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Iwo sangathe kuchita mwa mkhalidwe umenewo. Koma mwakulankhula kwina amakhala Mulungu. Mwaona, Iye amakhala Mawu a Mulungu mmawonekedwe a munthu, amatchedwa “munthu.”

Zindikirani, Iye sanasinthe nkomwe chikhaliidwe Chake, mawonekedwe Ake okha. Ahebri 13:8, amati, “Iye ali yemweyo

dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Koteru Iye sanasinthe chikhalidwe Chake pamene Iye anabwera. Iye nthawizonse amakhala Mneneri ameneyo, monse kudutsa m’badwo, chinthu chomwe chomwecho: Mawu, Mawu, Mawu, Mawu. Mukuona? Iye sangathe kusintha chikhalidwe Chake, koma Iye anasintha mawonekedwe Ake. Ahebri 13:8, amati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Iye anangosintha chigoba Chake.

<sup>89</sup> Monga ine ndinasintha pa kukhala mwamuna wa pabanja, pamene mwana wanga anabadwa, zitatero ine ndinadzakhala bambo. Pamene mdzukulu wanga anabadwa, ndine agogo. Mukuona? Koma, ine sindikusintha; ameneyobe—ameneyobe ndi ine. Mukuona? (Ndi mmene aliri Mulungu.) Izo zangokhala kuti ndinasintha anga. . . Mwaona, ndi kungosintha mawonekedwe ako chabe. Mukuona?

Zindikirani. Ndipo chirengedwe chimasintha izo kuchokera kokhala mnyamata kudzakhala wausinkhu wa pakati, kukakhala bambo wokalamba. Ndipo ndi inu pamenepo, inu mukuona, iwe umangosintha mawonekedwe ako.

<sup>90</sup> Tsopano, inu simungati mnyamata wamng’ono wakhala apayu, wausinkhu wa zaka sikisitini, mungati iye ndi agogo. Iye sangakhale. Mawonekedwe ake ayenera kusinthidwa. Zaka pang’ono zimasintha izo, zikatero iye amadzakhala agogo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>91</sup> Koma izo amakhala Munthu yemwe yemweyo nthawi zonse, Munthu yemweyo, Mulungu nthawizonse. Mwanjira iyi Iye amadziulula Yekha kwa anthu Ake, pochita zimenezi. Zindikirani, kudutsa mu m’badwo wa Lawi la Moto, Iye amadziulula Iyeyekha kwa anthu Ake. Mu m’badwo wa—wa Yesu, Iye amadziulula Yekha kwa anthu Ake. Mu m’badwo wa Mzimu Woyera, ngati Mwana wa Mulungu. Mwana wa Davide. . . Iye nthawizonse amadziulula Yekha mwachikhalidwe chimenecho kwa anthu Ake, amawapangitsa anthuwo kuti amudziwe Iye. Iye amaphimbidwa kuseri kwa chinachake, zindikirani, mwanjira yomwe yomweyo, kapena chikhalidwe chomwecho, nthawi zonse.

<sup>92</sup> Mulungu anaphimbidwa mwa Yesu, kuti adzachite ntchito ya chiwombolo pa mtanda. Mulungu sakanatha kufa, ngati Mzimu. Iyeyo ndi Wamuyaya. Koma Iye anachita kuvala chigoba ndipo anadzachita gawo la imfa. Iye anadzafa, koma Iye sibwenzi atachita izo mmawonekedwe Ake a Mulungu. Iye ankayenera kuchita izo mmawonekedwe a Mwana, ngati Mwana wa munthu, pa dziko lapansi. Mukuona? Iye ankayenera kudzakhala mmawonekedwe a Mwana. Kenako pamene Iye anadzabwerera pa Pentekoste, Iye anali Mwana wa Mulungu kachiwiri. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mukumvetsa lingalirolo? Iye anali. . .

<sup>93</sup> Iye anachita kubwera kudzalowa mu mnofu wa munthu, kuti...ndipo palibe aliyense, panalibepo chikhumbo chogonana. Chifukwa izo zikutsimikiziranso neno lathu la mbewu ya serpenti, mwaona, “kugonana,” mwamtheradi kugonana. Osati maapulo; kugonana! Izo nzoona. Izo ziyenera kukhala. Zindikirani apa, mwaona, pakuti munthu wabwino aliyense... Tayang’anani pa aneneri awo kumbuyo uko, koma Iye ankayenera kukhala woposa mneneri. Mukuona? Pofuna kuti adzachite zimenezo, Iye anabwera mwa kubadwa kwa namwali, kusonyeza kuti kubadwa mwa namwali kumatsimikizira... Iye ankayenera kubadwa mwakubadwa kwa namwali, kuti adzachotsepo themberelolo, Katemera. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Chotero, izo ziyenera kuti kunali kugonana. Iye anazitsimikizira izo mu kubwera Kwake Komwe; Iye sanabwere mu chikhumbo chogonana, koma podzera mwa kubadwa mwa namwali. Ndipo Iye anasintha chigoba Chake kuchokera kwa Yehova anadzakhala Yesu, ndi cholinga chakuti adzatenge ntchito ya chiwombolo mu sewero limene Iye anali kulichita, mwa Mulungu pa mtanda.

<sup>94</sup> Agriki ankafuna kuti amuwone Iye. Mu Yohane Woyera 12:20, ambiri a inu mwandimvapo ine ndikulalikira pa kunena kumeneko, “Mwabwana, ife tikufuna kumuwona Yesu.” Kodi inu munazindikira zimenezo?

<sup>95</sup> Tsopano, Agriki anali ophunzira, iwo anali amuna amphamvu. Ndipo iwo anali—iwo anali ndi—ndi kumverera kwakukulu kwa Mulungu, monga Paulo analalikira kwa iwo pa phiri la Mars. Ndipo iwo anali, iwo—iwo analitsogolera—iwo analitsogolera dziko mu sayansi ndi—ndi maphunziro, iwo anali anthu apamwamba. Koma iwo ankapembedza ndi kumakhulupirira mu nthano ndi zoterozo, mabuku a luso ndi luso la zosema, ndi zina zotero.

<sup>96</sup> Koma iwo—iwo—iwo anakondowededwa naye Munthu uyu Yemwe amakhoza kuchiritsa odwala ndipo amakhoza kuneneratu zinthu zimene zimachitika, mpaka pa dontho. Ndipo iwo anakondowededwa naye, kotero iwo anabwera kuti adzamuwone Iye. Tsopano, penyetsetsani mwacheru tsopano, musaphonye izi. Mukuona? Ndipo iwo anabwera ndipo iwo anati kwa Fillipi, yemwe anali waku Bethsaida, “Bwana, ife tikufuna kumuwona Yesu.” Ndipo Fillipi ndi wophunzira wina anamubweretsa iye kwa Yesu, kuti amuwone Yesu.

<sup>97</sup> Tsopano zindikirani mawu kumene amene Yesu analankhulanso kwa iwo, chifukwa iwo anabwera kuti adzawone Yemwe Iye anali, ndipo iwo analephera kuti amuwone Iye. Iwo anawona mawonekedwe, koma Iye anali mu kachisi Wake. Mulungu anali mu kachisi Wake, ataphimbidwa mu mnofu wa munthu. Zindikirani mawu amene Iye ananena, “Kupatula mbewu ya tirigu itagwera mu nthaka, mwaona, ndi kufa, iyo imangokhalapo yokha.” Mukuona? “Ora lafika,

ilo likhala kuti Mwana wa munthu akwezedwa, mwaona, ndipo Iye ayenera kuti achoke ku dziko lino. Ndipo kupatula ora ili litabwera, inu simudzatha konse kuziwona Izo.” Mukuona?

<sup>98</sup> Apa, nchifukwa chiyani iwo analephera kumuwona Yesu? Iye anali ndi chigoba. Mulungu anali ali ndi chigoba. Agriki ankafuna kumuwona Mulungu, ndipo apa Iye anali, koma iwo analephera kuti amuwone Iye chifukwa cha chophimbacho. Ndipo ndicho chinthu chomwecho lero, iwo sakutha kumuwona Iye chifukwa cha chophimbacho. Icho chiru pa nkhope zawo. Agriki awa anali ali ndi chigoba, kapena Yesu anali ali ndi chigoba kwa Agriki awa.

<sup>99</sup> Zindikirani, Iye ananena kwa iwo, “Kupatula mbewu iyi ya tirigu itagwera mu nthaka, iyo imangokhalapo yokha.”

<sup>100</sup> Iwo, iwo samatha kumvetsa kuti zikutheka bwanji, ndi chifukwa chiyani kuti iwo samatha kumuwona Iye. Apo panaima munthuyo. Iwo anabwera kuti adzamuwone Mulungu, ndipo iwo anamuwona munthu. Mukuona? Iwo sakanatha kumuwona Mulungu chifukwa Mulungu anali ataphimbidwa kwa iwo. Tsopano musunge izo mmalingaliro mwanu, Mulungu anali ataphimbidwa mwa munthu. Iwo amatha kunena kuti, “Palibe munthu yemwe angathe kuchita ntchito izi pokhapokhapo atakhala Mulungu. Palibe munthu angathe kuchita izo, ndipo zikutheka bwanji kuti apa paima munthu ndipo komabe ntchito za Mulungu zikuwonetseredwa kudzera mwa Iye!” Mwaona, iwo samatha kumvetsa kuti Mulungu anali ataphimbidwa.

<sup>101</sup> Iye waphimbidwa mwa munthu, chimodzimodzi monga Iye nthawizonse amaphimbidwira. Koma, Iye anali ataphimbidwira kwa iwo, Iye anali mu kachisi Wake wa umunthu. Mulungu anali mu kachisi wa umunthu. Tsopano, mukhale osamalitsa kwenikweni, tsopano Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mwaona? Mulungu ataphimbidwa, akudzibisa Yekha kwa dziko lapansi, ataphimbidwa mwa munthu. Mukuona? Apa panali Mulungu! Agriki amenewo akuti, “Ife tikufuna kumuwona Iye.”

<sup>102</sup> Ndipo Yesu anati, “Mbewu ya tirigu iyenera kugwa ndi kufa.” Iwe uyenera kuti ufe kwa malingaliro ako onse. Iwe uyenera kuchokako ku malingaliro ako omwe.

Monga mmene anali ophunzira aja, iwo samatha kufotokoza za kudya thupi Lake ndi—ndi kumwa Magazi Ake, koma, mwaona, iwo anali atafa kwa zinthu zimenezo. Iwo anali atafa kwa Mfundo, iwo anali atafa kwa Khristu. Ziribe kanthu kuti ndi chiyani, kapena kugonjetsedwa kochulukira bwanji kumene kumawoneka kuti Iye anali nako, iwo anakhulupirirabe Izo mulimonse. Mukuona? Iwo amatha kuwona mwa Munthu ameneyo; Munthu amene amadya, amamwa, amawedza, amagona, china chirichonse, anabadwa kuno pa dziko lapansi,

ndipo amayenda ndi iwo, amalankhula nawo iwo, amavala zovala monga ena onse a iwo, koma ameneyo anali Mulungu.

<sup>103</sup> Koteru Agriki amalephera kuti amuwone Iye, chifukwa Iye anali atabisika kwa iwo, mwa munthu. Zindikirani Mawu Ake kwa iwo, “Kupatula mbewu iyi ya tirigu itagwera mu nthaka.”

<sup>104</sup> Mulungu ataphimbidwa mmawonekedwe a munthu, anadzibisa Yekha kuti iwo asamuwone. Iwo amangotha kumuwona munthu basi. Koma Okonzedweratu awo anamuwona Mulungu. Wina anawona munthu, mmodzi winayo anawona Mulungu. Mukuona? Ndipo uyo anali Mulungu ataphimbidwa mwa munthu, kuwapangitsa awiri onsewo kukhala olondola, koma chikhulupiriro chako mwa icho chimene iwe sukuchiwona. Iwe umachikhulupirira icho, mulimonse. Mulungu ataphimbidwa mwa munthu. Iye anali mu thupi limenelo, ndipo thupi limenelo linali chophimba Chake. Chophimbacho chinang’ambika, mwaona, kuti Mulungu akhoze kuwonetseredwa.

<sup>105</sup> Mu Chipangano Chakale, Mulungu amabisidwa pamene Iye amakhala pa mpando Wake wachifundo; pa mpando wachifundo, ndi chophimba. Mu Chipangano Chakale, Mulungu amakhala mu kachisi Wake. Koma anthu amabweramo ndi kumadzapembedza monga chonchi, koma, kumbukirani, uko kumakhala chophimba (ameni) chimene chinkamubisa Mulungu. Iwo ankadziwa kuti Mulungu anali kumeneko. Iwo samatha kumuwona Iye. Lawi la Moto lija silimawonekanso kumeneko. Kodi inu mumadziwa? Palibepo nthawi imodzi mu Lemba, kuyambira nthawi imene Lawi la Moto linapita kuseri kwa chophimba chimenecho, imene Ilo linawonekeranso kachiwiri, kufikira Ilo litabwera kuchokera kwa Yesu Khristu. Mulungu anali ataphimbidwa!

<sup>106</sup> Pamene Iye anadzaima pa dziko lapansi, Iye anati, “Ine ndinachokera kwa Mulungu ndipo Ine ndikupitanso kwa Mulungu.”

<sup>107</sup> Kenako Paulo, (pambuyo pa imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro), ali panjira yake waku Damasiko, apo panali Lawi la Moto lija kenanso. Kodi Ilo linali chiyani? Kutuluka kuchokera kuseri kwa chophimba! Ulemerero kwa Mulungu!

<sup>108</sup> Iye anali kuseri kwa chophimba. Apa Iye anali kuseri kwa chiyani? Chophimba cha khungu. Mwaona, “zikopa za katumbu,” kuseri kwa chophimba. Ndipo pamene chophimba chija chinang’ambidwa pa tsiku la kupachikidwa, chophimba chimene Iye anakutiridwiramo chinang’ambidwa pa tsiku la kupachikidwa, mpando wonse wachifundo unabwera pa mbalambanda.

<sup>109</sup> Tsopano, Ayuda samatha kumvetsa momwe Mulungu akanakhallira ndi chifundo pa ochimwa, anthu oyipa monga ifeyo. Koma iwo samatha kumuwona Uyu Yemwe anali kupereka

chifundo, chifukwa Iye anali atabisika. Iye anali kuseri kwa mpando wachifundo, mkatimo, wokhala ndi zikopa za akatumbu zikulendewera pansi, zikumuphimba Iye. Kale. . .

<sup>110</sup> Kale, munthu aliyense akapita kuseri kwa chophimbacho, iyo imakhala imfa yadzidzidzi. Amen. O, ife tipezapo phunziro apa mu miniti, mwaona, ngati inu mungathe—inu mungathe kuchilandira Ichi. Kuyenda kupita kuseri kwa zikopa zimenezo. . . Ngakhale mmodzi wa ana a ansembe anayeserapo kuti achite izo nthawi ina, ndipo anafa. “Musamapite kuseri kwa chophimba chimenecho.” Munthu amene amapita kuseri. . . Bwanji? Nthawi imeneyo nkuti kulibeko chiwombolo, mmenemo. Izo zinali mwakulankhula kwina. Izo zinangokhala mwakulankhula kwina. Ndipo chirichonse cha *mwakulankhula kwina* chimakhala kuti sichinakhalebe chinthu chenicheni, mwaona, mwakulankhula kwina basi. Icho chinali chiwombolo. . . Tchimo limaphimbidwa, osati kufutidwapo. . . kuchotsedwapo, kani, osati kuchotsedwapo. *Kuchotsedwapo* ndiko “kusudzulidwa ndi kuikidwa kutali.” Ndipo koteru magazi a nkhosa ndi mbuzi samakhoza kuchita zimenezo, koteru Yehova amabisidwa kuseri kwa chophimba. Tsopano, kumbuyo kuseri kwa chophimba ichi kumene Iye amabisidwako, kukalowa kumeneko, munthu amagwa nkufa, akayesera kuti akalowe Kumeneko.

<sup>111</sup> Koma chichitikireni Pentekoste, chichitikireni Kupachikidwa, pamene chophimba chimenecho chinang’ambidwa kuchokera pamwamba mpaka pansi, kwa kam’badwo kameneko. . . Yesu anali Mulungu ameneyo, ataphimbidwa. Ndipo pamene Iye anafa pa Kalvare, Mulungu anatimiza moto ndi mphenzi, ndipo anang’amba chophimba chimenecho kuchokera pamwamba mpaka pansi, mwakuti mpando wonse wachifundo unali pa mbalambanda. Koma iwo anali akhungu kwambiri kuti aziwone Izo. Monga Mose akunenera apa, nayenso, kapena. . . Paulo anati, powerenga za Mose, “Pamene Mose akuwerengedwa, lero, chophimba chimenecho chikadali pa mtima wawo.” O, m’bale, mlongo, icho ndi chimene Ayuda anachita pamene chophimba chinang’ambidwa ndipo chinamubweretsa Mulungu pa mbalambanda, atapachikidwa pa mtanda. Iye anali pa mbalambanda, koma iwo samatha kuziwona Izo.

<sup>112</sup> Kodi zingakhoze kukhala zotheka kuti Amitundu achita chinthu chomwecho? O Mulungu! Pamene iwo akhala nayo mibadwo ya mpingo, ya Mwana wa Mulungu; koma pamene tsopano chophimba cha zipembedzo ichi ndi zinthu, chophimba ichi cha mwambo chimene ife tiri nacho kuyambira pa Pentekoste, pamene miyambo ya mpingo yang’ambidwa, zinthu zimene anthu amati, “Masiku a zoziziwitsa anatha, ndi zinthu izi,” ndipo Mulungu wachotsapo chophimba cha Iwo, ndipo wawubweretsa Iwo pa mbalambanda, ndipo iwo akonzekera

kuti awupachikenso Iwo kachiwiri, basi chimodzimidzi mofanana.

<sup>113</sup> Mulungu wovundukulidwa, ali pa mbalambanda, iwo bwenzi atamuwona Iye ataima pamenepo. Komabe Iye anali wawamba kwambiri, Iye anali munthu wamba. Iwo analephera kuziwona Izo. Mwaona, apo panaima munthu. “Chabwino,” iwo anati, “munthu uyu, kodi Iye anachokera ku sukulu iti?” Koma, kumbukirani, pamene nthungo ija inakantha thupi Lake, Mzimu umenewo unamusiya Iye, kachisi. . . zimango zoperekera nsembe zinatembenezika, ndipo mphenzi zinasesa kudutsa mkachisimo ndi kung’amba chophimbacho. Chinali chiyani icho? Apo panali Mulungu wawo atapachikidwa pa Kalvare, ndipo iwo anali akhungu kwambiri kuti aziwone izo.

<sup>114</sup> Amubweretsa Iye pa mbalambanda, ndipo panobe iwo sakuziwona Izo! Iwo achititsidwa khungu. Mulungu, kuphimbidwa mwa munthu!

<sup>115</sup> Inu mukukumbukira, Iye anatembenukira kenako kwa Paulo zitachitika zimenezo, ndi kwa Petro mu ndende, ngati Lawi la Moto. Mukukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>116</sup> Koma mu masiku otsiriza Iye akuyenera kuti adzabwererenso kachiwiri, koma Lawi la Moto likuyenera kuti libwererenso kuti lidzawonetsere Mwana wa munthu, mwaona, kudzawasonyeza Mawu, Kuwala. Miyambo, yakhala ilipo, idzachotsedwapo. Apo sipadzakhala kalikonse kati kadzasokoneze Izo; izo zichitika, mulimonse. Mulungu adzangozikhadzula zipembezdo zimenezo ndi miyambo.

Kodi Iye adzazichita izo ndi Mzimu wa mtundu wanji? Monga Iye anachitira pa malo oyambirira. Taonani zimene Iye anachita mu masiku a Eliya, mu masiku a Yohane. “Inu musati muziganiza kumanena mwa inueni kuti muli ‘naye Abrahamu kwa atate anu,’ chifukwa Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu.” Mukuona? Inu musati muziganiza, “Chifukwa, ine ndine wa *ichi* ndipo ine ndi wa *icho*.” Mukuona? Mulungu akung’amba chophimbacho, mwaona, kuti akasonyeze Yemwe Iye ali. Mwaona, muwone chophimbacho pamene icho chikung’ambidwa apa tsopano, ife tikupeza tsopano.

<sup>117</sup> Tsopano, ndipo nthawi ina, munthu akayenda kudutsa chophimba icho, iyo imakhala imfa yadzidzidzi. Tsopano ndi imfa kuti usapite kukadutsa Icho! Amen. Ngati iwe sungathe kuswa chophimba icho cha mwambo, kuswa khoma ilo la chipembezdo, kuti ukamuwone Mulungu ali mu mphamvu Yake, ndi imfa. Nthawi ina kumene izo zinali imfa kupitako, tsopano ndi imfa kukhala kunja kwa icho. Mpando wonse wa Chifundo ukukhala pa mbalambanda, aliyense akhoza kuwuwona Iwo, chophimbacho chang’ambidwa. Ulemerero



kwa Mulungu! Mpando wonse wa chifundo ukubwera pa mbalambanda.

<sup>118</sup> Zinatheka bwanji kuti Mulungu achitire chifundo ochimwa oyipa ngati ife, pamene Iye amadzibisa Yekha, chinali chinsinsi. Ndipo tsopano Izo ziri pa mbalambanda, kapena powonekera, zawululidwa ndi Mawu Ake. Izo nthawizonse zimakhala Mawu, mosalekeza, ameneyo ndi Mulungu. Ndi Mawu amene amatsegula izo. Ngati anthu amenewo akanawadziwa Mawu a Mulungu tsiku lijali pamene Yesu ankafa, iwo akanati awuwone Mpando Wachifundo, iwo akanamuwona Yemwe Iye anali.

<sup>119</sup> “Anali ndani Ameneyo pamenepo? Nchifukwa chiyani chophibacho chinang’ambidwa?” Kumbukirani, inali imfa kukalowa Mmenemo. Palibe amene amatha kumuwona Iye. Mose anamuwona Iye mmawonekedwe, Iye anali kamvulu... iwo unali—nsana wa Munthu. Chabwino, ndi Uyu apa, nsana wowukha magazi, Munthu yemwe uja! Kodi chinali chiyani Icho? Mulungu ankafuna kuti awasonyeze iwo Mpando Wachifundo. Mulungu ankafuna kuti awasonyeze iwo Yemwe Iye anali. Kotero chophimba mu kachisi, kuchokera mdzanja la Mulungu, kumwamba, chinang’ambidwa kuchokera pamwamba mpaka pansu, ndipo chinamuwoneka Mulungu pa mbalambanda. Izo anali Yesu Khristu atapachikidwa pa mtanda, Mpando Wachifundo. Ndipo kodi chinali chiyani izo? Anthu anali akhungu kwambiri kuti aziwone Izo.

<sup>120</sup> Tsopano izo zabwerezanso kachiwiri, miyambo yawo! Motani, ndiye, pa Tsiku la Pentekoste, Mawu anabwera ndipo anali mmawonekedwe a “Mwana wa Mulungu.” Ndipo iwo anayamba kuzichita bungwe izo ku Nicaea, Roma. Ndipo, chinthu choyamba, iwo anapita kwa Methodisti, Baptisti, Presbateria, Pentekoste, ndi zina zotero. Iyo ndi miyambo ya bungwe mpaka munthu sakudziwa pamene iye waima.

Koma, ulemerero kwa Mulungu, Iye analonjeza mu masiku otsiriza zimene Iye akanadzachita. Iye akanadzawasonyeza Mawu Ake pa mbalambanda, atatseguka pamaso pathu kachiwiri, mwaona, kuwatsegula Iwo.

<sup>121</sup> Ngati iwo akanangowadziwa Mawu, iwo akanadziwa Yemwe Yesu anali. Ngati munthu akanangowadziwa Mawu a Mulungu, iye akanadziwa ora limene ife tiri nkukhalamo ndi zimene zikuchitika. Iwo amangokana kuti amvetsere Mawu amenewo. Miyambo yawo! Ndi chiyani chinawapangitsa Ayuda amenewo kuti awone izo? Chiyani? Zinkawoneka ngati iwo akanatha kuwona kwenikweni, chifukwa chinthucho chinali chitang’ambidwa motseguka. Icho chinang’ambidwa motseguka ndi cholinga.

<sup>122</sup> Kodi chitsitsimutso chikuchitikachi ndi chachiyani tsopano? Kodi icho chipitirira motani? Kodi icho chingadalitsike motani? Ine sindikusamala kuti chiri ndi otsanzira ochuluka bwanji,

kapena china chirichonse, izo ziribe . . . Pamene Mose anatuluka, uko kunali gulu losakanizikana limene linatuluka ndi iye. Koma kodi izo zimachitikiranj? Ndi Yehova Mwiniwake akuchotsa chophimba pa Mulungu, kuti akasonyeze kusiyana kwa pakati pa chabwino ndi choipa. Ndi chiti, Methodist, Baptist, Presbateria, kapena ndani ali wolondola? Mawu a Mulungu ndi omwe ali olondola! “Mulole mawu a munthu aliyense akhale abodza, ndipo Anga Choonadi.” Mulungu samasowa wotanthauzira. Iye amachita kutanthauzira Kwake Kwake. Iye amawawonetsera Iwo, ndipo ku- . . . iko kumapereka kutanthauzirako. Mulungu kudzivundukula Yekha. O, mai! Pakati pathu pomwe, ife tikuwona dzanja Lake lalikulu likunena zinthu zimenezi, likuchita zinthu zimenezi.

<sup>123</sup> Ndiri ndi chinachake pa zimenezo usikuuno, mwaona, momwe mungamaliyang’anire dzanja la Mulungu, chimene Ilo limachita, momwe Ilo limadzifunulirira lokha. Mukuona?

<sup>124</sup> Ndipo anthu amati, “O, Zimenezo ndi zamkhutu. Zimenezo ndi kutengeka pamenepo. Palibepo kanthu kwa Izo. Zimenezo ndi zamkhutu. Ameneyo ndi Bezebule. Ameneyo ndi mdierekezi. Kumeneko ndi kubwebweta. Zimenezo ndi *izi*.” Mwaona, chinthu chomwecho chimene iwo ankanena za Iye.

<sup>125</sup> O mpingo, ndipo ngati tepi iyi iti idzatuluke, kodi inu simukuwona, atumiki a Uthenga, kodi inu muli pati? Kodi inu simukutha kuliwona ora limene ife tirimo? Mulungu, akudzisonyeza Yekha, akuika pambali. . . Taonani, Iye anatenga chophimba cha mkachisi ndipo anaching’amba icho mzidutswa, kuti iwo akhoze kumuwona Mulungu pa mbalambanda, ndipo iwo anali akhungu kwambiri kuti amuwone Iye. Ndipo Iye wachita chinthu chomwe chomwecho lero, wawaika Mawu Ake patsogolo pathu pomwe, zimene Iye analonjeza. Lonjezo lirilonse mu Mawu, liri patsogolo pathu pomwe, pa mbalambanda!

<sup>126</sup> Inu mukudziwa chimene mpingo wa Amitundu ukuchita? Chinthu chomwe chomwecho chimene mpingo wa Chiyuda unachita, wakhungu kwambiri kuti uziwone Izo. Ndi zokhazo. Izo zidzakhala pa mitima yawo chimodzimodzi basi monga izo zinali mu tsiku lijali.

<sup>127</sup> Zindikirani, imfa, kukhala kutali kwa Iwo tsopano. Inu muyenera kuti mukalowe mwa Iwo podutsa chophimba ichi, kapena inu simukalowako. Mulungu zikanatheka bwanji kuti awachitire chifundo iwo, koma kumbukirani chimene izo zinali, kuti Mulungu akuwonetsera chimene chinali kuseri kwa chophimba. Penyani chimene chinali kuseri kwa chophimba, Mawu! Kodi icho chinkaphimba chiyani? Mawu! Chinali chiyani icho? Iwo ali mu likasa. Anali Mawu amene chophimbacho chinkawabisa. Mukuona? Ndipo Yesu anali Mawu amenewo, ndipo Iye ndi Mawu amenewo, ndipo chophimba cha mnofu Wake chinkawabisa Iwo.

128 Ndipo lero chophimba cha mwambo chikuwabisa Mawu kachiwiri, kumati, “Iwo siali chomwecho.” Koma Iwo ali chomwecho! Mulungu akuchitira umboni za Iwo, kudzitulutsapo Yekha powonekera mowala ngati dzuwa, pamaso pa aliynse, ndipo iwo akulephera kuti awawone Iwo. Mulungu, atichitire ife chifundo.

129 Mwa choimira, Mose akubwera kuchokera Pamaso pa Mulungu, ali ndi Mawu a Mulungu a m’badwo umenewo. Tsopano penyani, ife tsopano tiri mu Eksodo 19. Musaphonye izi tsopano. Eksodo 19, Mose akubwera kuchokera Pamaso pa Mulungu, kapena 20 ndi 21, 19:20 ndi 21. Mose akubwera kuchokera Pamaso pa Mulungu. Iye wakhala ali mu Mawu. Mawu alembedwa. Ndipo iye, ali Pamaso pa Mulungu, limodzi ndi Mawu, iye anali ndi Mawu a m’badwo umenewo. Pamakhala Mawu a m’badwo uliwonse. Ndipo Mose akubwera, nkhope yake inawala kwambiri! Mukuona? Mawu anali mwa iye, atakonzeka kuti awonetseredwe, aperekedwe kwa anthuwo.

130 Mawu owona, Mulungu anali atawalemba Iwo, ndipo Iwo anali ndi Mose. Zindikirani, Iwo anali ndi Mose ndipo anali atakonzeka kuti awonetseredwe. Iye anali Mawu kwa iwo, iye anali Mawu amoyo, atabisika. Atadziphimba yekha, Mose amachita kuika chophimba pa nkhope yake. Bwanji? Iye anali Mawu amenewo. Amen. Kufikira Mawu amenewo atadziwitsidwa, Mose amachita kudziphimba yekha. Amen!

Kodi inu mukuziona Izo? Kulikonse kumene kuli Mawu, Iwo amaphimbidwa.

131 Mose anali ndi Mawu. Tsopano kumbukirani, Mawu akatha kuwonetseredwa, Mose amabwereranso kukakhala Mose kachiwiri. Mukuona? Koma nthawi imene Mawu anali mwa iye kuti awapereke, iye amakhala Mulungu; chabwino, iye samakhalanso Mose aponso. Iye amakhala ndi Mawu a Ambuye a m’badwo umenewo. Panalibe kalikonse kamene kamamukhudza iye kufikira zimenezo zithe kaye; anali ndi Mawu amenewo limodzi naye. Koterok, choncho, pamene iye amabwera, anthuwo amatembenuza mitu yawo; iwo samatha kumvetsa. Iwo anali atasinthidwa. Iye anali munthu wosiyana. Iye amabwera ndi Mawu amenewo. “Ndipo iye amaika chophimba,” Baibulo limatero, “pa nkhope yake,” pakuti iye anali ndi Mawu. Ndipo iye anali Mawu kwa iwo.

132 Tsopano taonani, ngati Mose...O m’bale, apa pakhala kutonzedwa. Koma ngati Mose...Monga Paulo ananena apa mu Akorinto Wachiwiri, mutu wa 3. Ngati Mose ankachita kuphimba nkhope yake ndi Ulemerero wa mtundu umenewo pa iye...mwaona, chifukwa umenewo unali ulemerero wa chirengedwe, limenelo linali lamulo la chirengedwe. Ndipo ngati Mose, akudziwa kuti lamulo limenelo lidzayenera kudzatha, koma Ulemererowo unali wawukulu kwambiri mwakuti iwo umawachititsa anthuwo khungu, koterok iwo amachita kuika

chophimba pa nkhope yake. Kodi Iwo udzakhala wochuluka bwanji? Anthu ochititsidwa khungu mwauzimu! Uh-huh. Ulemerero umenewo unali woti udzazilala, koma Ulemerero Uwu sungazilale. Mukuona? Mose anali ndi malamulo a chithupithupi, chitsutso, panalibepo chisomo, panalibepo kalikonse; iwo amangokutsutsa basi iwe. Koma Ichi chimene ife tikuchinenachi. . . Ilo linalibe chikhululukiro, ilo limangokuuza iwe yemwe iwe unali. Ichi chimakupatsa iwe njira yotulukirapo.

<sup>133</sup> Ndipo pamene Mawu amenewo ati adzavundukulidwe, o, kalanga, kodi ndi nkhope ya mtundu wanjii imene Iwo ati adzakhale nayo? Iwo adzayenera kuti adzaphimbidwe. Iwo adzayenera kuti adzaphimbidwe. Tsopano zindikirani. Kotero Mzimu waphimbidwa mu kachisi wa umunthu, mwaona, Iye ali woti azilankhula mawu achirengedwe ali ndi chophimba cha chirengedwe.

<sup>134</sup> Tsopano, Paulo akulankhula apa tsopano, ndipo umu—chiganizo ichi, Mzimu—Mawu, “Ife tiri atumiki, osati a lemba, lamulo; koma atumiki okhoza a Mzimu,” mwakuti Mzimu umalitenga lembalo ndi kuliwonetsera Ilo.

<sup>135</sup> Ilo linali lamulo chabe, iwe umachita kupita ndi kukayang’ana pa ilo, ndikuti, “Iwe usachite chigololo. Iwe usabe. Iwe usaname bodza. Iwe usachite *ichi, icho*, kapena *chinacho*.” Mukuona? Iwe umachita kuyang’ana pa ilo.

<sup>136</sup> Koma uwu ndi Mzimu umene umabwera pa Mawu olonjewedwa a m’badwo *uno*, ndi kuwabweretsa ndi kuwawonetsera, osati magome awiri a miyala, koma Kukhalapo kwa Mulungu wamoyo. Osati lingaliro losadziwika limene winawake analipanga, kapena Houdini wina, ndale; koma lonjezo kumene la Mulungu kuwululidwa ndi kumawonetseredwa pamaso pathu pomwe. Kodi ndi chophimba cha mtundu wanjii chiti chidzakhale kumbuyo kwake? Ndipo ku—kuphonya icho. . .

<sup>137</sup> Mwaona, izo zinali zopambana kwambiri mpaka ngakhale anthuwo anati, iwo ananena pamene iwo anamuwona Yehova akutsika mu Lawi la Moto ili, ndipo nayamba kugwedeza dziko lapansi, ndi—ndi zinthu zimene Iye amachita, ndi phiri kuyaka moto. Ndipo ngakhale wina akayerenzeza kuti apite ku phiri limenelo, amakafako. Izo zinali zazikulu kwambiri mpaka ngakhale Mose anachita mantha ndi chivomezicho. Ndiye, ngati nthawi imeneyo Iye anangogwedeza phiri lokha, nthawi ino Iye adzagwedeza miyamba ndi dziko lapansi.

<sup>138</sup> Nanga bwanji Ulemerero Umenewo? Ngati umenewo unaphimbidwa ndi chophimba chachirengedwe, uwu uli kwambiri. . . waphimbidwa ndi chophimba chazimu. Kotero musayesere kuti muziyang’ana pa zachirengedwe; muboworeze mukafike mu Mzimu ndipo mukawone pamene inu muli, mukawone ora limene ife tiri nkukhalamo.

139 Kodi Izo zikupanga chiganizo kwa inu? Mwaona, Icho ndi chophimba chauzimu chimene chiri pa anthu, akuti, “Ndine wa Methodisti. Ine ndiri chimodzimodzi monga aliynenseyo. Ndine wa Baptisti. Ndipo ndine wa Pentekoste.” Kodi inu simukuzindikira izo, chinthu chimenecho ndi chophimba cha mwambo? Icho chikumubisa Mulungu kwa inu. Izo ndi zinthu zimene zikukulepheretsani inu kuti musamamve kukoma zonse . . .

O, inu mukuti, “Ine ndimafuula ndi kulumpha-lumpha.”

140 Iye anati, “Mawu onse!” Eva anakhulupirira Mawu onse kupatula amodzi. Mukuona? Zizikhala Mawu athunthu a Mulungu, lonjezo la ora lino likuwonetseredwa. Mukuona?

141 Zindikirani tsopano pamene ife tikupitirira mtsogolo. Ndiri ndi zambiri apa zoti ndilankhulepo, koma ine ndiri ndi pafupifupi masamba twente, koma izo . . . za—za zolemba, koma ine—ine basi sindilankhula pa zonsezo. Mwaona, ine ndifulumira.

142 Iye waphimbidwa ndi chophimba chachirengedwe asanalankhule Mawu kwa anthuwo. Tsopano, Mulungu amayenera kudziphimba Yekha, monga Iye analonjezera, mu mnofu wa munthu. Mulungu! Kodi inu mukumvetsa Zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Mulungu ayenera kudziphimba Yekha mu mnofu wa munthu, ndi kuika chophimba chauzimu pa iwo, (mukuti, “Chabwino, ndine *ichi* ndipo ndine *icho*”), ndi cholinga chakuti akalankhule ndi anthuwo. Pamene chophimba chimenecho, chimene chiri chophimba cha mwambo, chikang’ambidwa, zikatero . . . icho chimene iwo amati, “Bwanji, masiku a zozizwitsa anatha.”

143 Mnyamata ananena ndi ine tsiku lina, m—mlaliki wamng’ono wa Baptisti kunjira uko, anabwera kwa ine, M’bale Green, ndipo iye anati, “M’bale Branham, ndi ichi chinthu chimodzi chimene ine ndiri nacho chotsutsana ndi inu.” Iye anati, “Inu mukuyesera kuti muwapange anthu . . .” Izo zinali uko ku Ramada Inn, pamene ife tinali ndi msonkhano kumeneko. Anati, “Inu mukuyesera kuti muwapangitse anthu azikhulupirira m’badwo wa atumwi, kuti azikhala moyo lero ngati kuti iwo ali mu m’badwo wa atumwi.” Anati, “M’badwo wa atumwi unatha ndi atumwi.”

Ine ndinati, “Iwo unatero?”

“Eya.”

Ine ndinati, “Wowayankhulira anali ndani mu m’badwo wa atumwi?”

Iye anati, “Atumwi khumi ndi awiri mu chipinda chapamwamba.”

144 Ine ndinati, “Ndiye Paulo panalibepo.” Ine ndinati, “Wowayankhulira anali Petro. Ndipo Petro ananena, pa Tsiku

la Pentekoste, pamene iwo anawona zonse izi zikuchitika, ndipo Mzimu Woyera ukugwira ntchito, iye anati, 'Lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.' Ngati Iye ali kuitanabe, ndiye kuti Chinthu chomwecho chiri pano. Ndi liti pamene m'badwo wa atumwi unatha ndiye? M'badwo wa atumwi udzatha pamene Mulungu ati adzasiye kuitana." Iye sananene kalikonse koma anatenga chipewa chake ndipo anachokapo.

<sup>145</sup> Izo zimatengera Mawu kuti uchite zimenezo. Ndi Mawu. Yesu anamuuzza Satana, "Kwalembedwa." Mukuona? Ndi zimenezotu, "Kwalembedwa."

<sup>146</sup> Ine ndinati, "Petro ananena kuti iwo siwudzatha konse. Onse amene Ambuye adzawaitana, Mdalitso uwu unali wa iwowo. Tsopano inu mukuti, 'Iye anasiya.' Liti?"

"Sindinachite choipa chirichonse?"

Ine ndinati, "Ayi, bwana, osati mpang'ono pomwe. Pitirirani." Uh-huh. Pomwe apo. Mukuona?

<sup>147</sup> Petro ananena kuti izo zinali za aliyense yemwe Mulungu adzamuitane, adzalandira Mdalitso womwewo wa utumwi. Ndiwo—ndiwo Mawu a Ambuye. Mukuona?

<sup>148</sup> Tsopano chophimba cha chachirengedwe. Mulungu, Mawu, anaphimbidwa mu mnofu wa munthu. Chinali chiyani icho? Mulungu anaphimbidwa mwa Mose. Mulungu anali mwa Mose, ataphimbidwa, ndipo Kukhalapo kwa Mulungu kunali mwa iye. Iye anali wangwiro kwambiri ndi Mawu amenewo mwa iye monga choncho, mpaka iye amachita kuphimba nkhope yake. Ndipo iye anali mneneri wotsimikiziridwa yemwe ankawafunyulula Mawu ndi kuwauza iwo, "Inu musachite! Inu mudzatore! Ndipo inu musachite!" Mukuona?

<sup>149</sup> Kutu akapereke Mawu Ake kwa kam'badwo kameneko, Iye anadziphimba Yekha mwa munthu, kupanda kutero Mawu akanachititsa khungu ngakhale oitanidwa omwe. Mukuona? Ngakhale anthu amene anali kunja uko, iwo sanakhoze kupirira kuti aziwone zimenezo. Mu—mu Eksodo ife tikupeza kuti, iwo anati, "Musiyeni Mose azilankhula, osati Mulungu." Mukuona chifukwa chimene Lawi la Moto silimawonekawoneka? Mukuona?

<sup>150</sup> Mulungu anati, "Ine—Ine—Ine ndichita zimenezo. Ine ndidzawadzutsira iwo Mneneri." Ameni! "Ine ndidzawadzutsira iwo mmodzi." Ndipo Iye anabwera ndendende basi. "Ine ndidzamudzutsa, ndipo Iye adzakhala, adzakhala Mawu."

<sup>151</sup> Iye anati, "Ngati iwo akufuna kuti awone chimene Mawu ali..." Anati, "Tsopano, Mose, Ine ndinawonekera kwa iwe uko, mu chitsamba chonyeka." Anati, "Ine nditsika ndipo ndidzayatsa moto phiri limenelo." Anati, "Iwo adzawona kuti iwe umanena zoon. Ine ndidzawonekera kuno mu—mu—

njira yomweyo yoyatsira. Ine ndidzawonekera kuno ndipo ndidzawatsimikizira anthuwo, Ine ndidzatsimikizira utumiki wako.” Ndi chimene Iye anamuuza Mose apa, mawu ambiri zedi.

<sup>152</sup> Zindikirani, Iye anati, “Tsopano Ine ndikuti—Ine ndikupatsa iwe ulemerero pamaso pa anthu.” Anati, “Tsopano, iwe wawauza iwo kuti Ine ndinakomana nawe iwe uko mu chisamba chonyeka; tsopano Ine nditsika, Moto womwewo, ndipo Ine ndiwadziwitsa anthuwo kuti awone kuti iwe sumanama za Izo.” Inu mukhoza kutsimikizira Izo mwasayansi, apobe, ngati inu mukufuna kuteru. Mukuona? “Ine ndibwera komweko ndipo ndiwadziwitsa iwo.”

<sup>153</sup> Ndipo pamene Iye anayamba kubangula, pamene Yehova anayamba kubangula, anthuwo anati, “Ayi! Ayi! Ayi! Musamulole Yehova kuti alankhule; ife ti—ife tifa.”

<sup>154</sup> Mwaona, Iye amayenera kuti aziphimbidwa, koteru Mulungu anadziphimba Yekha mwa Mose ndipo anamupatsa Mose Mawu. Ndipo Mose anatsika ndipo anadzalankhula Mawu a Ambuye, mu chophimba chiri pa nkhope yake. Kulondola uko? Yehova anaphimbidwa mmawonekedwe a mneneri, chifukwa izo mwamtheradi zikanati. . .Ndipo Mulungu anati Iye samalankhulanso ndi iwo kenanso monga choncho. Iye azingolankhula ndi iwo kudzera mwa mneneri. Ndiyo njira yokhaya imene Iye azilankhula kuyambira pamenepo mpakana. Ndiyo njira yokhaya imene Iye amalankhulira. Izo nzoona. Palibe njira ina iliyonse. Iye samanama.

<sup>155</sup> Zindikirani, Mose yekha ndi amene anali ndi Mawu. Tsopano, uko kunalibeko—gulu linabwerako, kunalibeko ngakhale Afarisi, kapena Asaduki, kapena kunalibeko—kagulu kenakake kapena mtundu. Anali Mose! Iye anamutenga munthu mmodzi. Iye sangathe kutenga malingaliro awiri kapena atatu osiyana. Iye amatenga munthu mmodzi. Mose anali ndi Mawu, ndipo Mose yekha. Yoswa analibe Iwo nkomwe. Panalibe aliyense yemwe anali nawo Iwo. Ameni! Yoswa anali—general; Yoswa anali mtsogoleri wa nkondo; Yoswa anali wokhulupirira, Mkhristu. Koma Mose anali mneneri! Mawu sangathe kubwera kwa Yoswa; Iwo ayenera kubwera kwa Mose. Iye anali mneneri wamkulu wa oralo. Zindikirani, Mawu sanabwere konse kwa Yoswa kufikira Mose atachokapo. Ayi, bwana. Mulungu amachita ndi mmodzi pa nthawi. Mulungu ndi mmodzi. Mukuona? Tsopano, Mose yekha ndi yemwe anali ndi Mawu, osati gululo.

<sup>156</sup> Taonani, Mulungu anachenjeza kuti munthu aliyense asayerekeze kuti amutsatire Mose kukafika mu chophimba icho; otsanzira. Mukuona? Mkazi, mwamuna, wansembe, aliyense yemwe anali, waumulungu bwanji, mwamuna chotani, waulemu wochuluka bwanji, kaya akhalepo ochuluka bwanji; Iye anachenjeza, “Mumusiye Mose azibwera yekha! Ndipo ngati munthu aliyense, ngakhale chinnyama, chikakhudza izo,

chiyenera kuphedwa pomwe apo.” Osakalowelera ku chophimba chimenecho. Chophimba chimenecho ndi cha munthu mmodzi. Uthenga umenewo ndi umodzi. Mukuona? Mu kachisi, munthu mmodzi ankapita kamodzi pa chaka, atadzedwa ndipo atakonzeka kuti azikalowamo; osati kuti akatulutseko Mawu, koma kuti akapereke nsembe magazi. Ngakhale kukayenda mmenemo pamaso pa Iwo, mmodzi yekha. Munthu wina aliyense amafako. Mukuona?

<sup>157</sup> Iwo akumafa mwauzimu lero. Ichi ndi chophimba chauzimu. Mukuona? Chijachi chinali chophimba chachirengedwe. Ichi ndi chophimba chauzimu. Mukuona? Iwo akupitirirabe kumayenda kuseri kumeneko, iwe ukhoza kuwauza iwo. “O, ine ndikudziwa! Ine ndikudziwa zimenezo, koma ine . . .”

Ine ndinati, “Pitirirani, ziri bwino, izo zikungolankhula . . .” Inu mukukumbukira, mliri wotsiriza ku Igupto unali imfa, kusanachitike kutulukako. Mliri wotsiriza pa dziko lapansi ndi imfa yauzimu, kusanachitike kutulukako. Kenako iwo adzawotchedwa ndi kubwezeretsedwanso kukakhala fumbi, ndipo olungama azidzayenda pa maphulusa awo. Koma chinthu chotsiriza ndi imfa yauzimu, powakana Mawu.

<sup>158</sup> Tsopano zindikirani, Mulungu anachenjeza kuti munthu aliyense asayerekeze kumutsatira Mose kupita mu chophimba cha Moto. Mose anali woti aziphimbidwa, iye amayenera kuti azitulukira kumeneko. Mose ankalowako ngati Mose, ankalowa mu Lawi la Moto ili; ndipo pamene iye amabwererako, iye amakhala ataphimbidwa. Pakuti, iye amapita Kumeneko, mwa miyambo yake, miyambo ya akuluakulu. Iye anali *atawona* Lawi la Moto, koma tsopano iye akukalowa *mu* Lawi la Moto. Mukuona? Ameni! Ndipo iye amatulukako, ataphimbidwa. Mawu a Mulungu mwa munthu, ataphimbidwa! Apa iye amabwera akutuluka, o, mai, ine ndikukhoza kuziwona izo. Anachenjeza kuti aliyense asayerekeze izo, palibe amene angatsanzire Izo. Inu kulibwino musatero. Mukuona? Ngakhale wansembe kapena munthu woyera, aliyense yemwe anali, kadinolo, bishopo, china chirichonse, chikayesera kupita mu chophimba chimenecho, chimafa. Mulungu anawachenjeza iwo. Ife sitimakhala ndi zotsanzira.

<sup>159</sup> Mawu Ake amawululidwa kwa mmodzi. Iwo nthawizonse akhala akutero, mneneri amabwera ndi Mawu a Ambuye, m’badwo uliwonse, nthawi zonse, kutsika kudutsa Lemba. Mawu amadza kwa mmodzi. Mu m’badwo uliwonse, chimodzimidzi, ngakhale mu mibadwo ya mpingo, kuyambira kwa woyamba womwe mpaka kwa wotsiriza. Enawo ali ndi malo awo awo, izo nzoona, zindikirani, koma muzikhala kutali ndi Lawi la Moto ilo. Mukuona? Ndi phunziro bwanji limene ife tikuphunzira apa! Mwaona, aliyense ankafuna kuti akhale Mose, ndipo aliyense . . .



160 Inu mukukumbukira zimene Datani ndi iwo ananena uko? Iwo anati, “Tsopano, Mose, dikira apa miniti chabe! Iwe ukudzitengera wekha kwambiri, mwaona. Tsopano, aliponso anthu ena pano omwe Mulungu wawaitana.”

161 Izo ndi zoon. Iwo, mmodzi aliyense, amatsatira mwabwino nthawizonse pamene iwo anali kutsatira, koma pamene wina anayesera kuti adzikweze ndi kutenga malo a Mulungu amene Iye anamupatsa Mose, yemwe anali wokonzedweratu ndi wodzozedweratu ku ntchito imeneyo, kuyesera kuti aitenge iyo, moto unatsika pansu ndipo unadzatssegula nthaka ndi kuwamezera iwo mmenemo. Mukuona? Mukuona? Muzisamala. Mukuona? Mungokhala Mkristu wabwino, waumulungu wa Mulungu, kumakhulupirira Mawu. Mukuona? Kumakhala kutali ndi Lawi limenelo. Ndi phunziro bwanji!

162 Mulungu anali atawonekera koyamba kwa Mose mu chitsamba chonyeka, Mulungu anali ataphimbidwa mu Lawi la Moto. Tsopano mveterani mwatcheru kwenikweni tsopano kwa miniti. Mulungu, poyamba anabwera kwa Mose, Iye anaphimbidwa. Mulungu anali mu Lawi la Moto, amabisala kuseri mchitsamba, mwaona; monga kuseri kwa zikopa, mwaona, kuseri kwa mpando wachifundo pa guwa. Mukuona? Iye amaphimbidwa. Iye nthawizonse amaphimbidwa. Ndipo pamene Iye anabwera kwa Mose, Iye anali mu Lawi la Moto, ataphimbidwa mu Lawi la Moto. Koma apa, pamaso pa anthu, Mulungu anamutsimikizira iye ndi Lawi la Moto lomwelo. Mukuona? Mose anati. . .

163 Tsopano penyani. Kodi inu mukuwerenga? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukulola malingaliro anu kuti achokepo? Kodi mungatero inu? Kodi. . . “Iye amene ali ndi makutu, msiyeni iye amve.” Mukuona?

164 Pamene Mulungu anawonekera kwa Mose, zinali mu Lawi la Moto, pamene Iye anamuitanira iye ku utumiki wake. Ndipo Mose anabwera ndipo anadzawauza anthuwo za izo. Iwo samatha kukhulupirira izo, komabe iye amachita zozizwitsa ndi zinthu. Koma, nthawi iyi, Iye mowonekera, mwasayansi anawonekera ndipo anatsimikizira utumiki wa Mose kuti anali Mulungu yemweyo amene analankhula ndi iye, chifukwa Iye anawonekera mmawonekedwe a Lawi la Moto ndipo anadzayatsa moto phirilo. Ndipo Ilo linadzabwera kwa Mose mu chisamba, linalankhula ndi iye. Chabwino.

165 Kuwonekera koyamba kwa Mulungu, kwa Mose, mu chitsamba chonyeka, chophimba. Pamaso pa anthu, Mulungu anaphimbidwanso ndipo anadzamutsimikizira Mose, mwa chophimba, pa kudziphimba Yekha ndi Moto womwewo, Lawi la Moto lomwelo linatsika. Kuchokera—kuchokera pamenepo. . . Kuchokera kwa iwo, kuti iwo azingomva Mawu a Mulungu okha. Inu mukumvetsa izi? Mawu okha, iwo amamva Liwu Lake. Pakuti, Mose anali, kwa iwo, Mawu amoyo. Mose! Mwaona,

Mulungu anali atatsimikizira kwambiri Mawu amenewo kwa Mose! Mwaona, Mose anati... Mulungu ananena kwa Mose, “Upite uko. Ine ndikakhala ndi iwe. Iye ali... Palibe chimene chiti chidzaima pamaso pako. INE NDINE YEMWE NDIRI.”

<sup>166</sup> Mose anabwerako, ndipo anati, “Inu mukhoza kusakhulupirira izi, mwinamwake, koma Mulungu wawonekera kwa ine mu Lawi la Moto ndipo Iye wandiuza ine zinthu izi.”

<sup>167</sup> “O, ife tiri nazonso zinthu za mtundu umenewo zikuchitika.” Farao anati, “Bwanji!” Abusa a Farao anati, “Chabwino, inu muli ndi matsenga otchipa. Bwanji, ine ndiri nawo azamatsenga kuno amene angathe kusandutsa njoka kukhala... ndodo—ndodo kukhala njoka. Bwerani kuno, azamatsenga.” Ndipo iwo anabwera kumeneko ndipo anadzachita chinthu chomwecho.

<sup>168</sup> Mose ankadziwa. Panalibe kanthu kalikonse kanamuvutitsa iye. Ndi otsanzira angati amene iwo anali nawo, sizinapange kusiyana kulikonse. Mose anangoima njii. Chinthu choyamba inu mukudziwa, izo zinakwawa pamenepo kwakanthawi, ndipo, molunjika, njoka ya Mose inangodya zonse za izo. Mukuona? Bwanji? Monga atumwi aja, iwo samatha kuwafotokoza Iwo. Mose sankadziwa momwe Mulungu akanadzachitira izo, koma Iye anali woti azichita izo.

<sup>169</sup> Kumbukirani, Iye anati Ayane ndi Yambre adzabwereranso mu masiku otsiriza, mwaona, kutsanzira. “Ndipo adzanyenga Osankhidwa omwe ngati nkotheke,” Mateyu 24:24. Mukuona? Ndendende basi zinthu zomwezo, kudzachita mtundu womwewo wa zozizwitsa ndi chirichonse. Mupenye Mawu amenewo! Mupenye Mawu amenewo! Munthuyo amati amachita zozizwitsa ndipo akufunabe kuti azikhulupirira kuti alipo Amulungu atatu, ndipo pali mitundu yonse iyi; inu muchokeke kwa mtundu umenewo. Ife tikudziwa izo—izo nzolakwika, mwaona, kulibeko chinthu choterocho. Mukuona? Mawu, Mawu aliwonse, Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa ya Mulungu! Genesis, Mawu amodzi! Cha apa, anati, “Musachotsepo kapena kuwonjezerapo mawu amodzi.” Mwaona, Iwo ayenera kukhala Mawu omwe aja. Mukuona?

<sup>170</sup> Zindikirani, anthuwo anawona chinachake chimene chinali chitachitika. Mose anali ataphimbidwa ngati... Iye anali mneneri, ndipo Mulungu anali atawatsimikizira Mawu Ake tsopano, anapita kumeneko. Ndipo iye anawona zizindikiro ndi zodabwitsa. Ndiyeno, chabwino, anthu awa anadzapatula kwa iwoeni, mpingo. Mwaona, *mpingo* umatanthauza “oitandidwa atuluke.” Mukuona? Iwo atatha kuitandidwa atuluke kuchokera mdziko ndipo nadzakhala anthu, mwaona, kenako Mulungu anadzilola Yekha kuti adziwike kuti Iye anali Lawi la Moto lija. Iye anatsimikizira uthenga wa Mose. Mukuona? Iye anali Lawi la Moto. Iwo akanajambula chithunzi cha Ilo, ine ndikuganiza, ngati iwo akanakhala ndi makamera, chifukwa ilo lonse linali pa Moto. Koma iwo—iwo anatsimikizira zimenezo, Mulungu

kutsimikizira kuti Uthenga unali wolondola. Uthenga unali uli pafupi, chirichonse chinali, iwo anali oti akhala ndi kutuluka pamenepo. Anamuphimba mneneri Wake kwa anthu otuluka awa.

<sup>171</sup> Anthuwo, akuganiza, anawona kuti chinachake chamuchitikira iye. Iye anali tsopano wosiyana ndi a Israeli onsewo. Iye anali wosiyana, uthenga wake unali wosiyana, iye anali wosiyana ndi ansembe, iye anali wosiyana ndi chirichonse. Mwaona, iye anali munthu wosiyana. Anthuwo anawona kuti chinachake chinali chitachitika. Mulungu anali atadziphimba Yekha mwa mneneri Wake, kuti akalankhule Mawu Ake kwa iwo. Ndizo zimene Iye anali atachita. Mose anali Mawu amoyo aja kwa anthuwo, ataphimbidwa ndi Lawi la Moto, kulankhula za chimene chikanati chidzaphimbidwe mtsogolo kuseri kwa zikopa za katumbu. Mukuona?

<sup>172</sup> Mawu ankayenera kubwera kuchokera kwa Mose, poyamba. Mukuona? Mose anali ndi Mawu. Iwo analembedwa ndi Mulungu, panalibe aliyense amene akanawatanthauzira Iwo, Mose amayenera kuti awatanthauzire kaye Iwo, poyamba. Ndi chifukwa chake iye amaphimba nkhope yake, chifukwa iye. . . Kodi inu mukuziwona Izi? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Mukuona?

Ndi Izi *apa*. [M’bale Branham akunyamula Baibulo lake—Mkonzi.] Ife tikhoza kulitenga Ilo, kulinyamula Ilo, ndi chirichonse kumeneko, koma Ilo liyenera kuti liwululidwe. Pofuna kuti awulule, Mose amachita kukhala Mulungu kwa anthuwo.

Inu mukuti, “Zimenezo ndi zamkhutu.”

<sup>173</sup> Bwanji, Iye anamuza, mpaka anamuza Mose, Iyemwini, “Iwe ukakhala Mulungu, ndipo Aroni akakhala mneneri wako! . . . ? . . .” Mukuona? Kotero apo Iye anabwera, mwaona, Iye amachita kudziphimba Yekha, chifukwa Mulungu nthawizonse amakhala kuseri kwa chophimba. O, mai! Kodi inu mukuziona Izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Mulungu amabisala kwa anthu.

<sup>174</sup> Anati, “Atate, Ine ndikukuthokozani Inu, Inu mwazibisa Izo kwa anzeru ndi aluntha, ndipo mwaziululira Izo kwa makanda, kwa iwo amene akufuna kuti aphunzire.” Mukuona?

<sup>175</sup> Mulungu amabisala kuseri kwa chophimba. Mose amaphimba nkhope yake. Mose anali Mawu amoyo ataphimbidwa pamenepo. Anthu amawona Lawi la Moto limenelo, anati, “Tsopano ife takhutitsidwa.” Mukuona? “Musiyeni Mose azilankhula.” Mukuona? “Musamulole Mulungu alankhule, kuwopa kuti tingafe.” Mose anayenda mpaka anakalowa mu Lawi la Moto limenelo. Mukuona?

<sup>176</sup> Ndipo anati tsopano, Iye anati, “Tsopano Ine—Ine sindimalankhulanso ndi iwo panonso monga chonchi. Ine

ndiwapatsa iwo mneneri.” Mukuona? Ndipo umo ndi momwe nthawizonse Iye amachitira izo. Mukuona? Anati, “Tsopano asiye ni iwo apite kumeneko.” Koma mneneri uyu ayenera kukhala ndi Mawu awa. Ngati iye waphimbidwa ndi mwambo, Mulungu sanamutume iye. Ngati iye waphimbidwa ndi Mawu, Mulungu awatsimikizira Iwo. Mulungu amatanthauzira Mawu Ake Omwe. Mose amawalankhula Iwo; Mulungu amawathanthauzira Iwo. Ameni.

<sup>177</sup> Mose amati, “Ambuye akuti chakutichakuti!” Ndipo Ambuye amachita basi zimene Iye wanenazo. Izo zimawapanga Iwo kukhala owona.

<sup>178</sup> Tsopano Iye anati, “Tsopano, Mose, iwe ukumvetsa. Anthuwo akumvetsa tsopano. Wawona, Ine ndakuwonetsa iwe, Ine ndakutsimikizira iwe.” Mulungu anali atadziphimba Yekha mwa mneneri uyu, kuti akalankhule Mawu Ake kwa anthuwo. Mose anali Mulungu wamoyo kwa iwo, Mawu a moyo a Mulungu akuwonetseredwa. Ndicho chifukwa chake nkhope yake imaphimbidwa. Mukuona?

<sup>179</sup> Ndipo kodi inu mukudziwa chinthu chomwecho mwa Mkhristu woona akuphimbidwa lero, kwa osakhulupirira? Iwo akawawona akazi amenewo ali ndi tsitsi lalitali ndi zinthu, amati ndi... “Tamuwonani wa modelo yakale uyo.” Akazi amene amapinda tsitsi lawo kumbuyo, amati, “Ali ndi tayara lakuphwa, amangilira tayara la sipeya pamenepo.” Mwaona, Zonsezo zaphimbidwa. Iwo ndi akhungu. “O,” iwo amati, “Ine ndiri ndi Ph.D, L...” Ine sindikusamala zimene inu muli nazo, inu ndinu mbuli apobe kwa Mawu. Kulondola ndendende. “O, izo, ndicho chinachake basi chaching’ ono. Ine...” Muzitenga maphunziro ang’ono ang’onowo poyamba.

<sup>180</sup> Nanga bwanji anthu amene amanena kuti iwo ndi ophimbidwa mu Kukhalapo kwa Mulungu, ndi kumalalikira mwambo wina wa tchalitchi? O, chifundo, kalanga! Amene amawonjezera ndi kuchotserapo, ndi china chirichonse, pobailamo zinthu zawo zawo ndi malingaliro awo awo, ndipo osati Mawu a Mulungu, mwaona, ndi chophimba cha mtundu wani? Amene ali ndi chophimba cha zachipembedzo. Mulungu waching’amba pakati chophimba chimenecho!

<sup>181</sup> Iwo anati, “Palibepo chinthu choterocho ngati aneneri. Palibepo chinthu choterocho, mu masiku otsiriza ano, ngati atumwi ndi aneneri. Palibepo chinthu choterocho ngati machiritso Auzimu. Palibepo chinthu choterocho ngati apenyi, panonso. Palibepo chinthu choterocho ngati Marko 16 kuti akukwaniritsidwa. M’badwo wa atumwi unatha.” Iwo anawaphimba Iwo kwa anthu. Koma Mulungu anabwera pamenepo ndi Moto Wake wa Mzimu Woyera, ndipo anadzaching’amba chinthu chimenecho kuchokera pamwamba mpaka pa-... [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Mulungu anang’amba chophimbacho.

182 Mose anali chophimba, Mawu amoyo a Mulungu ataphimbidwa kuseri kwa mnofu wa munthu. Lawi la Moto linali mwa Mose, zoonu, kulankhula za zomwe zimati zidzaphimbidwe mtsogolo kuseri kwa zikopa, inu mukuona.

183 Tsopano, awo, Mawu, Mawu anabweretsedwa, kenako Iwo anadzalembedwa, kenako Iwo anadzaikidwa kuseri ndipo anali ataphimbidwabe, pakuti Mulungu nthawizonse amakhala mu Mawu amenewo. Ameni! Iyeyo ndi Mawu, nthawizonse. Iye anali mu Mawu amenewo. Ndi chifukwa chake Mawu amenewo amayenera kuti aziphimbidwa.

184 O, m'bale, mlongo, kodi inu mukuzimvetisa Izi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Taonani! Kodi inu simukuwona? Iwo akhala ophimbidwa kudutsa mu mibadwo iyi, molingana ndi zimene Mulungu ananena, ndipo Iwo adzatsegulidwa mu masiku otsiriza, Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zimenezo zidzamatulidwa, ndipo Chinthu chathunthuchochidzafika powonekera kwa anthuwo, zomwe zakhala zikuchitika nthawi yonse. Ora la Uthenga wa mngelo wa chisanu ndi chiwiri, zinsinsi zonse za Mulungu ziyenera kudziwitsidwa mwa Eliya ameneyo, ora lotsiriza lino; momwe Khristu watulutsidwira kunja kwa mpingo Wake, Mwana wa Mulungu; momwe Iye akuwululidwira ngati Mwana wa munthu kachiwiri; momwe Mpingo uti udzaikidwire mu dongosolo, ndi chirichonse cha tsiku lotsirizalo, popanda kachikhulupiriro, popanda chipembedzo, basi mwamtheradi Mawu kumakhala moyo mwa munthu payekha. "Ine ndidzamtenga mmodzi, ndi kumusiya wina. Ine ndidzamtenga *uyu*, ndi kumusiya *uyo*." Mukuona? Pangokhala basi... Palibepo zingwe, palibepo zipembedzo, palibepo zomangirira kapena kalikonse; ndi mtima wokhala ndi Mulungu, ndipo Iye yekha. Mukuona?

185 Zindikirani, kuphimbidwa mu mnofu wa munthu. Mose ali ndi Mawu amenewo, akulankhula zomwe mtsogolomo zikanadzaikidwa kuseri kwa chikopa cha katumbu. Koterokuti... Chomwechonso ali Khristu Mose wathu. Khristu ndiye Mose wathu. Iye anali Mulungu ataphimbidwa mu mnofu wa munthu, kuphimbidwa mu umunthu, mu thupi. Izo nzoona. Ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye amaphimbidwa ndi zikopa za akatumbu. Iye amaphimbidwa. Ndipo nthawi iyi Iye akuphimbidwa mwa Munthu. Mukuona? Tsopano zindikirani, "yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," analonjeza Mawu Ake kwa m'badwo *uno*. Iye akadali Khristu, Mawu olonjedwa kwa m'badwo uno, ataphimbidwa mu mnofu wa munthu. Mawu ndi Mulungu.

186 Kudzozako ndi munthu. Mawu akuti *Khristu* amatanthauza wodzozedwayo, mwaona, "wodzozedwayo." Ndiye, Mose anali Khristu mu masiku ake, iye anali wodzozedwayo. Yeremiya anali Khristu mu masiku ake, ali ndi gawo la Mawu a tsiku limenelo.

<sup>187</sup> Koma pamene Yesu anabwera, Iye anabwera ngati Muomboli Wodzozedwa Uyo; ndipo zimenezo zinali zonse ziwiri Mose ndi zonse zimene zinali mwa Mose, ndi Mawu onse, ndipo Umulungu wonse mu thupi unali mwa Iye. Ndicho chifukwa chophimba chonsecho cha mkachisi chinang'ambika, ndipo mpando wachifundo unabwera pa mbalambanda, Iye anali Wodzozedwayo.

<sup>188</sup> Zindikirani tsopano, chophimba mu mnofu wa munthu, Mawu olonjezedwa kwa m'badwo uno ayenera nawonso kuphimbidwa. Zindikirani. Mamembala a mpingo okonda tchimo ndi ochimwa sangathe kuwawona Iwo chifukwa cha chophimba cha umunthu.

<sup>189</sup> Ndi chifukwa chake iwo samatha kumuwona Iye. “Bwanji, Iye ndi munthu. Kodi Iye anachokera kuti? Kodi Iye ali ndi khadi la chiyanjano lake liti? Kodi Iye ndi wa tchalitchi chiti?” Ine ndikufuna kuti ndilankhule pa zimenezo usikuuno, “Kodi Iye ndi wa tchalitchi chiti?” Mukuona? Ndipo kotero, mwaona, tsopano, “Kodi Iye ndi wa tchalitchi chiti, liti—gulu liti? Kodi Iye anali ndi sukulu iti? Kodi Iye anawapeza kuti maphunziro Ake? Chabwino, Munthu uyu anabadwa, molingana ndi mwambo, kapena molingana ndi—mbiri ya Iye kuzungulira kuno, Munthu uyu anabadwa kunja kwa chikwati choyera. Bwanji, Iye, ndithudi, Iye ndi wa mdierekezi. Mwaona, Iye ndi—Iye ndi wa mdierekezi. Iye anabadwa kunja kwa chikwati choyera, ndipo Yosefe anangomukwatira iye pofuna kumutetezera iye kuti asagendedwe, chifukwa iye anali wachigololo. Ndipo Munthu ameneyo angabwere ndi kumadzatiuza ife ansembe zoti tizichita?”

<sup>190</sup> Ndipo apo panali Mulungu ataima pamenepo, akuwulula Mawu amenewo, akulira, “Mulungu wanga, chifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?” Nyimbo zomwezo zimene iwo ankaimba mu kachisi, zimene Davide anawakonzera iwo zaka zapitazo, zokhudzana ndi Khristu. “Mafupa Anga onse iwo akuwonekera pa Ine. Iwo apyoza manja Anga ndi mapazi Anga.” Ndipo apo iwo anali ataima pamenepo, akuimba imeneyo, ndipo Munthu yemweyo anali akufa pa mtanda. Ndipo pamene iwo anatsiriza ndi . . .

<sup>191</sup> Pamene Iye anafa, Mulungu Wakumwamba anatsika pansu, monga Iye anachitira pa Phiri la Sinai, ali ndi Moto Woyera, ndipo anadzawotcha chotchinga cha mkachisi icho kuchokera pamwamba mpaka pansu, anaching'amba icho pakati. Ndipo kodi iwo akanachita chiyani? Kumayang'ana pomwe apo kuchokera pa zenera la mkachisi, pa Kalvare, ndipo pamenepo panali Mulungu ali pa mbalambanda, Nsembe.

<sup>192</sup> Koma iwo sakuziwonabe Izo, lero. Mulungu mu tsiku lotsiriza lino wang'amba miyambo imeneyo, ndipo wawabweretsa Mawu a m'badwo uno pa mbalambanda, ndipo iwo sakudzawabe Izo. Iwo sakuwadziwa basi Iwo. Izo—izo ndi

zophweka kwambiri. Mwaona, izo ndi zophweka kwambiri. Izo ndi zotalikirana kwambiri ndi zinthu za dziko lapansi.

<sup>193</sup> Ine ndinalalikira tsiku lina pa kusonkhana kwinakwake, za, “Kukhala nati.” Limodzi la masiku amenewa ine ndikufuna kuti ndidzalankhule pa zimenezo, “Kukhala nati.” Ndife tonse manati a winawake, kotero—kotero ine ndidzakhala mmodzi wa Khristu. Paulo anati iye “ankawerengedwa kuti anali chitsiru.” Ndithudi, iwe uyenera kukhala. Mwaona, izo zimatengera nati kuti izigwire zinthu pamodzi. Mukuona? Uko nkulondola.

<sup>194</sup> Kotero zindikirani chophimba, mnofu wa munthu. Ayi, tsopano, anthu okonda tchimo samatha kuwona zimenezo. Anthu awo amwambo achipembedzo, iwo samatha kuwona zimenezo, chifukwa Iye anali munthu. Bwanji? Mnofu wa munthu uwo umamubisa Mulungu.

<sup>195</sup> Tsopano, ngati Iye anali Lawi la Moto lalikulu limene linatsika, mwaona, Lawi la Moto lalikulu linali litatsika ndipo linawasonyeza iwo icho chimene Iye anali, kuti Iye anali Lawi la Moto lalikulu ili, iwo mwina akanakhulupirira zimenezo; ngati Yehova akanapita kumeneko.

Koma inu mukuona chimene Iye anachita, ndi cholinga chakuti Iye adzawalambalale onse ophunzira, anthu anzeru awo, Iye anangodziululira Yekha monga Iye anamulonjezera Mose, mwaona, “Ine ndizilankhula ndi iwo kudzera mwa Mneneri.” Ndipo Iye anali Mwana wa munthu, Mneneri. Ndipo ena a iwo anazindikira Zimenezo, pafupifupi peresenti imodzi pa zana ya mazana a mu dziko, iwo anakhulupirira Iwo; ena onsewo sanakhulupirire. Koma, Iye anali, chimodzimodzi basi.

<sup>196</sup> Koma apo panali Mulungu Wamphamvu ataima pa mbalambanda, Mpando Wachifundo! Iye anali kufa ana Ake Omwe akuti. . . Ana Ake Omwe pamenepo, akuti, “Ife sitikumufuna Iye! Tiribe naye ntchito Iye!” Anamulavulira Iye.

<sup>197</sup> Choimira, kumbuyo uko, pamene Davide ankachoka mkachisi, mfumu yokanidwa. Anapita kudutsa mu msewuwo, ndipo munthu wamng’ono, wokalamba wolumala akukwawa pamenepo, sanankonde konse iye, anamutcha iye “wachinyengo wachikale” kapena chinachake, kumulavulira pankhope pake pomwe. Ndipo apo mlonda anasolola lupanga, anati, “Kodi ine ndingausiye mutu wa garuyo ukhale pa iye; atalavulira pa mfumu yanga?”

<sup>198</sup> Davide anati, “Msiyeni iye yekha, Mulungu wamuuza iye zimenezo.” Ndipo Davide mwinamwake samadziwa zimene iye amanena. Anapita pa phiri, akuyang’ana mmbuyo, akulira.

<sup>199</sup> Zaka eyiti handiredi kuchokera pamenepo, Mwana wa Davide anali kukwera phiri lomwelo, akuyang’ana kumeneko, akulirira Yerusalemu, Mfumu yokanidwa. Ndipo iwo analavulira pa nkhope Yake.

200 Kodi inu simukuwona? Ndi chinthu chomwe chomwecho. Mukuwawona Mawu awo akubwera chotsika, akutsatira chotsika lero? Nthawizonse amakanidwa ndi ambiri, mwaona, ndipo amakhulupiriridwa ndi apang'ono.

201 Tsopano, onani, iwo samatha kuwakhulupirira Iwo. Agriki amenewo, iwo samatha kumuwona Iye, Iye anali ali mu kachisi Wake wa umunthu. “Bwanji,” iwo anati, “dzina la munthu uyu ndi Yesu; Iye ndi wochokera ku Nazareti.”

202 Tsopano, iwo amakhala ndi dzina limodzi lokha kumeneko mmasiku amenewo. Monga, “John, Jim,” iwo amati, “John waku Jeffersonville, Jim waku New Albany,” kapena chinachake monga choncho, inu mukuona.

203 Iye anati, “Uyu ndi Yesu waku Nazareti. Izo zimakhulupiriridwa mwawamba kuti amayi Ake anapatsidwa pakati ndi msilikari.” Mukuona? Ndiyeno zimenezo ndi ndendende zimene iwo ankakhulupirira. Zedi! Ndipo anati iwo amati, tsopano, “Ndipo uyu ndi Yesu waku Nazareti.” Inu mukuona? “Kodi Iye ndi ndani?” Mwaona, iwo samatha kumvetsa Zimenezo.

204 Koma, bwanji, Mawu awa a tsiku limenelo, pamene Iye anali kulalikira, anati, “Fufuzani Malemba. Mwa Iwowo inu mukuganiza kuti inu muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Iwo akuchitira umboni Yemwe Ine ndiri. Ngati inu simungathe kundikhulupirira Ine; mundiiwale Ine, ngati chophimba, muwakhulupirire Mawu amene akutulukawo. Awiri ndi mboni,” Iye anati, “Ine ndikulankhula ndipo Atate akumandilankhulira Ine.” Amen. Izo nzoona.

205 Ine ndikulankhula za Mawu a tsiku la lero, ndipo Atate akuwatsimikizira Iwo. Tsopano kodi uwo ndi umboni kwa inu? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi umenewo, mwaona. Umo ndi mmene ziri zoti zidzakwaniritsidwire.

206 Zindikirani mu Akorinto Wachiwiri tsopano, a...mu Akorinto Wachiwiri, mutu wa 3, ndime ya 6, kachisi wakale ankasungira Mulungu kuseri kwa zikopa zakale, kuchokera kwa Ayuda. Pamene chophimba chakale chinang'ambidwa, apobe Ayuda... anachititsidwa khungu kwa Yemwe Iye anali, ndi Yemwe Iye ali panobe. Ndiyeno Pentekoste inawulula Yemwe Mulungu woona ndi wamoyo anali, pamene chophimba chija chinadulidwa pawiri, ndi Mulungu, kuchokera pamwamba. Nchifukwa chiyani chophimba chimenecho chinachita zimenezo? Nchifukwa chiyani icho chinachita izo?

207 Nchifukwa chiyani kwabwera Uthenga woterowo lero kuti udzachite zimene Iwo wachitazi? Nchifukwa chiyani Iwo wabwera? Bwanji?

208 Panali winawake yemwe ankati andiitane ine, tsiku lina kuno osati kale litali, ankafuna kuti adzatsutsane nane zokhudza—m'badwo wa mpingo, kuti, “Mulungu amakhala mu



mpingo Wake woyera,” ndi zinthu monga choncho. Ndipo ine ndinadzapeza kuti anali mlaliki wina wa mkazi, ndipo ine ndinangoiwala za izo. Mwaona, ngati akanakhala mwamuna wina zikanakhala zabwino bwino, izo zikanakhala zosiyana. Koma, kotero, koma ndi cha ntchito yanji kuti ndikalumphire ku dziko lina uko, pamene ine ndasiya msonkhano kuno kuti ndichite zimenezo, inu mukuona? Kotero ine ndinangowasiya iwo okha. Wakhungu akamatsogolera wakhungu, iwo—iwo onse amakagwera mdzenje.

<sup>209</sup> Kotero, kotero tsopano mu m’badwo uno, pamene chophimba cha chipembedzo chakale ndi mwambo zang’ambidwa, kwa Mawu a Mulungu, kuti Iwo akhoze kuwonetseredwa! Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mwambo umati, “Zinthu zonsezo zinatha.” Mulole Izo zilowerere pang’ono pokha. “Zinthuzo zinatha.” Koma, mu tsiku lino lotsiriza, chophimba cha mwambo icho chang’ambika pakati, ndipo apa pakuima Lawi la Moto. Mukuona? Ndi Uyu apa, akuwonetsera Mawu a tsiku la lero. Chophimbacho chang’ambika.

Tsopano, dziko, panobe silikuwakhulupirira Iwo. Ziribe kanthu kuti ndi chiyani, iwo sakuwawona Iwo. Iwo sakuwawona Iwo. Iwo sanatumizidwire iwo.

<sup>210</sup> Kumbukirani, Mwana wa Mulungu sanawululidwire kwa Sodomu; anali atumiki awiri aja. Izo nzoona.

<sup>211</sup> Koma, uyu, Mulungu Mwiniwake mu mnofu wa munthu anawululidwa kwa Abrahamu, Wosankhidwayo. Ndipo penyani zimene Iye anachita kuti adziwulule Yekha. Ndipo tsopano Abrahamu anadziwa, pamene Iye anadziwa zimene zinali mmalingaliro a Sarah kumbuyo kwa Iye, iye anati, anamutcha Iye, “Elohim! Wantchito Wanu . . .”

<sup>212</sup> Zindikirani tsopano, kuti zidzathe kuwonetseredwa. Mawu akhala ali ndi chophimba pa Iwo zaka zonsezi, kwa anthu, “Izo sizingatheke.”

<sup>213</sup> Inu mukukumbukira ulaliki umene ine ndinalalikira mmawa umene ine ndinkachoka pano nthawi yoyamba, wa Goliatu ndi Davide? Ine ndinati, “Tayang’anani pa wotsutsa kunja uko, akunena kuti ‘masiku a zozizwitsa anatha.’”

Mudzawawone matepi amenewo pamene iwo azibwera, mudzaiwone imodzi iliyonse, momwe Iwo akubwerera momveka ndi momveka; ngati inu muli ndi makutu omvera, mwaona, maso openyera.

Chiyani? Ine ndinati, “Apo pakuima dziko lalikulu la zachipembedzo kunja uko, kumanena mu m’badwo wa sayansi uno, kuti izo sizingatheke.” Koma ine ndinati, “Mulungu . . .” Mu Kuwala kuja, Icho chisanajambulidwe nkomwe, koma kamodzi; chinali chisanajambulidwe pamenepo. Izo zinali uko pa mtsinje; iwo asanajambule konse chithunzi cha Iko. Mukuona? Ine

ndinati, “Iye anandiuza ine kuti izo zidzachitika; Iye adzapanga kuitana ndipo iko kudzasesa mafuko.”

<sup>214</sup> Ndipo ngakhale kwa Doctor Davis, anati, “Iwe, ndi maphunziro a sukulu ya galamala, unalekezera mu giredi seveni, uzidzapempherera mafumu ndi otchuka, ndipo udzayambitsa chitsitsimutso chimene chiti chidzasese mafuko?”

Ine ndinati, “Izo ndi zimene Iye wanena.”

<sup>215</sup> Ndipo izo zachitika. Mukuona? Mwaona, izo zachitika. Ndicho chinthu chake cha izo, izo, Iye samasowa wotanthauzira. Iye wazichita izo. Mwaona, Iye anazichita kale izo, izo zikuzitanthauzira zokha, mwaona, akuitana Osankhidwa Ake, mwaona, kuchokera—kuchokera ku mayendedwe onse a moyo. Tsopano izo zawonetseredwa.

<sup>216</sup> Ine ndinanena kuti Davide anaima uko, wamng’ono, mnyamata wowonda, wopanda nyama ndi nsana wake wonse utapindikira mkati, ali ndi legeni mdzanja lake. Ndipo, bwanji, Sauli anamuyang’ana iye, mkulu wa gulu la azitumiki, anati, “Bwanji, iwe, ndiwe wosaphunzitsidwa nkomwe!” Iye anati, “Ndiwone ngati ine ndingathe kukupatsa iwe Ph.D. kapena china.” Anaika chida ichi pa iye, icho. . . Iye anapeza kuti icho sichinamukwanire munthu wa Mulungu.

<sup>217</sup> Anati, “Mundivule ine chinthucho.” Anati, “Ine sindikudziwa kanthu za icho.” Anati, “Mundisiye ine ndipite momwe ine ndikudziwira, chimene ine ndinaumenya nacho mkango, chimene ine ndinamenya nacho chimbalangondo.” Iye anali ngati wa kuthengo. Iye anati, “Mundisiye ine ndipite mwanjira iyi.”

<sup>218</sup> Ndipo Goliati wokalamba uyu anati, “Kodi inu mukunditumizira ine garu kuti adzamenyane ndi ine?” Anati, “Ine ndikutunga iwe pa nsonga ya nkondo wanga ndi kukapachika nyama yako pamwamba apo ndi kusiya mbalame kuti zikadye iyo.”

<sup>219</sup> Davide anati, “Iwe ukukumana nane ine ngati Mfilisiti, ndi chida ndi nthungo, ndipo ine ndikumana nawe iwe mu Dzina la Ambuye Mulungu wa Israeli.” Muwoneni mneneriyo, Davide, anati, “Lero ine ndidula mutu wako kuchokera pa phewa lako.” Ameni! O, mai! Iye ankadziwa chimene iye anali nacho, yemwe iye anali atamukhulupirira, ndipo anali wokakamizidwa kwathunthu kuti Iye anali wokhoza kusunga icho chimene iye anachipereka kwa Iye. Mukuona? Kotero izo zinachitika mulimonse.

<sup>220</sup> Kunena kwakale, “Masiku a zozizwitsa anapita,” makoma agwetsedwa pansu! Yehova akuimabe pa mbalambanda, akuwonetsera Mawu Ake, Uyo wovundukulidwayo. Izo nzoona. Zindikirani.

221 Mpingo wa Amitundu nawonso wachititsidwa khungu kwa chophimbacho, chitatha kung'ambika ndipo chikumuwonetsa Mulungu, chophimba cha zachipembedzo. Motani? Powaphimba Mawu mwa munthu kachiwiri. Zimenezo ndi ndendende zimene Israeli analephera kuti aziwone. Ngati izo akanakhala Mngelo wina kapena chinachake, Israeli akanakhulupirira Izo. Koma pokhala kuti izo sizikanakhala Mngelo, izo zimayenera kukhala munthu. Amen!

Mulungu sangathe kuswa Mawu Ake. Mu masiku otsiriza ziyenera kukhala chinthu chomwecho kachiwiri. Mukuona? Nchiyani chinampangitsa Israeli khungu? Munthu Uja. “Ndiwe Munthu ukudzipanga Wekha kukhala Mulungu.” Ndi chimene iwo anamuphera Iye, ndipo, lero, chifukwa Uthenga unabwera podzera mwa munthu ndipo osati Angelo. Mukuona? Mulungu sangathe kusintha njira Yake, kusintha Mawu Ake. Iye anati Iye samasintha. Mukuona? Zindikirani, analonjeza! Ndipo Amitundu achititsidwa khungu lero monga Israeli anali, chifukwa (chiyani?) chophimba. Mulungu ataphimbidwa mwa munthu, zinampangitsa khungu Israeli.

Zindikirani, zinayamba zamuchititsapo khungu wina. Wina, Iwo adzamchititsa khungu; winayo, Iwo adzamuululira Choonadi. Iwo adzatseka maso a ena, ndi kudzatsegula maso a wina.

222 Taonani, Yesu anaima ndipo anati, “Chabwino, dzina lako ndi—ndi—ndi Simoni, ndipo dzina la abambo ako ndi Yonasi.”

Iye anati, “Ambuye Mulungu!” Mukuona? Fillipi. . .

Iye anati, “Inu munandidziwa liti ine?”

Iye anati, “Tamuonani m’Israeli, mwa yemwe mulibemo chinyengo!”

Ndipo iye anati, “Rabbi, Inu munandidziwa liti ine?”

223 Iye anati, “Fillipi asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe.”

224 Iye anati, “Rabbi, Ndinu Mwana wa Mulungu. Ndinu Mfumu ya Israeli.”

225 Chabwino, apo panaima amenewo apo, anati, “Iye ndi Bezezebule.” Mukuona? Kodi Iwo anachita chiyani? Anatsogola maso a wina, anachititsa khungu a ena. Kodi ansembe anati chiyani? “Bwanji, Munthu ameneyo ndi Bezezebule!”

226 Mkazi wamng'onoyo anati, “Ine ndikudziwa Mesiya akubwera, yemwe akutchedwa Mmodzi Wodzozedwayo. Mwaona, Mmodzi Wodzozedwayo adzadza. Ife sitinakhale nawo aneneri. . . Inu muyenera kuti ndinu mneneri. Koma Mmodzi Wodzozedwayo adzadza. Ife tikumuyembekezera Iye. Ano ndi masiku otsiriza kwa Amitundu. . . kapena kwa Ayuda.” Anati, “Lino ndi tsiku lotsiriza.” Mwaona, onse awiri Asamaria ndi Myuda amayembekezera Mesiya. Mukuona? Anati, “Nthawi

yake ndi ino kuti Iye awonekere. Ife tikudziwa, pamene Iye adzadzaza, Iye adzachita zinthu zimenezi. Iye adzatiuza ife zinthu zimenezi.”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

Maso ake anatseguka; apolisi, ansembe anachititsidwa khungu.

<sup>227</sup> Ndicho chimene Uthenga nthawizonse umachita. Iwo umatsegula maso a ena, umawulula Choonadi kwa ena, pamene Iwo ukuchititsa khungu ena; umakhala ndi tanthauzo la pawiri. Ena akhoza kumutenga Mwana ameneyo ndi kuyang’ana molunjika mwa Iye, ndi kuchita khungu; ena akhoza kutenga Iwo ndi kuchokapo ndi Iwo. Ndiko kusiyana kwake.

<sup>228</sup> Monga izo zimachitikira mu m’badwo uliwonse, Umulungu kuphimbidwa mu mnofu wa munthu. Zindikirani, Iye anatero. Aneneri anali Umulungu, utaphimbidwa. Iwo amakhala Mawu a Mulungu (ndi kulondola uko?) ataphimbidwa mu mnofu wa munthu. Kotero, iwo sanamuzindikire Mose wathu chonchobe, mwaona, Yesu.

<sup>229</sup> Zindikirani ataphimbidwa kuseri kwa zikopa zakale za akatumbu mu kachisi wakale, anali Mawu, anali Mawu akuwonetseredwa pa magome a mwala.

<sup>230</sup> Tsopano, ine ndiyesera kuti nditsirize mu pafupifupi maminiti twente tsopano, ngati ine ndingathe, ndikwanitsa ikamati hafu pasiti leveni. Zindikirani, ngati inu mungazindikire, ine ndatsegula masamba ena apa, inu mukuona, kuwopa kuti...kuwopa kuti ndingadule... kuwupanga iwo kukhala wautali. Ine ndikudziwa kuti mwatenthedwa, mwatopa.

<sup>231</sup> Kuseri kwa kachisi wakale, mu chophimba, kumakhala chiyani kuseri kumeneko? Yehova anali chiyani? Kumabisidwa chiyani kuseri uko? Kodi chophimbacho chinkabisa chiyani? O, aleluya! Kodi chophimbacho chinkabisa chiyani? Ichu chinkabisa Mawu. Chophimba, zikopa zakale za katumbu, amabisidwa, zimabisa Mawu ku maso awo, achirengedwe. Kuseri kumeneko, ukonso, kumakhala mkate woweyula. Kuseri ukonso, kumeneko, kumakhala Ulemerero wa Shekinah. Koma Izo zonse zimabisidwa kwa iwo. Izo zonse zimabisidwa. Ulemerero wonse wa Mulungu umakhala kuseri kwa chikopa chakale cha katumbu, izo nzoona, zonsezo zimakhala zobisidwa kwa diso lachirengedwe.

<sup>232</sup> Ziri chomwechonso lero, panonso. Iwo amatchedwa “gulu la overa odzigudubuza, otentheka,” koma iwo sakudziwa chimene chabisika kuseri uko. Ndicho chimene iwo sakuchidziwa. Mukuona?

<sup>233</sup> Ndiye pamene Mulungu, mu chifundo, anang’amba chophimbacho kuti iwo awone, iwo anali atakutiridwa kwambiri

mu miyambo yawo. . . izo zinali zobisidwabe kwa iwo, ngakhale mpaka tsiku la lero.

<sup>234</sup> Chimodzimidzinso tsopano! Ulemerero, Mphamvu ya Mzimu Woyera, Ulemerero wa Shekinah umene umabwera pa wokhulupirira, tsopano ine ndikutanthauza wokhulupirira weniweni, zimene zimapangitsa ntchito za Mulungu ndi chikhulupiriro kuti zibwere mwa iye, kuti awakhulupirire Mawu a Mulungu, zonsezo ndi zobisika kwa maso amenewo. Iwo amati, “Zinthu zimenezo zinapita.” Inu mukuona, iwo akukhalabe kuseri kwa chophimba.

Inu simuli kuseri kwa chophimba icho panonso, ang’onoang’ono Inu, Mulungu wabwera pa mbalambanda kwa inu.

<sup>235</sup> Tsiku lina, M’bale Fred Sothmann, M’bale Tom Simpson. . . Ine sindikudziwa ngati iye wabwera nkomwe kuno kapena ayi. Ambiri a ife tinali uko ku mpingo wa Baptisti, ndipo mtumikiyo ananena chinachake chimene chimamveka chabwino kwambiri. Tonse a ife tinati, “Ameni!” Aliyense mu tchalitchicho anasolola makosi awo ndi kuyang’ana mmbuyo. Mukuona? Mukuona? Ife tinapeza chinyenyiswa chimene chinabwera kuchokera kuseri kwa Shekinah uko, inu mukudziwa, ndipo ife tinakhala ngati okondwa kumwa zimenezo. Ife tinanena, mwakulankhula kwina, “Zikomo Inu, Ambuye!” Mukuona? Ndipo, pamene iwo anatero, anthu awa anali ataphimbidwa kwambiri iwo anangoseka pa izo. Iwo samadziwa kuti Izo zinali chiyani. Mukuona? Iwo akadali ophimbidwabe. Kotero, alipo ena amene ali mkati ndipo ena ali kunja. Ndipo kotero. . . Koma Mulungu ali pa mbalambanda pathu, atabisika. Chimodzimidzinso tsopano!

<sup>236</sup> Ndiye pamene Mulungu, mu chifundo Chake, anang’amba chophimbacho, Iye anabweretsedwa pa mbalambanda. Koma, iwo anali atakutiridwa kwambiri mu miyambo yawo, Iye anali atabisidwabe kwa iwo.

Chimodzimidzinso tsopano! Ulemerero wonse uwo, wabisidwa, wabisidwa kwa ife mwa Khristu, Mawu, Yemwe ali Kachisi wathu.

<sup>237</sup> O, tsopano, ine ndiyenera kuti ndikumbe pansu mu izi pang’ono pokha. Mundikhululukire ine chifukwa cha kutengeka kwanga mmawa uno, koma, o, ine—ine ndakhala ndikufuna kuti ndidzachipereke ichi kwa nthawi yaitali, ine. . . icho chikungomangika mwa ine. Mukuona?

<sup>238</sup> Zindikirani, Ulemerero wonse umene uli mwa Mulungu uli mu Mawu. Madalitso onse amene ali mwa Mulungu ali mu Mawu. Izo nzobisika, kwa wosakhulupirira, chifukwa cha miyambo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Koma Zonsezo ziri mwa Khristu. Zonse zimene Mulungu anali, Iye *anzitsanulira* Yekha, “kenos,” ndipo zinabwera mwa Khristu; ndipo ife, tinadzalowa mwa Khristu, tiri kuseri kwa chophimba.

239 “Chabwino, ine ndiri mwa Khristu,” inu mumatero. Ndiyeno nkumakhulupirira kuti alipo Amulungu atatu? Kumabatiza mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera”? Kumakhulupirira mu miyambo yonse iyi ndi zinthu zimene inu mukhulupiriramo, za akuluakulu? Ayi, inu mukadali apobe kuseri kwa chophimba. Mukuona? Mubwere mudzalowe mu chophimbacho. Iye, Khristu, ali Mawu.

240 “Motani? Ine sindimakhulupirira mu machiritso Auzimu. Ine sindimakhulupirira mu zozizwitza izi ndi zinthu monga Zimenezo.”

241 Chabwino, inu mukuona, ndinu—inu simuli mkati, mkati mwa chophimba. Inu simukudziwa kanthu za Iwo. Mukuona? Khristu ndi Mawu! Ndipo pamene ife tikukhala mu Mawu, ife tiri mwa Khristu. Ndipo zingatheke bwanji ine kukhala mwa Khristu, nkumamukana Khristu? Anali Iye amene anati, “Sipadzakhala mawu amodzi ati adzawonjezedwe kapena kuchotsedwapo.” Zingatheke bwanji kuti inu muchotserepo ndi kuwonjezerapo, ndiye? Mwaona, izo zikukusonyezani inu chophimba chimene wakuphimbani nachoni inu. Mukuona?

242 Ife kumakhala mwa Iye! Ndiye ife, tikamakhala mwa Iye, ife timakhala ophimbidwabe kwa achipembedzo ndi odzinenera a mdziko. Mwaona, Ulemerero wathu umene ife tiri nawo ndipo nkumamva kukoma, ife tikadali ophimbidwabe kwa iwo akunjawo. Iwo amaganiza kuti ndife “openga, nati,” aponso. Mukuona? Mukuona? Izo nzoona. Koma ife amene tiri muno, mwa Khristu, tinabatizidwira mwa Iye, (Akorinto Woyamba 12), mwa Iye, ife tiri otenga nawo a Ulemerero uwu. Mukuona? Koma osati akunjako; inu mukuyang’anabe mkati, nkumawakana Iwo. Mukuona?

243 Kotero tsopano ife tikuitanidwa kuti tikalowe mwa Iye, kuti tikakhale otenga nawo a zonse zomwe Iye ali. Ife tikuitanidwira kukalowa mwa Iye, zomwe ziri zobisika kwa osakhulupirira, mwa chophimba cha mnofu wa munthu. Mukuona? Iwo akuwudziwa Ulemerero umenewo, iwo amawerenga za Iwo, Iwo uli mu Mawu apa, “Ulemerero wa Mulungu” ndi zinthu monga zimenezo, izo ndi maneno chabe kwa iwo. Kwa ife, ndi kuwonetseredwa! Mukuona? Izo si manenoso; izo ndi chenicheni! Amen!

244 Mulungu anati, “Pakhale kuwala,” amenewo anali maneno. Koma tsopano pali kuwala. Iko si maneno; iko ndi kuwala. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

245 Tsopano iwo si Mawu olembedwa chabe kwa ife, iwo ndi chenicheni. Ife tiri mwa Iye. Tsopano ife tikumva kukoma. Tsopano ife tikumuyang’ana Iye. Tsopano ife tikumuwona Iye, Mawu, akudziwonetsera Yekha. Izo ndi zobisika, kunja uko, chifukwa (chiyani?) Izo zaphimbidwa mu mnofu wa umunthu. Mukuona?

246 O, iwo amati, “Gulu la anthu lija, kodi iwo anapita sukulu yakuti? Kodi—kodi ndi maphunziro anji omwe iwo ali nawo? Kuti, nkuti—nkuti komwe iwo anachokerako? Kodi—kodi—kodi iwo ndi a gulu liti?” Mukuona? Huh! Mwaona, iwo sakuwamvetsa Iwo.

247 Bambo ananena kwa munthu wina, tsiku lina, anati, “Iwe umayenera kukhala wa chipembedzo kuti ukhale Mkhristu.”

248 Iye anati, “Ine ndine Mkhristu; ine sindiri wa chirichonse cha izo.” Uh-huh. Anati, “Mulungu anandichotsera ine khansa iyi,” anati, “tsopano inu mukuganiza chiyani za zimenezo?” Ameneyo anali dokotala. Iye anati, “Mundisonyeze ine zipembedzo zimene zikuchita zimenezo.” Mukuona? Chabwino. Mukuona? Izo zikadali zophimbidwabe.

249 Iye tiri mkati mwa Khristu. Tsopano, monga nthawi imeneyo, okhulupirira owona onse amamuwona Iye, Mawu a lonjezo a tsiku lino, akuwonetseredwa poyera. Amenewo ndi mawu aakulu ngati inu mungathe kuwamvetsa iwo. Mukuona? Mukuona? Okhulupirira onse owona, amene ali mu Mawu, amamuwona Mulungu mwapoyera. Chophimba chinang’ambika, ndipo Mulungu akuima poyera pamaso panu, akuwonetseredwa. Mukuona? Mulungu, akuwonetseredwa, poyera.

250 Pofuna kuti tichite izi, chophimba chathu cha chipembedzo chakale chiyenera ching’ambidwe kachiwiri. Pofuna kuti tiwone kwenikweni chimene Iwo ali, iwe uyenera utuluke pakati pa chinthu chimenecho. Mukuona? Iwe ukapanda kutero; iwo akhala akukokerabe chophimbacho pamaso pako, nthawi zonse, “O, palibepo kalikonse kwa Iwo.” Koma apa Iwo analembedwa, ndipo apa Iwo akuwonetseredwa, inu mwaona. Mukuona?

251 Tsopano, nanga bwanji ngati munthu akana kuti aliwone dzuwa, nkumati, “O, apo, ine ndikudziwa Mulungu anati, ‘Pakhale kuwala,’ koma kulibeko chinthu choterocho. Ine ndikupita mchipinda cha pansi. I—ine ndikukana basi kuti ndiliwone ilo?” Munthuyo ndi wopenga. Pali chinachake chalakwika ndi iyeyo.

252 Pali chinachake cholakwika ndi mwamuna kapena mkazi, wokhoza kuwona lonjezo la Mulungu ndipo, nkuwawona Iwo akuwonetseredwa, ndipo kenako nkumakana kuti awakhulupirire Iwo chifukwa chipembedzo chikukokera chophimba pansi. Mwaona, waphimbidwa!

253 Pofuna kuti uchite izi, zophimba zathu za chipembedzo ziyenera ziswedwe, ndi Mzimu wa Mulungu wa Moto ndi Lupanga, zimene ziri Mawu Ake. Nthawizonse Mawu Ake ndi Lupanga Lake. Mukuona? Ndipo Iye anatenga Lupanga Lake tsiku lijali, lodzaza ndi Moto, ndipo anang’amba chotchinga chimenecho kuchokera pamwamba mpaka pansi. Iye akuchita chinthu chomwe chomwecho ndi Lupanga

lomwelo lero! Osati “kachikhulupiro kanga, bukhu langa la tizikhulupiro, ka—katekisimu wanga.” Koma Lupanga la Ambuye, mukuwona, kung’amba chotchingacho mpaka pansi, ndipo inu nkumamuwona Mulungu ataima pa mbalambanda, akuwonetseredwa mu Mawu Ake. Ndi mawonekedwe a ulemerero bwanji kuwayang’ana! Mukuona? Chabwino. Mzimu Woyera wa Mulungu ndi Moto, Lupanga Lake, limang’amba icho. Mawu amang’amba chotchinga cha chipembedzo.

<sup>254</sup> Chabwino, ngati inu mutamangoti, “Mawu,” ndipo Mawuwo nkusamagwira ntchito? Lingakhale la ubwino wanji Lupangalo kukhala pano, ndi kumati, “Ilo silingang’ambe”? Kumati, “Uh,” ndipo ilo osang’amba?

<sup>255</sup> Koma pamene inu muliyika Lupanga la Mulungu ilo pamwamba apo ndipo nkuliwona ilo likung’amba, ilo—ilo lagwiridwa ndi dzanja lodzozedwa lotumidwa kuti lidzachite zimenezo. Mwaona, likung’amba motsegula icho, ndipo ndi Uyo apo. Apo izo zikumuwonetsa Mulungu ali pa mbalambanda, Yehova wankulu. Amenewo ndi Mawu Ake akuwonetseredwa, gawo limene linalonjezedwera lero. Kodi inu mukuzimvetsa Izo? Mukuona? Pamene Lupanga, lonjezo la lero, mu tsiku la lero, zomwe izo ziyenera kukhala, ndipo Mulungu nkutenga Lupanga Lake ndipo nkung’ambira pansi chotchinga cha chipembedzo ndi kuzikokera izo mmbuyo, ndi kudziwonetsera Yekha ndi kusonyeza kuti Iye ali pamenepo, Lawi la Moto lomwe lija. Zindikirani, amenewo ndi Mawu akuwonetseredwa kwa malonjezo a lero.

<sup>256</sup> Ife tikuwawona Iwo monga anachitira Petro pamene iye anati, “Ambuye, ndi kwa ndani kumene ife tingapiteko, titatha kuwona Izi?” Tingapitenso kuti? Ndi mpingo wanji umene ife tingajowine, pamene ife tinabadwira mwa Umodzi? Mukuona? Kodi inu mungathe. . . Kodi inu mungajowine chipembedzo chiti mutatha kudziwa Zoonadi izi, mwaona, pamene iwo (aliyenseyo) akuwakana Iwo? Mmodzi aliyense wa iwo! Ine ndiribe mmodzi yemwe akunena kapena kuchita chinthu kwa Iwo. Kulondola. Izo nzoona.

<sup>257</sup> Ine ndinayamba maulendo awa kuno, amene matchalitchi forte-thuu pa malo amodzi anathandizira; pamene ine ndinakafika uko, ine ndinalibe aliyense. Mmodzi aliyense wa iwo amati, “Iye amakhulupirira mu chitetezero Chamuyaya.” Zimenezo zimawapangitsa azamalamulo kukhala panja. Ena amati, “Iye amatizira mu Dzina la Yesu.” Zimenezo zimawasiya ena onsewo panja, mwaona. Koteru, ena a iwo amati, “Iye amakhulupirira mu mbewu ya serpenti. Serpenti ilibe mbewu!” Izo zima. . .

<sup>258</sup> Baibulo limati, “Ine ndidzaika udani pakati pa Mbewu yake ndi mbewu ya serpenti.” Mukuona? Mukuona zimenezo?



259 Icho, cho—chophimba, chinachotsedwapo pa Mawu. Mukuona? Izo nzoona. Izo zaululidwa kwa makanda. Icho—chinachotsedwapo. Iwo akuwawona Iwo. Ndipo zikhala, monga nthawiina ananenerapo. . . Izo nzoona. Ndiye izo zidzakhala, monga nthawiina ananenerapo, “Pamene inu mudzawona,” pamene chophimba ichi chidzachotsedwepo pa Mawu, miyambo ikadzachotsedwapo pa Mawu, monga nthawi ina Yesu ananena, “pamene inu mwandiwona Ine, inu mwawawona Atate.” Mukuona? Mulungu ndi Mawu Ake ali mmodzi. Tsopano kodi inu mukumvetsa? Pamene Mawu awonetseredwa, kodi Iwo ndi chiyani? Mukuona?

260 Yesu anati, “Fufuzani Malemba, inu mukuganiza kuti inu muli nawo M- . . . Inu mwakhulupirira mwa Mulungu, mukhulupirirensa mwa Ine. Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine. Koma ngati Ine ndikuchita ntchito, Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi. Pamene inu mwandiwona Ine, inu mwawawona Atate.”

261 Ndipo pamene inu muwawona Mawu akuwonetseredwa, inu mwawawona Atate, Mulungu, chifukwa Mawu ndi Atate. Mawu ndi Mulungu. Ndipo Mawu, akamawonetseredwa, ndi Mulungu Mwiniwake akutenga Mawu Ake Omwe ndi kumawawonetsera Iwo pakati pa okhulupirira. Palibe kanthu kamene kangawapange Iwo kukhala amoyo koma okhulupirira, okhulupirira basi. Sikuti ndi . . . Izo sizinga . . .

262 Inu mukhoza kutenga tirigu ndi kumubzala iye mu—mu—nthaka ya mtundu wina, iye sangamere nkomwe. Koma, chiyani, iye amayenera kukhala ndi feteleza winawake mu nthakamo kuti amumeritse tiriguyo. Ndipo ngati mulibemo—ngati umo . . . ngati feteleza wa mu nthakamo alibe—alibe, tirigu akapanda kuphuka kwa feteleza ameneyo, iye sadzamera nkomwe. Kotero ziribe kanthu kuti Mawu akugwera pati, ngati Iwo sagwera mu mtima wa mtundu woyenera . . .

263 Yesu ananena choncho. “Ina inagwera mmphepete mwanjira, pa nthaka ya miyala, ndipo mbalame za mumlengalenga zinabwera ndi kudzaidya iyo.” Ndiyeno Iye anati, “Ina inagwera pa minga ndi nthula, zomwe zinadzuka ndi kutsamwitsidwa pomwepo,” miyambo, zipembedzo, zosamalira za mdziko zinawatsamwitsa Iwo. Koma anati, “Zina zinapita mu nthaka yabwino ndipo zinabala mazana mazana,” anati, “umenewo ndiye Ufumu wa Mulungu.”

Ndi chinthu chomwe chomwecho, mwaona, ena sadzakhulupirira izo nkomwe.

264 Ena adzakhulupirira kwa kanthawi pang’ono, monga ophunzira. Iwo anamutsatira Iye, ambiri a iwo, sevente anamutsatira Iye kwa zaka, kuti adzafufuze; pafupi chaka ndi theka, kapena zaka ziwiri; basi kuti adzafufuze, kufikira iwo atapeza chinachake mwa Iye, ena . . . ngati kuti mwanjira ina Iye

anali ndi mphamvu ina yochitira zinthu izi, kapena ngati phazi la kalulu, wamatsenga wa mtundu wina, zimene Iye amachita kuti apange zinthu izi, momwe Iye amadziwira zimene zinali mu mtima wa anthu ndi zimene iwo amaganiza. Ndipo potsiriza iwo anadzapeza kuti Iye ananena kuti Iye “anabwera kuchokera Kumwamba,” Iye “anali Mawu Iyemwini.” Ndipo pamene iwo anachita izo, izo zinali zowachulukira iwo. Iwo anati, “Palibe munthu yemwe angathe kumvetsa Izi.” Ndipo iwo anamchokera Iye. Amenewo anali iwo amene anagwera pa minga.

<sup>265</sup> Izo zikubwereranso kwa chinthu chomwe chomwecho, mwa osonkhana aliwonse, inu mumakhala ndi odzipangitsa kukhulupirira, osakhulupirira, ndi okhulupirira. Izo zakhala ziripo mwa osonkhana aliwonse. Inu mumawapeza iwo nthawi zonse. Ena a iwo amadzipangitsa kumakhala ngati ndi okhulupirira, umenewo ndiye mtundu woipitsitsa. Ndiyeno iwo ali nawo awo amene ali kwenikweni osakhulupirira; iye sangakuvuteni inu, iye amangochokapo ndi kugwedezapo mutu wake. Koma iwo amene amadzipangitsa kukhulupirira, amati iwo ndi okhulupirira, mtundu wake ndi umenewo, ndiwo mtundu umene inu muyenera kusamala nawo, ndi odzipangitsa-kukhulupirira amenewo. Ndiyeno alipo ena okhulupirira enieni. Mukuona atatu amenewo apo?

<sup>266</sup> Analipo osakhulupirira. Mwamsanga pamene Iye anati, “Mudye Thupi la Mwana wa munthu,” o, bambo, zinathera pompo!

<sup>267</sup> Enawo anali odzipangitsa-kukhulupirira. Iwo anakhalabe mpakana, chimodzimodzi monga Yudasia anachitira, mpaka kumapeto komwe.

<sup>268</sup> Komano okhulupirira enieni, iwo samatha kuzifotozoza Izo, koma iwo amakhulupirira Iwo, mulimonse. Iwo anapitirirabe.

<sup>269</sup> Chophimba, mwambo wa osakhulupirira, chikachotsedwapo, iwe umamuwona Mulungu. Pamene chophimba cha miyambo chachotsedwapo, iwe ukhoza kuwona kuti Mulungu akadali Mulungu wa Mawu Ake. Iye akusungabe Mawu Ake. Iye ali—Iye ali Mulungu, Mlembi wa Mawu Ake.

Yemwe wabisala kuseri kwa zophimba za khungu, kwa ena. Inde, izo nzoona. Kwa iwo amene sangathe kupita kuseri kwa chophimba, Iye akadali panobe kuseri kwa zophimba za chikopa.

<sup>270</sup> Zindikirani. Ndiye, ife, zikatero ife timadzakhala gawo la Iye, pamene inu mukhala chophimba chomuphimba Iye. Inu mumakhala gawo la Iye, bola ngati Khristu akukhala mwa inu, monga Khristu anali wa Mulungu. Chifukwa Mulungu anali mwa Iye, amamupanga Iye kukhala Mulungu. Ndipo pamene Khristu ali mwa inu, chiyembekezo cha Ulemerero, inu mumadzakhala gawo la Khristu. “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita nayenso azidzazichita.”

Mukuona? Inu mumadzakhala gawo la Khristu bola ngati Khristu akubisala mwa inu. Ndiye izo zimabisika kwa wosakhulupirira, koma inu mumadziwa Iye ali mwa inu. Inu mukusungira Khristu yemwe ali kuseri kwa chophimba, khungu. Ndiye ife, chifu-. . .Kuseri, chifukwa cha chophimba ichi, chophimba apanso mu mnofu wa munthu, chikumubisa Mulungu (Mawu) kwa wosakhulupirira.

<sup>271</sup> Monga kunalembedwa, mwaona, “Olembedwa, inu ndinu akalata olembedwa,” Baibulo linatero. Tsopano, kodi *kalata* ndi chiyani? Iyo ndi “mawu olembedwa.” Ndipo inu ndi “olembedwa.” Mwakulankhula kwina, inu mukhoza kuwerenga Iwo monga chonchi, “Inu,” Iwo amati, “inu ndinu akalata olembedwa,” kapena, “inu ndi Mawu, amene alembedwa, akuwonetseredwa,” palibe kanthu kangawonjezeredwe kwa Iwo. Inu simungati, “Ndine kalata yolembedwa,” ndipo nkumakhala mtundu wa chinachake wosiyana ndi chimene *Ili* linalamba kale, [M’bale Branham akusasa Baibulo lake—Mkonzi.] chifukwa palibe chimene chingawonjezeredwe kapena kuchotsedwapo.

<sup>272</sup> Monga Doctor Lee Vayle akulemba bukhu lotchuka ili, ine ndikufuna kuti inu mudzaliwone ilo pakapita kanthawi. M’bale Vayle ali pano, ali pabwalopa penapake. Ine ndinamuwona iye panja. Ine sindikuganiza kuti iye angathe kulowa mkati. Koma iye akulemba bukhu kumeneko, ndi—ndi lododometsa kwambiri, la M’badwo wa Laodikaya. Ndipo ine ndikufuna inu. . .Ilo likhala likuchoka kosindikizidwa posachedwapa. Koteru, ife tikuliwerenga ilo kotsiriza tsopano. Ndipo anali kulemba, ndipo ife timakambirana Iwo mmenemo, mwaona, zokhudza. . .

<sup>273</sup> Aliyense nthawizonse amabwera kwa ine, ndikuti, “M’bale Branham, mabingu asanu ndi awiri awo amene liwu linabangula, ndipo Iye anati, ‘Usalembe Izi ayi, mwaona, koma uzitsekere Izo,’” ndikuti, “amenewo adzakhala mabingu asanu ndi awiri amene ati adzaululidwe mu masiku otsiriza, mwaona, mabingu asanu ndi awiri amene ati adzatiuze ife?” Tsopano, kodi zimenezo sizikumveka mwabwino kwenikweni? Mukuona? Koma taonani zimene inu mumalankhula pamene inu mukunena zimenezo.

Iye anati, “Uwone kuti iwe usalembe Izo ayi.” Mukuona? Mabingu asanu ndi awiri awa analankhula maliwu awo, mwaona, ndipo Iye anati, “Usalembe izo, mwaona, koma Izo ndi zakuti zidasindikizidwe mu Bukhu kufikira masiku otsiriza.”

<sup>274</sup> Tsopano winawake wakhala ali, ambiri akhala akunena ndi ine, ndipo azamulungu kumati, “M’bale Branham, ngati Ambuye Mulungu. . .” Amati, “Ngati—ngati. . .Ndi chokuchitikirani chanu, chimene Ambuye wakupatsani inu chifukwa cha anthu Ake,” ndikunena izi modzichepetsa, anati, “inu mungathe kulemba b—Baibulo inueni, Mawu anu, ngati Mulungu wawonetsera.”

275 Ine ndinati “Izo zikhoza kukhala zoon.” Mwaona, iye amayesera kuti andigwire ine. Mukuona? Ndipo ine ndinati, “Koma, inu mukuona, ine sindingathe kuchita zimenezo.”

Iye anati, “Nchifukwa chiyani kuti inu musatero? Inu muli nazo zokuyenerezani zonse.”

276 Ine ndinati, “Koma, inu mukuwona, mawu amodzi sangathe kuwonjezedwapo kapena kuchotsedwapo.” Mukuona?

277 Ndipo iye anati, “Chabwino, ndiye, mabingu asanu ndi awiri awo, inu mukuona,” anati, “kodi kuwomba kwa mabingu asanu ndi awiri kuja, kodi zimenezo sizingakhale kuti Vumbulutso limaperekedwa kwa munthu wina?”

278 Ine ndinati, “Ayi, bwana, kutero kungakhale kuwonjezera chinachake kwa Iwo kapena kuchotsapo Chinachake kwa Iwo.”

279 Zonsezo zinaululidwa Mmenemo, ndipo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zinatsegula vumbulutso la chimene Izo zinali. Ndicho chimene izo zinali. Mwaona, izo zikadali apobe mu Mawu. Inu mukuona, iwe sungathe kuchotsera ku Mawu amenewo. Izo sizingawasiye Mawu. Ndipo Mzimu wa Mulungu sungawasiye nkomwe Mawu amenewo. Iwo udzakhala nawobe Mawu; kuwachititsa ena khungu, ndi kutsegula maso a ena. Iwo nthawizonse udzachita zimenezo.

280 “Inu ndi akalata olembedwa, owerengedwa ndi anthu onse.” Kapena, inu ndinu... Ine ndimamasulira Zimenezo, kuzitembenuzira mbali iyi, mwaona, basi kungozitembenuza Izo, “Inu muli akalata amene alembedwa,” chifukwa inu simungathe kuwonjezera kanthu kwa Iwo, “amene akuwerengedwa ndi anthu onse; Mawu owonetseredwa a Mulungu,” mwakulankhula kwina.

Ndipo Petro ndi Yohane, kuti asonyeze izo, pamene iwo anapita kumeneko, iwo anazindikira kuti iwo anali mbuli ndi osaphunzira, iwo analibe maphunziro, koma iwo anazindikira kuti iwo amakhala ndi Yesu. Mukuona? Iwo anali mbuli ndi osaphunzira, koma iwo anali akalata olembedwa, mwaona, anawerenga kuti iwo anali ndi Yesu. Chifukwa, Yesu anali akudziwonetsera Yekha kudzera mwa iwo, Khristu ataphimbidwa mu mnofu wawo; akuwonetseredwa, kumapangidwa kukhala wamoyo.

281 Chimodzimidzi monga Iye anali mwa Mose. Pamene Mawu anali mwa Mose, iye anali Mulungu mu thupi. Pamene Iwo anali mwa Yesu, Iwo anali Mulungu mu thupi. Mukuona? Chinthu chokha chimene Iye anachita chinali kusintha chigoba Chake, osati Mawu Ake, osati chikhalidwe Chake. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye amangosintha mawonekedwe Ake. Iye anasintha kuchokera kwa Nowa anapita kwa Mose; Iye anasintha kuchokera kwa Mose anapita kwa Davide; kuchokera kwa Davide, Yosefe; mpaka mmusi kufikira

Iye anadzabwera mu chidzalo cha Umulungu mu thupi. Mukuona?

<sup>282</sup> Izo ndi Mulungu yemwe yemweyo! Ameni. Ameni. Ine ndikuyembekeza kuti zimenezo zikudutsa. Mukuona? Izo ndi Mulungu yemwe yemweyo, koma Iye wangotenga chophimba china. Mwaona, Iye wavala chophimba china.

<sup>283</sup> Iye anazichita izo mwa okonzanso, anavala chophimba, anavala chophimba. Mpaka, potsiriza, Iwo anabwera kudutsa m'badwo wa Chilutera, kutsika kudutsa m'badwo winawo, kenako potsiriza Iwo anadzafika kokhala Amphumphu. Basi Iwo asanabwere, mneneri anaukanso kachiwiri. Chimene izo zikuchita, izo zikuchitira mthunzi Mawu, kusonyeza kumbuyo kuno, kuwulula zimene zachitika, zimene zasiyidwa, kuti mpingo udzakhala wopanda . . . osati wopanda kumvetsa. Ndiye pamene izi zikuzimilira, ndiye, monga Yohane ananena, “Ine ndiyenera ndichepe, Iye ayenera akule,” ndiye zonse-mu-zonse zikubwera mwa Iye. Iye akuwonetseredwa kwathunthu, kudzera mwa Luther, Wesley, ndi m'badwo wa Pentekoste, ndipo mpaka mmusi, mpaka mmusi, Iye akuwonetseredwa kwathunthu, inu mukuona, kumabwera mmusi, kuwonetseredwa basi, Mulungu akudzifutukula: Kumamuwona Iye (Tsopano, zindikirani.) akukwaniritsidwa mu malonjezo Ake a tsiku la *Iero*, monga *iwo* anali nazo.

<sup>284</sup> Tsopano Mose anali Mawu tsiku lijali, chifukwa Mawu anaperekedwa kwa iye a tsiku limenelo; Mose. Yosefe anali Mawu mu masiku ake, akufanizitsa Khristu ndendende. Mwaona, mmodzi aliyense wa iwo anali Mawu.

<sup>285</sup> Ndipo pamene Yesu anabwera, Iye anali Mawu mu chidzalo Chake, chifukwa dongosolo lonse la chiwombolo limagona mwa Iye. Dongosolo lonse la chiwombolo silinagone mwa Mose, silinagone mwa Yosefe, silinagone mwa Eliya. Mwaona, iwo amangokhala gawo chabe la Mawu, akulozera kwa Iwo. Mukuona? Tsopano zindikirani, musunge malingaliro anu; apa Iwo akubwera, pamene ine ndikulankhula. Mwaona, dongosolo lonse silinali mwa iwo. Iwo anali akulozera kwa Iwo.

<sup>286</sup> Choncho, atachokapo Iye, Chidzalo, ife sitingathe kulozera kwa chinachakenso. Izo zikulozera mmbuyo kwa Iye, Mawu. [M'bale Branham akunyamula Baibulo lake—Mkonzi.] *Ili* ndiro Vumbulutso lathunthu; palibe chimene chingawonjezedwe kapena kuchotsedwapo kwa Ili. Ndi *limenelo* Vumbulutso lathunthu. Zonse izo, mthunzi wa Iye wakudzayo; koma pamene Iye anabwera, Iye anali Wangwiro. Ahebri 1, “Mulungu mu nthawi za amakedzana ankalankhula ndi makolo kudzera mwa aneneri,” Mulungu ankalankhula kudzera mwa zophimba, aneneri, “koma mu masiku otsiriza ano kudzera mwa Mwana Wake, Yesu Khristu.” Ndi zimenezotu. Anavundukulidwa uko pa Kalvare, Mwana wa Mulungu, anavundukulidwa.

287 Zindikirani, “anapangidwa wamoyo.” Ndipo, lero, pamene Mawu akuwonetseredwa mu zotengera za anthu, zophimba, zimenezo ndi mwamtheradi Mawu akukwaniritsidwa mu tsiku limenelo, zimene zikubwereranso kwa Mulungu. Pobatizidwira kulowa mwa Iye, molingana ndi Akorinto Woyamba 12, ife timafika pozindikiridwa ndi Iye. Amenii.

288 Ine ndinati theka la ora, koma zingatheke kuti ine ndikhale motalikirapo pang’ono? [Osonkhana akuti, “Amenii.”—Mkonzi.] Mukuona? Taonani, ine basi sindingathe kuti ndiphonye izi apa. Zindikirani, kuzindikiridwa ndi Iye!

289 Tsopano zindikirani. Ndi angati ali mbadwa za Amerika muno? Kwezani mmwamba manja anu. Chabwino, inu ndi mbadwa ya Amerika, ndiye inu mukuzindikiridwa ndi fuko lino. Chirichonse chimene fuko lino liri, inu muyenera kukhala. Ndi kulondola uko? Inu muli ulemerero wake wonse ndipo muli manyazi ake onse. Inu mumazindikiridwa ndi iye. Inu ndinu wa Chimerika, kotero inu mumatenga za Amerika. Aleluya!

290 Ine ndinali ndi George Washington pamene iye ankawoloka Delaware. Ine ndimazindikiridwa ndi iye. Izo nzoona. Ine ndinali ndi Abraham Lincoln ku zolankhula za ku Gettysburg. Ine ndinali kuima pamenepo. Ine ndinali ndi asilikari ku Guam, anyamata inu, pamene inu munkakweza mbendera ija. Ine ndinali kumeneko. Ndine wa Chimerika; ine ndimazindikiridwa ndi zimenezo. Amenii. Tsopano, kukhala wa Chimerika, chirichonse chimene manyazi ake ali mu Kuwukirako, ine ndimawanyamula iwo, chifukwa ndine wa Chimerika. Izo nzoona.

291 Ndipo ngati Mkhristu, ine ndimazindikiridwa ndi Iyeyo. Amenii! Ine ndinali ndi Nowa pamene iye ankakalowa mu chombo. Ine ndinali ndi Mose pamene iye ankatuluka ku Igupto. Amenii! Ine ndinali Eliya pa Phiri la Karimeli. Inde, bwana! Ulemerero kwa Mulungu! Ine ndinali ndi iye pamene iye ankachita zimenezo. Ine ndinali moonadi ndi Iye, ine ndinazizindikiritsa ndekha mu imfa Yake uko pa Kalvare pamene ine ndinkafa ku zinthu za mdziko, kwa inemwini ndi miyambo yonse. Ine ndinazindikiridwa ndi Iye. Ine ndinazindikiridwa ndi Iye pa mmawa wa Isitara pamene Iye anawuka kwa akufa. Ine ndinazindikiridwa ndi Iye pa Tsiku la Pentekoste, pamene Mzimu Woyera unatsika ngati mkokomo wa mphepo yamphamvu. Ine ndinazindikiridwa ndi Iye. Zonse zimene Iye anali ine ndinali, zonse zimene ine ndiri Iye anali; amenii, pokhala akufa mwa Iye ife timazindikiridwa ndi Iye. Chimene Iye ali ine ndiri. Amenii!

292 Chimene fuko lino liri ine ndiri. Ndine wonyadira kukhala chimenecho. Ndine wokonzeka kunyamula manyazi ake. Ndine wokonzeka kunyamula chitonzo chake pokhala wa Chimerika. Izo nzoona. Koma ndine pawiri zimenezo kwa Yesu

Khristu! Zonse zimene Iye anayamba wakhalapo ine ndiri. Ine ndimakonda kuzindikiridwa ndi Iye.

<sup>293</sup> Atumwi amenewo, pamene iwo ankabwerera, iwo anachiyesa...iwo anasekedwa, ndipo anatchulidwa china chirichonse, iwo anachiyesa kuti unali ulemu wawukulu kunyamula chitonzochi cha Dzina Lake.

<sup>294</sup> Ndine wokondwa lero kukhala mmodzi wa iwo, kuzindikiridwa ndi Mawu, omwe ali Khristu. Kuzindikiridwa ndi Iye! Pobatizidwira kulowa mwa Iye, ife timazindikiridwa; kuzindikiridwa mu chifaniziro Chake, kuzindikiridwa ndi Mawu Ake, omwe ali Iye. Ngati ine ndiri mwa Khristu, ndine Mawu Ake; pakuti Iye ali Mawu, ndipo chimene Iye ali ine ndiri. Ameni! Kodi inu mukumvetsa Zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino.

<sup>295</sup> Mawu kuwonetseredwa, kapena kuwululidwa mu Vumbulutso limenelo uko, ndiye kodi zimenezo zikundiika pati ine? Ngati Iye ali Ulemerero wa Shekinah uwo, ndine gawo la Iwo. Ameni! O! Ameni! Izo nzoona. Mawu Pawokha akamawululidwa, amadziulula Wokha.

Taganizani! Zinsinsi za Mulungu zikudziwitsidwa kwa ife mu tsiku lino, ndi Mtumiki Wakumwamba yemweyo yemwe anadziwitsidwa kwa iwo mu masiku amenewo; zindikirani, Lawi la Moto lomwelo limene linamutuma Mose; Lawi la Moto lomwelo limene linali pa Mose yemwe analemba Baibulo; Lawi la Moto lomwelo limene Paulo anakomana nalo pa njira yake waku Damasiko.

<sup>296</sup> Ndipo Paulo analemba Chipangano Chatsopano. Kumbukirani, Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, iwo ankangolemba zimene iwo amaziwona; koma Paulo anali ndi Vumbulutso. Iye analisisola Ilo, pakuti iye anali atakomana ndi Lawi la Moto, iyemwini. Ndipo taganizani, chimodzimidzi...

<sup>297</sup> Kumeneko, Yosefe, onse amenewo ankalemba zimene zinkachitika, aliyense ankalemba mu tsiku limenelo. Koma pamene Mose anabwera powonekera, iye anali ndi Vumbulutso. Iye anali atakomana nalo Lawi la Moto, ndipo Ilo linawulula kwa Mose momwe Genesis. Iye analemba mabuku oyambirira anayi a Baibulo, Mose anatero. Ndi kulondola uko? Pakuti iye anakomana naye Mulungu mmawonekedwe a Lawi la Moto, ataphimbidwa mu Lawi la Moto.

<sup>298</sup> Pamene Paulo anakomana naye Iye pa njira... Ophunzira ankangolemba zimene iwo amaziwona Iye akuchita, koma Mose anali ndi Vumbulutso; anapita mpaka ku Igupto kwa zaka zitatu ndipo anakaphunzira, ndipo anakawona kuti Mulungu wa Chipangano Chakale anali Yesu wa Chatsopano, Vumbulutso! “Ine sindinali wosamvera masomphenya Akumwamba.” Izo nzoona. Kulondola!

<sup>299</sup> Ndipo taganizani za Izo! Lawi la Moto lomwelo limene linkabwera pa amuna awo amene ankalemba Baibulo, ndi Lawi la Moto lomwelo pano, lero, likutanthauzira Baibulo. Ameni! Momwe ife tikumuthokozera Iye chifukwa cha izo! Chimodzimodzi! Ndi chithonhozo bwanji! Ndi kuzindikiridwa bwanji! Ndine wokondwa kwambiri kuzindikiridwa mu zimenezo, ine sindikudziwa kuti ndichite chiyani! Ine kuli bwino kuti ndizindikiridwe mu Zimenezo kusiyana ndi Baptisti yonse, Methodist, Presbateria, Lutheran, ndi ena onse a iwo. Kuzindikiridwa mu Mawu amenewo kumene kuli Ulemerero wa Shekinah uwo ndi Vumbulutso!

<sup>300</sup> Lawi la Moto kuwonekera poyera pakati pathu, kuzindikiritsa kuti Uthenga ndi wolondola, monga Iye anachitira pa Phiri la Sinai. Kumbukirani, uthenga woona usanabwere, Mose analalikira ndipo anawatsogolera iwo kuti atuluke mu Igupto; koma kumeneko, malamulo enieni asanalembedwe (Zisindikizo zinabweretsedwamo), Mulungu anatiska pamaso pa anthuwo ndipo anatsimikizira kuti Mose anatamizidwa kuchokera kwa Iye, (kulondola uko?) mu Lawi la Moto limene Mose anati iye analiwona mu chisamba ndipo linalankhula naye iye.

<sup>301</sup> O, mu masiku otsiriza ano, kuliwona Lawi la Moto lomwe lija pakati pathu pomwe, likulankhula Mawu omwewo; osati zokhazo, koma kuwatanthauzira Iwo powawonetsera Iwo, ndi powatsimikizira Iwo, Iwo ndi Choonadi.

Kotero, anthu alibe njira imodzi yokaikirira, pokhapokhapo mwadala iwo atafuna kuti azitero. Ndipo, ndiye, “Iye amene achimwa mwadala atha kudziwa Choonadi, apo sipakhalanso nsembe ya tchimo.”

<sup>302</sup> Zindikirani, Lawi la Moto lomwelo limene linatumizidwa kwa Mose ndi kwa Paulo, limene linalimba Baibulo, tsopano latumizidwa kuti lidzaulule Ilo. Chisomo cha Mulungu, Mulungu wosasintha, akukwaniritsa malonjezo a Mateyu 28, “Taonani, Ine ndiri ndi inu nthawizonse”; kukwaniritsa Yohane Woyera 14:12, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita, inunso”; kukwaniritsa Luka Woyera 17:28-29, “Mu masiku otsiriza Mwana wa munthu adzaululidwa,” mwaona, mwaona; Malaki 4, “Taonani, Ine ndidzakutumizirani inu Eliya mneneri, yemwe ati adzabwezeretse Chikhulupiriro cha anthu kubwerera ku Mawu apachiyambi.” Mukuona? Momwe izi. . . Mukuona? O, mai!

<sup>303</sup> Iye anafa, kuti adzaziulule Yekha kwa ife. Tsopano tiyeni ife tife kwa ifeeni, kuti timuwulule Iye kwa ena. Tiyeni ife tife kwa miyambo ndi zinthu, kuti tikamuwulule Iye kwa ena. Tife kwa zipembedzo, kuti tikamuwulule Iye kwa ena.

<sup>304</sup> Zindikirani, kachisi wakale anali nawo mkati mwake Ulemerero wa Shekinah, ndi Kuwala kwa Shekinah pa Mawu. Mawu ndi Mbewu; Iwo amabweretsa mkate woweyula kwa



okhulupirira okha. Magazi nawonso amakhala pa pangano; ndipo Magazi ndi madzi, madzi amene amapereka moyo kwa njere, tirigu, mbewu, yomwe ili Mawu.

<sup>305</sup> Chimodzimidzi monga Yesu anati, “Monga Mose anakweza njoka ya mkuwa,” ndiye kenanso Iye anati, “Mulungu anakonda dziko lapansi mwakuti Iye anampereka Mwana Wake yekhayo wokonedwa; aliyense amene akhulupirira pa Iye asataike.” Mose anakantha thanthwe mu chipululu, kuti akawapulumulutse anthu otaika, kapena kuti abweretse madzi. Mulungu anamukantha Yesu, kuti akatulutsemo Mzimu kuchokera mwa Iye, kwa anthu akufa. Magazi anatuluka mwa Iye, chimene chiri, “Madzi otsuka mwa Mawu.” Chimene, Madzi amabweretsa Moyo kwa Mbewu. Ndipo zinabweretsa Ulemerero wa Shekinah; kuwalira pa Mawu, omwe anabweretsa mkate woweyula. Ndipo mkate woweyula unali wa anthu osankhidwa okha. Uh-huh. Kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>306</sup> Tsopano kulowa mu chophimba, kudutsa chophimba, kukafika mu Kukhalapo Kwake, kumene kuli Mawu (osati kachikhulupiriro), Mawu; mmenemo kumawona Ulemerero wa Shekinah, Shekinah, Mphamvu, Mzimu Woyera kumawalira pa Mawu, kumabweretsa lonjezo, zikusonyeza kuti uli kuseri kwa chophimba. Amen!

Ndawoloka zophimba zong’ambidwa kumene  
Ulemerero sulephera, (Uh!)

Aleluya, aleluya; ndikukhala mu Kukhalapo  
kwa Mfumu.

Ndawoloka zophimba zong’ambidwa kumene  
Ulemerero sulephera,  
Ndikukhala mu Kukhalapo kwa Mfumu.

<sup>307</sup> Chikopa chakale cha katumbu, zipembedzo, zang’ambidwira pansi. Ine ndabowoleza kudutsa zimenezo, ndakalowa mu Ulemerero wa Shekinah, ndipo ine ndikuwawona Mawu. Ine ndikuwona Lawi la Moto likuyenda. Ine ndikuwawona Mawu akuwonetseredwa. Zimene Iye ananena kuti Iye akanadzachita mu masiku otsiriza ano, ine ndikuziwona izo zikukula. Ine ndikuwawona ana akudya Mkate wa Shekinah iwo wobwera kuchokera ku kucha kwa Mawu amenewo, amene amawakhulupirira Iwo. Amen! Ndi ora lodabwitsa bwanji limene ife tiri nkukhalamo! Mwaona, Shekinah amakhala pa Mawu; ndipo pansi pamenepo pamakhala Mkate. Ndipo pamenepo pamakhala Magazi, akukonkhedwa, chimene chimawapatsa Iwo madzi. Mzimu umapereka Moyo kwa Mawu. Ndipo . . .

Ndi angati anawerengapo, anamvetserapo tepi ya *Mlandu*? Inde. Ndikuganiza, ambiri a inu munatero. Inu munawona pamenepo, izo zimatengera . . .

Mawu amenewo ayenera kukula. Pofuna kuti akule, Iwo ayenera kukhala pa nthaka ya mtundu woyenera. Mukuona? Ndipo Mulungu amapanga lonjezo, ndipo ilo limagunda mtima umenewo, izo sizingathe kulephera.

308 Nowa anadikirira zaka handiredi ndi twente. Abrahamu anadikirira zaka twente-faifi, pa mwanayo. Mulungu ananena choncho, ndipo izo zinakhazikitsa izo. Mukuona? Ndi chiyani chimenecho? Mawu anali ali pamenepo akutsiriridwa ndi chikhulupiriro, akuwakhulupirira Iwo, izo zinabweretsa zotsatira. Izo zinabweretsa mwana; izo zinabweretsa mvula; izo zinabweretsa chigumula; izo zinabweretsa namwali yemwe adzaima.

309 Mneneri anati, “Namwali adzaima.” Sindikukaika kuti mtsikana wamng’ono aliyense amapita ndipo amakakonzekera zovala za mwana. Chabwino, mneneri uyu Yesaya anali mneneri wozindikiridwa, wotsimikiziridwa ndi Mulungu. Ndipo Ambuye anati, “Namwali adzaima. Ine ndiwapatsa iwo chizindikiro chazimu, chizindikiro chachikulu; namwali adzaima.”

310 Pamenepo, anthu onse awo, okhulupirira amenewo, chimodzimidzi monga inu nonse. Ndipo iwo anamumva mneneri amenewo akunena zimenezo, mtsikana wamng’ono aliyense. . . Bambo aliyense amati, “Ameneyo akhala mwana wanga wamkazi. Inde, bwana.” Aliyense amapita ndipo amakagula nsapato ndi mathewera ndi chirichonse, amakonzekera, chifukwa iwo amadziwa kuti iye akhala naye iye. Kambadwo kameneko kanadutsa, ndipo iwo anaganiza, “Mneneri wozindikiridwa, wotsimikiziridwa ndi Mulungu uja, angathe bwanji kunena cholakwika chirichonse? Izo ziyenera kukhala chomwecho!”

311 Zinali zaka eyiti handiredi mtsogolo, koma iye anadzabala mwanayo. “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita.”

312 “Ndipo kudzachitika mu masiku otsiriza,” atero Mulungu. Mwaona, ndife pano, k—Kuwala pa Mawu. Monga kuwala kwa dzuwa kumaisintha mbewu kuchokera ku ulemerero kupita ku ulemerero, ife nafenso timakhala—timakhala ofanana ndi Iye pamene ife tikukhala mu Kukhalapo Kwake; monga Iye, kuwumbidwa mu chifanizo Chake chodala pamene ife tikuyenda ndi Iye.

313 Penyani chimene dzuwa limachita. Inu mukabzala mbewu, chimachitika ndi chiani? Mbewu imeneyo imavunda. Mkati mwa mbewuyo mumakhala moyo. Moyowo umatulukirapo ndipo umabweretsa phesi. Tsopano, iyo siimawoneka ngati yoyambayo.

Ndi uyo Luther. Iye anali phesi. Chabwino.

Phesilo linapitirira ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, ilo linatulutsa ngayaye. Mwaona, chimenecho chinali chitsitsimutso cha Wesley; sizinali monga zinazo.

Kenako potsatira panabwera chitsitsimutso cha Pentekoste, mwaona, zinabweretsa ubatizo wa Mzimu Woyera. Chabwino.

Chinachitika ndi chiyani? Ife tinapeza chuku pa khutu. Izo zinayamba kumawoneka moyipa. Chinthu *ichi*, chinthu *icho*, icho sichikuwoneka ngati Mawu. Icho sichiri monga zonse za Izo. Icho sichiri monga Njere yapachiyambi imene inapita pansi.

<sup>314</sup> Koma Mulungu akadali pomwepo kuti akapange izo—izo zikakhale chimodzimodzi basi. Zindikirani, kodi izo zikuchita chiyani? Izo potsiriza zikubwereranso ku Mbewu yapachiyambi kachiwiri. Pamene Iye anadzabwera mmawonekedwe a Martin Luther; pamene Iye anadzabwera mmawonekedwe a John Wesley; pamene Iye anadzabwera mmawonekedwe a Pentekoste; Iye ayenera kuti adzadziwulule Yekha kachiwiri monga Mbewu yomwe ija imene inapita pansi, Mwana wa munthu. Iye anadziwulula Yekha ngati Mwana wa Mulungu, kudzera mu m'badwo wa phesi ndi zina zotero, koma mu m'badwo wotsiriza uno Iye ali woti adziwulule Yekha ngati Mwana wa munthu kachiwiri. Mukumvetsa izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino, monga pachiyambi, kuwumbidwa!

<sup>315</sup> Ndipo kodi phesilo limakula chiyani? Ilo likumakula nthawi zonse. Phesi laling'ono limenelo limakula, komabe ilo siliri monga mbewu yapachiyambi ija. Chimodzimodzinso ndi uthenga wa Luther; ayi, potsatira panabwera—mauthenga enawo, Finney, Sankey, Knox, Calvin, mpaka mmusi, palibe aliyense wa iwo. Iwo anali akadali apobe uthenga koma, chimene iwo unali, iwo sanapeze Vumbulutso lathunthu la Iwo chifukwa nthawi yake siinali imeneyo. Inu simungathe kuyika njere pa mbewu nthawi yake isanakwane. Mukuona? Ndiyeno, potsiriza, apo panadzabwereranso Mbewu yapachiyambi imene inapita mu nthaka.

<sup>316</sup> Mukuona Mulungu amatsatira chirengedwe ndendende. Mwaona, Iye anabadwa ali mwanawankhosa, ndi chifukwa chake Iye anakabadwira mu khola. Anaankhosa samabadwira mmakama. Mwaona, Iye *anatsogozedwa* waku Kalvare. Mwanawankhosa, nkghosa zimatsogozedwa. Izo nzoona. Mbuzi zimatsogolera izo kokaphedwa, inu mukudziwa zimenezo, nyumba yophera. Mbuzi zimatsogolera izo, koma izo zimayenera kuti zizitsogozedwa. Huh! Izo nzoona. Kotero Iye anatsogozedwa kokaphedwa, mwaona, chifukwa Iye anali Mwanawankhosa.

<sup>317</sup> Chirichonse chimamuzindikiritsa Iye mu chirengedwe. Ndi chifukwa chake Iye anabadwa mu Malichi kapena Epulo, osati mu Disembala; Iye sakanatero, kumakhala mapazi twente a chisanu kumeneko pa nthawi iyo ya chaka. Osati mulungu

wa dzuwa, koma Iye anali Mwana wa Mulungu. Mukuona? Mwana wa dzuwa wa Chiroma pa tsiku la twente-faifi la Disembala, pamene dzuwa limadutsa malo ake kumeneko ndipo iwo amakhala ndi zochitika za Chiroma, ndipo amadzitcha tsiku lobadwa mulungu wa dzuwa, ndipo iwo anazipanga izo kukhala Mwana wa Mulungu. Ayi, ayi. Iye anali Mwana wa Mulungu. Tsiku lake lobadwa linali ndi chirengedwe chonsecho. Ndendende.

Tsopano zindikirani apanso tsopano pamene ife tikupitirira, ife tatsala ndi kanthawi pang'ono.

<sup>318</sup> Tsopano ku ungiro. Phesilo litatha kuwumbidwa; ngayaye zitatha kuwumbidwa; njere itatha kubwera mu chitsononkho; ndiye iyo imayenera kubwera ku ungiro, kubwereranso ku mbewu ya nthawizonse kachiwiri.

Ndipo, kumbukirani, njere imayenera kumeretsedwa. Mukuona? Ngati iyo siitero, iyo siingakhale moyo. Mukuona? Palibe za izo zimene zinali kunja kwa mauthenga amenewo ziti zidzabwere konse ku Moyo. Izo ziyenera kumeretsedwa kwa Iwo. Koma, kumbukirani, Moyo womwewo umene unali mu phesi umadzakhhalanso mu njere. Iwo ukungodzikhwimitsanso wokha, mwaona. Iye anadziulula Yekha, (chiyani?) Mwana wa munthu, njere imene inapita mu nthaka. Mukuwumva Uthengawo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.]

Agriki ananena kwa Iye, "Ife tikufuna timuwone Yesu."

<sup>319</sup> Iye anati, "Pokhapokhapo njere ya chimanga ikagwera mu nthaka." Mukuona? Chabwino.

<sup>320</sup> Tsopano kodi kenako Iye Yekha anadziwulula chiyani? Mmawonekedwe osiyanasiyana; phesi ndi ngayaye, ndi zina zotero, ndi masamba onse ndi chirichonse. Iye anadziwulula Yekha pamenepo, (chiyani?) Mzimu womwe womwewo, koma mmawonekedwe osiyana. Mukuona? Koma chotsirizira cha mbewu imeneyo ndi chiyani? Iyo ikubwereranso kukakhala njere yapachiyambi. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.]

<sup>321</sup> Ndipo utumiki Wake ukubwera, kuchokera kwa okonzanso awo, ukubwerera ku Mawu apachiyambi kachiwiri. Mawu amadza kwa mneneri. Ndipo Iye analonjeza izo, mu Malaki 4, "Ndi kudzabwezeretsa Chikhulupiriro cha anthu kubwerera ku mbewu yapachiyambi." Imene inapita mu nthaka ili pano chimodzimidzi. Njere yatulukira kudzera apa. Iyo inatulukira ngati Mwana wa Mulungu, tsopano Iyo ikudziwulula Yokha apa ngati Mwana wa munthu, ndipo kenako Iyo ikudziwulula Yokha ngati Mwana wa Davide pa Mpando wachifumu. Mwaona, Ana atatu amenewo, chimodzimidzi basi. O, mai, apanso monga yapachiyambi!

<sup>322</sup> Tsopano kwa utumiki wangwiro wa Iyemwini; osati munthu wina, osati chipembedzo china, monga iwo

agwirira ntchito kudutsa m'badwo uwo uko, mwaona; koma Iyemwini kuwonetseredwa, kudziwonetsera Yekha kwa lonjezo, kupangitsa Luka Woyera 17:28, Malaki 4, ndi ena otero, Ahebri 13:8, kulondola ndendende basi. Pa nthawi imeneyo, kodi iyenera kukhala nthawi yanji? Pamene Mbewu yachifumu ya Abrahamu ikuyembekezera Mwana wolonjezedwa. Ndipo zoimira zonse ziyenera kukwaniritsidwa. Ndipo Mulungu Mwiniwake anawonekera mmawonekedwe a munthu, kwa mbewu yachirengedwe ya Abrahamu, chisanachitike chiwonongeko, ndipo Yesu anati zidzakhala chinthu chomwecho kwa Mbewu yachifumu iyi Mwana wolonjezedwayo asanabwere.

<sup>323</sup> Zindikirani chophimba chakale chimene chinkabisa Ulemerero. Zikopa zakale za akatumbu, panalibepo kukongola kuti ungamukhumbwe; ngakhaleenso mnofu Wake. Ndi chifukwa chake anthu ankati, “Kamunthu kakang’ono kokalamba kofooka monga choncho?” Mwinamwake wa usinkhu wa zaka sate, nkukhala waimvi, ndi ndevu Zake za imvi, analibe zochuluka zoti ungamuyang’anepo. Baibulo linati, “Analibe kukongola kuti tingamukhumbire Iye.” Iye sanali kuwoneka ngati Mfumu, chikopa chakale cha katumbu, koma, o, zimene zinali mkatimo!

<sup>324</sup> Ndipo gulu laling’ono la “oyera-odzigudubuza” litakhala pamodzi mu chipinda chotentha ngati ichi, iwo amawatcha iwo, opanda mawonekedwe ochuluka kuti nkukhumbiridwa, koma chimene chiri mkatimo! Ine ndikutsimikiza icho nchophimbidwa kwa mitima yambiri, inu mukuona. Inu mukuona? Chabwino.

<sup>325</sup> Kunjaku Izo sizinali kanthu, koma zonse zinali mkatimo. Ukakhalamo mkati mwa Izo, ndiye iwe umaziwona Izo. Iwe umalowamo chotani Mmenemo; pogwirana chanza, kujowina? Ayi. Kubadwira Mmenemo. Kufa, kuchotsa chikopa chako chakale cha katumbu, mwaona, iwe wako wakale, kuti ukalowe mwa watsopanoyo. Mukuona? Kuchisiya chikopa chakale cha katumbu.

<sup>326</sup> Kuwala kwa Shekinah sikumatero. . . Mvetserani, atumiki! Atumiki, ine ndikufuna kuti inu mumvetsera kwa Izi. Ukakhalamo kamodzi mkatimo. . . Tsopano ine ndizitenga izi mophweka kwenikweni, kuti inu mukhale otsimikiza kuti mwazimva Izi. Ukakhalamo kamodzi mkati mwa chophimbamo, pansu pa Ulemerero wa Shekinah, Kuwala kwa Shekinah sikumawatenga Mawu a Mulungu ndi kumuwulula Yesu kuti ndi “wambwebwe,” ayi, monga azipembedzo akuchitira lero, “kuwerenga maganizo, oyera-odzigudubuza, Belezebule.” Ulemerero wa Shekinah sumamuwulula Iye kukhala wa izo.

<sup>327</sup> Koma Ulemerero wa Shekinah umachetsa Mbewu yolonjezedwera ora limenelo, ya Mawu, kumusonyeza Iye kuti akadali apabe Kakombo wa Mchigwa. Iwo umabweretsa

Mbewu imeneyo, Kakombo wa Mchigwa, Mkate wa Moyo, Alfa ndi Omega, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iyeyo ndi gawo la okhulupirira. Ulemerero wa Shekinah umamuwulula, kwa wokhulupirira, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

<sup>328</sup> Osati, “Masiku, Iye ndi wakale, ndipo Iye anafa ndipo zonse zinatha.” Kotero amzanga, ngati inu mukukhulupirira zimenezo, ngati inu mukukhulupirira zimenezo, inu simunafikebe mu Ulemerero wa Shekinah. Ulemerero wa Shekinah ungamuwulule bwanji Iye kukhala mwa anthu atatu? Mukuona? Ulemerero wa Shekinah ungamuwulule motani Iye kuti muziwabatiza, anthu, mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” pamene palibepo munthu mu Baibulo anabatizidwapo mwanjira imeneyo? Ulemerero wa Shekinah ungamuikire Iye malire bwanji kwa mtumwi, pamene Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Mukuona?

<sup>329</sup> Ulemerero wa Shekinah umamuwonetsera Iye. Iwo umawabweretsa Mawu a lonjezo, mpaka kwa inu. Ndi chifukwa chake Iye ankachita kuphimba nkhope ya Mose, chifukwa mwa iye munali Mawu. Iye anamuphimba Yesu, ngati Munthu wamng’ono wodzichepetsa, kuwaletsa iwo kuti asamuwone Yehova. Ndipo Iye akudziphimba Yekha lero, mu zotengera zadongo, zokhala ndi Shekinah. Kunjaku amawoneka ngati gulu la oyera-odzigudubuza, zikopa zakale za akatumbu, koma mkatimo mukubisa Ulemerero wa Shekinah.

Ndipo Iwo umachetsa Mkatewowejula umene ife timadyapo, ndi kumayendetsa kudutsa mdzikoli kwa, mazana a mamailosi, mwaona. Icho ndi Chakudya cha okhulupirira. Icho ndi cha wokhulupirira yekha. Kumbukirani, Mkatewowejula umakhala wa wokhulupirira yekha, mwaona, Mbewu ya Mkatewowejula. Zindikirani. Kodi iwo umachita chiyani? Ulemerero wa Shekinah uja, ukakhala pa Mkatewowejula, umateteza Iwo kuti usavunde.

<sup>330</sup> Kumbukirani, manna aja amene ankabwera kuchokera Kumwamba, iwo amakaikidwa mu Ulemerero wa Shekinah, kuchokera ku kam’badwo kamodzi mpaka kwa kena. Kunjako, iwo umakhala ndi mphutsi mwa iwo, ukakhala usikuwonse, iwo umavunda. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>331</sup> Kunja kwa Ulemerero wa Shekinah, “Masiku a zozizwitsa anatha. Mwaona, zonsezo ndi zotengeka.” Koma mkatimo . . .

<sup>332</sup> Taonani, iwo ali ndi mbewu ina ya mpendadzuwa yochokera mu nkhekwe za ku Igupto imene inaikidwa kumeneko mmasiku a Yosefe, zaka zikwi zinai, pafupifupi, zapitazo. Yosefe anaiyika iyo mu nkhekwe. Iwo ankabzala iyo. Iyo imakhala moyo. Bwanji? Iyo inali ndi moyo.

<sup>333</sup> Kodi Ulemerero wa Shekinah uwu lero ndi chiyani? Kuti tikalowe kudutsa chophimba, kukamuwona Mulungu Yemwe akuima patsogolo panu, kukawona Mulungu Yemwe akuima pamaso pathu, l—Lawi la Moto. Iye waphimbidwa mu mnofu wa munthu. Koma kodi Shek'nah, kodi iwo unkachita chiyani? Mbewu ya Mkatewowejula, Mawu omwe ife tiyenera kukhala nawo moyo mu tsiku la lero, mwa malonjezo awa, Ulemerero wa Shekinah umachetsa Mkatewowejula uwo, umawuberetsa iwo pochitika, kuwupangitsa iwo kukhala Mkate kwa wokhulupirira; umene umakhala mmasamba a Baibulo, chaka ndi chaka, Mawu a m'badwo uno.

<sup>334</sup> Kwa zipembedzo, Icho ndi chopunthwitsa. Kwa zipembedzo, iwo amapunthwa pa Izo. Kudutsa mu zakazi, Luther, Wesley, Martin Luther, ndi onse, Sankey, Finney, John Smith, Knox, onse ankapunthwa pa Izo.

<sup>335</sup> Koma kodi muchitika chiyani mu masiku otsiridzawa? Kodi "*kuwulula*" ndi chiyani? "Kuzibweretsa!" Kodi Malaki 4 adzachita chiyani? Kudzawatembenuza anthu kuwachotsa ku chopunthwitsa chimenecho, kudzatswa miyambo, ndi kudzawulula Mkate ndi Ulemerero wa Shekinah. Kuwuwona Iwo ukucha ndi kutulutsa ndendende basi zomwe Iwo anati Iwo ukanadzachita, o, mai, Mkatewowejula wa m'badwo uno. Kwa chipembedzo, chopunthwitsa, "gulu la otengeka." Koma, ife amene tikukhulupirira!

<sup>336</sup> Koma tsopano monga Chivumbulutso 10 walonjezera, "Zinsinsi zonse za Mulungu, zimene zakhala zobisidwa mmasamba kudutsa mzaka zimenezo, zidzacha, zidzabweretsedwa mu m'badwo wa Uthenga wa mngelo wa chisanu ndi chiwiri." Kulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.]

Kodi Iye ananena chiyani, chaka ndi miyezi sikisi yapitayo, pafupifupi zaka ziwiri tsopano? "Upite ku Tucson; ukakhale kumpoto kwa Tucson, kuphulika kwakukulu," ndi zimene zikanadzachitika, "Zisindikizo zidzasegulidwa," Zisindikizo zimene zikuwulula zinthu izi. Kubwereranso monga Iye ananenera.

Ndi chiyani chimenecho? Izo zikusonyeza kuti Izo sangakhale munthu. Izo zikugunda mwangwiro, molunjika basi monga momwe izo zingakhalire, nthawi iliyonse. Ndi chiyani chimenecho? Ilo ndi dzanja la Mulungu, mwaona, pamaso pathu. Ndipo chifukwa izo ziri mu kagulu kakang'ono, kophimbidwa mu mnofu wa munthu, izo zaphimbidwa kwa dziko lakunjali. Iye wabisidwa kwa dziko lakunjali. Iye akudziwulula Yekha kwa makanda omwe angathe kuphunzira. Mukuona? Izo nzoona.

<sup>337</sup> Lirilonse, mwaona, fanizo lililonse mu Baibulo, mtundu uliwonse wa Baibulo, ukuwonetseredwa pomwe pano pamaso pathu. Mulungu yemweyo, mu Lawi la Moto, limene linalemba

Baibulo, zonse mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano, ali pomwe pano akuwonetsera Ilo, kusonyeza ndendende basi chimene izo zinali, kutanthauziranso izo mobwereza, ndipo kuzipanga izo motsimikizika kuti ndiko kutanthauzirako.

<sup>338</sup> “Ife tiri nako kutanthauzirako!” Ndiye tiyeni tiziwone izo zikuchitika. Mwaona, ndi zimenezotu, tiyeni tiziwone izo zikuwonetseredwa.

<sup>339</sup> Kuwonetseredwa! Yesu anati, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, musandikhulupirire Ine ayi.” Mwaona, izo ziyenera kutsimikiziridwa.

<sup>340</sup> Koma tsopano—tsopano, osati kutsimikiziridwa monga Yesu, iwo anaika—chisanza kuzungulira mutu Wake ndi kumumenya Iye mmutu, ndikuti, “Ngati Ndiwe Mneneri, tiwuze ife yemwe wakumenya Iwe.” “Ndipo ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, sandutsa mkate uwu.” Mwaona, ameneyo ndi mdierekezi. “Ngati Ndiwe Mwana wa Mulungu, tsika pa- . . .”

<sup>341</sup> Ine ndikutanthauza, Vumbulutso limene Iye ayenera kuti achite, ndicho chimene Izo ziri. Koma tsopano, monga Chivumbulutso 10 akuwululidwa, zinsinsi za Mulungu zikuwonetseredwa, kudziwidwa, monga linalonjezera Bukhu la Chisindikizo cha Chisanu ndi chiwiri.

Tsopano mulole chikhulupiro chanu mwa Iye Yemwe ali Mawu . . . Chifukwa, mu Chivumbulutso 10 amati . . .

<sup>342</sup> Kapena, Chivumbulutso 19, kani. Ine ndinali nditalemba apa, Chivumbulutso 10, tipite kwa iye; koma si 10 ayi, ndi 19. Pamene Iye adzadza, Iye azidzatchedwa, “Mawu a Mulungu,” akukwera pa kavalo woyera, ndipo omutsatira Akumwamba adzakhala kumbuyo kwa Iye.

<sup>343</sup> Muswe chophimba cha maphunziro a chipembedzo! Muswe chophimba cha mwambo wa chipembedzo! Muswe zophimba izo zimene zikumubisa Iye kwa inu! Muswe zophimba izo za kunyada, akazi inu. Ndinu—ndinu ana aakazi a Mfumu; muzichita monga izo, muzikhala moyo monga izo. Muswe chophimba chirichonse, ziribe kanthu zimene Ph.D. ndi LL.D. ikunena. Ngati izo ziri zosiyana ndi Baibulo limenelo, muswe kudutsa chophimba chimenecho!

Pakuti, ife tadutsa chophimba chong’ambidwa. Ife tiri kumbali inayo tsopano, kumbali inayo. Ndipo inu mudzawona, ngati inu mutangochita zimenezo, kuswa miyambo yakale iyo ndi zinthu, ndi kubwera kwa Iye, inu mudzamuwona Iye ataima, Mgonjetsi Wamphamvu, Mawu a lonjezo a m’badwo uno, akuwonetseredwa. Inu mudzamuwona Mulungu Wamphamvu akuvundukulidwa, mudzamuwona Iye ali pakati pathu pomwe pano, atavundukulidwa, Mulungu Wamphamvu, wosagonjetsedwa ndi miyambo.



<sup>344</sup> Iwo anayesera kuti amubise Iye kumbuyo uko; iwo anatero, kwa zaka, koma nthawi ya lonjezo inkayandikira pafupi. Mulungu anadzutsa Mose nthawi ina, ndipo iye anawamasula anawo kukhala amfulu kwa zinthu zimenezo. Ndipo Iye akadali panobe... Iye sangathe kugonjetsedwa. “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita.” Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

<sup>345</sup> Iwo amati, “Izo sizingachitike.” Koma izo zinachitika. Ndiye, pamene izo zinachitika, iwo anati, “Izo ndi za mdierekezi.”

<sup>346</sup> Koma izo sizimasintha Mawu a Mulungu, mpang’ono pomwe. Izo zimakhalabe “Mulungu,” kwa wokhulupirira, “Mgonjetsi Wamphamvu; yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” mwa chikhalidwe Chake, mwa Mawu Ake, Ahebi 13:8.

<sup>347</sup> Ine ndikutseka, ponena izi, chifukwa ndi faivi minisi kuti ikwane thwelofo, ndingonena izi. Ine ndatsala ndi pafupifupi teni, masamba thwelofo ena. Ine ndidzazitenga izo nthawi inayake, mwinamwake usikuuno.

<sup>348</sup> Zindikirani, zindikirani izi. Kunali kugulitsa nthawi ina, ndipo iwo anapeza zeze wachikale. Inu mwaimvapo iyo nthawi zambiri. Zeze wakale; ndipo wogulitsayo anati, “Kodi ichi ndipatsidwa ndalama zingati?” Ine mwina ndikhoza kusalankhula izo molondola, monga mwa ndakatuloyo. Izo zakhala ziri zambiri, zaka zambiri, koma izo zimabwera mmalingaliro mwanga. Ndipo iwo ananyamula zeze wakaleyo, iye samawoneka bwino bwino; amawoneka wotuwa, chirichonse. Iye amalephera ngakhale kuti apeze kugulidwa pa iye. Potsiriza, ine ndikuganiza iye anapeza wina wopereka dolla, kapena chinachake monga choncho.

<sup>349</sup> Ndipo apo panali wina ataima pamenepo yemwe samaganiza kuti iye ayenera kugulitsidwa mtengo umenewo, kotero iye anapita ndipo anakamutenga iye. Iye anamukhwatcha iye mmanja mwake, ndipo anakoka utawo ndi kuupaka utoto iwo, ndipo iye anaimba nyimbo. Ndipo pamene iye anatero, aliyense anayamba kulira. Iwo anali asanayambe aimvapo nyimbo yoteroyo mmoyo wawo.

Kenako wogulitsayo anati, “Kodi ine ndipatsidwa zingati?”

<sup>350</sup> “Thuu sauzande!” “Faivi sauzande!” “Teni sauzande!” Mukuona? Chinali chiyani icho? Dzanja la mbuye linali litaulula chimene chinaphimbika mu ching’wenyeng’wenye chakalecho.

<sup>351</sup> Chimodzimodzinsu lero! Bukhu lakale, Ilo ndi lopanda mawonekedwe, Ilo lakhala likusekedwa, kuwotchedwa, kunyozedwa. Koma nthawi yafika imene iwo ali ndi kugulitsa kwa chipembedzo, Mgwirizano wa Dziko lonse wa Mipingo. Iwo akugulitsa Iyo ngati kaya chiyani. Kudzakhlapo kugulitsa kwa zipembedzo.

<sup>352</sup> Koma, kumbukirani, chiripo chinachake mu Bukhu lakale chimene chinalonjeza kuti padzakhala okonzedweratu, dzanja lodzozedwa lidzabwera tsiku lina, limene liti lidzalitenge Ilo ndi kudzapangitsa Mawu a Bukhu ili, kudzera mu mtima wokonzedweratu, kupita ku ntchito imene Iwo anapangidwira, kudzawulula malonjezo amene ali Mmenemo. Ilo likhoza kuwoneka, o, ngati gulu lakale la oyera-odzigudubuza, kapena chinachake chimzake; koma zimangotengera dzanja la Mbuye, Mawu pa Ilo, kuti liwulule Mawu amenewo, ndipo izo zimakhala zoposa woyera-wodzigudubuza. Ilo lakhala zimenezo kwa mmodzi aliyense wa ife, sichoncho izo, abwenzi? Izo si gulu la otengeka. Izo zimatengera kuti utawo uli pa dzanja la Ndani.

Tiyeni tipemphere.

<sup>353</sup> Atate athu Akumwamba, mwa chikhulupiro lero ine ndikuwona Mbuye wa Bukhu lakale, limene iwo alisinthanitsa ndi miyambo. Iwo alisinthanitsa Ilo ndi zipembedzo. Iwo anayesera kuti aligulitse Ilo. Tsopano iwo akuligulitsa Ilo ndi—ndi Mgwirizano wa Mdziko wa munthu, wa mipingo, achikominisi, achikunja. Kugulitsako kuli mkati, Ambuye.

<sup>354</sup> Mulungu, bweranipo! Ndithudi, Inu mutero. Titumizireni ife mneneri ameneyo, Ambuye, amene akukoka uta umenewo, yemwe akutenga Mawu awa ndi kutsimikizira kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ambiri, Ambuye, agulitsa miyoyo yawo, iwo aponyera kunja miyambo yakale, iwo aswa zophimbazo. Iwo akulifuna Ilo, Ambuye. Iwo apereka chirichonse, chirichonse, mungowapatsa iwo Yesu.

<sup>355</sup> Ambuye, ine ndikuganiza Inu mwatsimikizira Izo kwa iwo tsopano. Iwo abwera kuchokera konsekonse. Iwo amataya zimene akanadya. Iwo amachita chirichonse, kuyesera kuti adzafike ku misonkhano, kuti adzachite zonse zimene iwo angathe, chifukwa iwo apeza Ngale imeneyo ya mtengo wawukulu. Zinthu zinazo ndi zazing’ono kwambiri. Adalitseni iwo, Atate.

<sup>356</sup> Paikidwa pa guwa ili, mmawa uno, Ambuye, mipango. Mwinamwake ena a iwo azichoka lero, msonkhano wa machiritso usanayambike usikuuno. O Mulungu Wamuyaya, yang’anani pansi. Ine ndikudziwa kuti Inu muli pano, Inu mwaphimbika. Ndipo ine ndikutumiza zophimba zazing’ono izi, Ambuye, zotchedwa “mipango,” ndi “zovala” pang’ono, ndi “nsapato” pang’ono za ana aang’ono. Ndipo ine ndikuzitumiza izo ngati maumboni apang’ono a chophimba, zomwe Mawu Anu alalikira pa izo mmawa uno, ndipo, ngati wokhulupirira, ine ndikuika manja anga pa izo, thupi langa, kusonyezera kuti ine ndikukhulupirira Iwo. Ndipo, mwa chikhulupiro, mmodzi aliyense mchipinda chino akuchita chimodzimodzi, Ambuye. Mulole odwala akakhale bwino.

<sup>357</sup> Inu mukhoza kuwakhwacha m—Mawu kuchokera pano, Ambuye, monga wazeze wakale anachitira kwa zeze, muzipange izo chomwecho, Ambuye. Muzipange izo ziyimbe nyimbo yoyenera, uta mdzanja la Mbuye, ndiye ife timuwona Iye ataima pa mbalambanda.

<sup>358</sup> Momwe anthu awo ayenera kuti anaganizira tsiku limenelo, pamene iwo samapereka kalikonse, pamene iwo samapereka kalikonse kwa zeze wakaleyo. Iwo samamufuna iye. Iwo sakanafuna kukhala naye iye mnyumba mwawo. Koma pamene ananyamulidwa ndi yemwe akanatha kumuimba iye, pamene iwo anagulitsa chirichonse chimene iwo anali nacho, kuti amutenge iye. Iwo anali akukangana ndi kumenyenirana iye. Inali nthawi itatha pamene.

<sup>359</sup> Zidzakhala chomwechonso nthawi ina pamene Lipenga la Ambuye lizidzawomba, nthawi idzakhala itatha. Iwo amene amatonzedwa ndi kumasekedwa, amene amaima apo pamaso pa chopimba chotseguka ndipo nkumawawona Mawu a Mulungu akuwonetseredwa (*ena* adzafuula kuwafuna Iwo, koma, monga Inu munanena, “Nthawi idzakhala itatha pamene”), iwo anakalowa mu Phwando la Chikwati; ndipo *iwo* anasiyidwa kunja kumene kuli kulira, kusisima, ndi kukukuta kwa mano.

<sup>360</sup> Mumuthandize munthu aliyense kuti akhulupirire, mmawa uno, Atate; muswe chotchinga chirichonse cha kudzikonda, chotchinga chirichonse cha kusakhulupirira, ndipo amuwone Mgonjetsi Wamphamvu atavundukulidwa pamaso pa okhulupirira. Pakuti, “Taonani, Ine ndidzakhala ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka kumathero a dziko lapansi. Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzamandiwona Ine kenanso, komabe inu muzidzandiwona Ine.” Dzisonyezeni Nokha pakati pathu, Ambuye, monga Inu mwakhala mukuchitira. Zikhale ziri chomwecho kufikira ife tidzawonekere pamaso Panu, pamene en morphe adzakhale atasinthidwa ndipo Inu nkudzakhalanso Mwana wa munthu, ndi Mwana wa Davide. Perekani izi, Ambuye, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu.

Pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, tonse mu pemphero.

<sup>361</sup> Ndikudabwa lero ngati alipo ena pano amene...mkati kapena kunja. Palibepo njira yomwe tingabweretsera kuitanira pa guwa apa, chifukwa palibepo malo. Koma ine ndikudabwa, moonamtima, kodi inu mukukhulupirira izi kuti ndi Choonadi? Kodi inu mukukhulupirira kuti mu tsiku ili limene ife tiri nkukhalamo, ndi chisokonezeko chonse ichi ndi m’badwo wa sayansi wonga umene unali mu masiku a Nowa, mu masiku a Mose, masiku a Khristu, Mulungu ameneyo, Atate wamkulu wa ife tonse amene tabadwira mwa Iye, akuima pakati pathu lero?

<sup>362</sup> Lawi la Moto lowonekera ili limene linatsimikiziridwa mwasayansi, zaka zambiri zapitazo, ndiri mnyamata

wamng'ono, linalankhula ndi ine kunja uko ndipo linandiuza ine kuti ndizidzakhala komwe kuno, zomwe zikanati zidzachitike. Ndinakuuzani inu za izo, ndiyeno Ilo... Tsiku lina uko pa mtsinje, utumikiwo usanayambe, chitsitsimutso choyamba, Iye anawonekera mlengalenga, anazizindikiritsa Yekha ndipo anapereka kutumako. Zaka zonsezi ine ndakhala ndikuzibisa izo mu mtima mwanga, kumuphimba Khristu, Lawi la Moto lomwe lija likutanthauzira Mawu, monga zinalonjezedwa. Ife tiri mu tsiku lotsiriza, basi Kudza kwa Ambuye. Ndipo ngati inu muzipeza nokha kunja kwa chophimba chimenecho, chimene chiri imfa kukhala kunjako, kodi mutero inu mwa chikhulupiriro, mmawa uno, kunena kuti, "Mwa thandizo la Mulungu. Ndipo ndi thandizo Lanu, Ambuye, ine ndikufuna kuti ndiswe chophimba chimenecho. Ine ndikufuna kuti ndikafike kumene Inu muli, kuti ndikawawone Mawu athunthu a Mulungu"?

<sup>363</sup> Musayesere kuti mukhale Mose. Musayesere kuti mukhale Aroni. Musatero. Mungokhala yemwe inu muli, koma mukhale Mkristu.

<sup>364</sup> Kodi mutero inu, ndi mitu yanu yoweramitsidwa, mungakwezere manja anu kwa Mulungu, ndikuti, "Ambuye Mulungu, mundithandize ine mkati mwa chophimbamo"? Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Ndizo, tangoyang'anani manjawa!

<sup>365</sup> Kunjako, kumbukirani, ine ndikhoza kusaliwona dzanja lanu. Izo si—izo si zoyenera kwambiri kuti ine ndiwawone iwo, mulimonse; izo ndi, Mulungu. Izo ziri kokha, kwa ine, izo zikungondipanga ine kuwona kuti—Mbewu yagwera penapake, ndipo, koma Mulungu amawona mtima weniweni.

<sup>366</sup> Ngati alipo ena aliwonse amene sanakweze manja awo, akufuna kuti akweze tsopano, mukweze manja anu ndi kukumbukiridwa mu pemphero. Kwezani manja anu. Mulungu akudalitseni. Zimenezo ndi zabwino. Mulungu akudalitseni inu.

<sup>367</sup> Atate, ife tikupemphera lero kuti awa, Ambuye, amene sanadutsebe chophimba icho. Iwo aima kunja uko monga Israeli; iwo akupenyera. Iwo akukhulupirira, koma iwo sanabowolezebe kukalowa mu Ichi apabe, kuti akakuwone Kuwala kwa Shekinah kwakukulu kuja, zonse ziwiri mwauzimu ndi mwathupi, mwakuti diso la makina la kamera likujambulabe chithunzi; pafupi masabata awiri apitawo, anajambulanso Iko kachiwiri. Inu mukudziulula Nokha, Ambuye, Mulungu Wamphamvu kuvundukulidwa kwa wokhulupirira; ndiwophimbidwabe kwa wosakhulupirira; koma wovundukulidwa kwa wokhulupirira.

Mulole iwo abowoleze, lero, Ambuye, akawone kuwala Kwake kwakukulu ndi Ulemerero. Mulole mitima yawo isinthidwe ife tisanabwerere nkomwe ku tchalitchi usikuuno.

Mulole iwo onse adzazidwe ndi Mzimu Wanu, Kukhalapo Kwanu. Mulole Mbuyeyo atenge chikhulupiriro chimenecho chimene iwo ali nacho, achiyendetse icho kudutsa pa Mawu; mulole nyimboyo iyimbenso, “Inu munadzozedweratu, asanaikidwe maziko a dziko lapansi, kuti mudzakhulupirira Izi. Khulupirira, mwana Wanga, ndipo upulumutsidwe.”

<sup>368</sup> Atate, Mulungu, ife tikuwapereka iwo mmanja Mwanu tsopano, tikuzindikira kuti palibenso china chimene ife tingathe kuchita. Zonsezo ziri ndi Inu tsopano, Atate. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana Wanu. Ameni.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye  
 Anafukwa . . . anayamba kundikonda ine  
 Anandigulira chipulumutso changa  
 Pa mtengo wa Kalvare.

<sup>369</sup> Kodi mukunkonda Iye? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

Wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu ali kwa ine,  
 Wauphangu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu  
 Wamphamvu Iye ali;  
 Iye akundipulumutsa, akunditeteza kwa  
 tchimo lonse ndi manyazi,  
 Wodabwitsa Muomboli wanga, mtame Dzina  
 Lake!

Ine nthawi ina ndinali wotaika, tsopano ine  
 ndapezeka, mfulu ku kutsutsika,  
 Yesu akupereka ufulu ndi chipulumutso  
 chathunthu;  
 Kundipulumutsa ine, kunditeteza ine kwa  
 tchimo lonse ndi manyazi,  
 Wodabwitsa ali Muomboli wanga, mtame  
 Dzina Lake!

O, wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu ali kwa ine,  
 Wauphangu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu  
 Wamphamvu Iye ali;  
 O, kundipulumutsa, kunditeteza kwa tchimo  
 lonse ndi manyazi,  
 Wodabwitsa Muomboli wanga, mtame Dzina  
 Lake!

<sup>370</sup> Ndi angati akumuwona Iye ataima, Mgonjetsi Wamphamvu, Mawu atasandulika thupi, akuvundukulidwa pamaso pathu; Alfa, Omega; Iye amene Anali, Yemwe Ali, ndipo Adzadza; Muzu ndi Mphukira ya Davide; anali Mwana wa munthu, Mwana wa Mulungu, Mwana wa munthu, ndipo adzakhala Mwana wa Davide? Inu mukukhulupirira Izo ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Kudzivundukula Yekha mu m’badwo uliwonse, kubweretsedwa kwa wokhulupirira, kudziphimba Yekha mu mnofu wa munthu

kwa wosakhulupirira. Iye wabisika kuseri kwa chophimba. Mulungu ataswa chophimba chirichonse, ndipo ife timuwone Iye mmene Iye aliri!

Yesu anadula unyolo,  
Yesu anadula unyolo,  
O, Yesu anadula unyolo,  
Pamene Iye anakumasulani!

Kutsidya kwa Yorodani,  
Mminda yokoma ya Edeni  
Komwe Mtengo wa Moyo ukuyanga,  
Uko kuli mpumulo wa ine.

Yesu anadula . . .

Kodi inu simukufuna kuti muwoloke Yorodani tsopano? Kodi simunatope mu chipululu? Tiyeni tipite uko mu malonjezo!

Yesu anadula unyolo,  
Yesu anadula unyolo,  
O, pamene Iye anakumasulani!

<sup>371</sup> Tiyeni tikweze dzanja lathu tsopano.

Ine nthawizonse, ndidzamtama Iye,  
Ine nthawizonse, ndidzamtama Iye,  
Ine nthawizonse, ndidzamtama Iye,  
Poti Iye wandimasula!

<sup>372</sup> Ameni! Kodi zimenezo sizikukupangani inu kumverera bwino? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] O, ndi zodabwitsa bwanji! Ndi zodabwitsa bwanji, sichoncho Iye, ndiye? Tiyeni tigwirane chanza wina ndi mzake tsopano, tikuti:

Yesu anadula unyolo,  
Yesu anadula unyolo,  
O, Yesu anadula unyolo, (Mulungu akudalitseni inu, m'bale.)  
O, ndipo Iye anakumasulani!

Ine nthawizonse, ndidzamtama Iye, (Mulungu Wamphamvu)  
Ine . . . (“Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” anangosintha mawonekedwe Ake.) . . . ndidzamtama Iye,  
Ine nthawizonse, ndidzamtama Iye,  
Pakuti Iye (anandichotsera tizikhulupiriro tonse kutali ndi ine) anandiika ine . . . (kuti ndizikhulupirira Mawu Ake).

<sup>373</sup> O, kodi simukumva Zeze wa Mbuye akulira kutsidyako, uta ukukhwatchidwa pa Mawu awa? Iye ali yemweyo dzulo, lero!

Ine nthawizonse, ndidzamtama Iye,  
 Ine nthawizonse, ndidzamtama Iye,  
 Ine . . . (Iye, Mawu!) . . . nthawizonse,  
 nthawizonse ndidzamtama Iye, (Kodi Iye  
 anachita chiyani?)  
 Pakuti Iye (kuseri kwa katani) anandimasula  
 ine!

<sup>374</sup> Matamando akhale kwa Mulungu! Ine ndikunkonda Iye. Kodi inu simukunkonda Iye? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi izi si Zakumwamba? [“Ameni.”] Ine ndimakonda gawo ilo la Mawu, mwaona, Mzimu Woyera basi mwanjira yokoma, yodzichepetsa iyo. Ine—ine ndimangozikonda Izo. O, tangoganizani!

Kumbali ina ya Yorodani, (ine ndikuyandikira  
 kumeneko tsopano)  
 Wokoma . . . (wachisavundi) wa Edeni, . . .  
 (Kodi ine ndikapezako chiyani kumeneko?)  
 Kumene Mtengo wa . . . (mmememo munali  
 mmunda wa Edeni) mukuyanga,  
 Kuli mpumulo wa ine.

<sup>375</sup> Inu mukufuna kuti muzipita? Iye anadula unyolo.

Yesu anadula (mwambo uliwonse) unyolo  
 uliwonse,  
 Yesu anadula unyolo uliwonse (zipembedzo  
 zonse, tizikhulupiriro tonse),  
 Anadula unyolo uliwonse,  
 Ndipo Iye anakumasulani!

<sup>376</sup> Matamando akhale kwa Mulungu! Ine ndimangonkonda Iye. Nzosadabwitsa Yesaya anati, “Iyeyo ndi Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha, Wodabwitsa!”

Wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu ali kwa ine,  
 Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu  
 Wamphamvu Iye ali;  
 O, kundipulumutsa, kundisunga kuchokera ku  
 tchimo lonse ndi manyazi,  
 Wodabwitsa, Muomboli wanga, mtame Dzina  
 Lake!

<sup>377</sup> O, mai! Zimenezo zimasuntha mtima wanga. Ndi wodabwitsa bwanji Iye! Ine ndikukuuzani inu, kulibeko mapeto kwa Izi. Izi, ine ndinabwera mu Izi zaka sate-firii zapitazo, ndikumverera mwanjira iyi. Ndipo ngati Iye achedwa, tsiku lina ine ndidzatseka maso anga, ine ndidzachokapo mwanjira yomweyo. Ameni!

Wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu ali kwa ine,  
 Wauphungu, Kalonga wanga wa Mtendere,  
 Mulungu Wamphamvu Iye ali;  
 Iye kundipulumutsa, Iye kunditeteza kwa  
 tchimo lonse ndi manyazi,  
 Wodabwitsa, Muomboli wanga, mtame Dzina  
 Lake!

<sup>378</sup> Ine ndikhoza kukhala pano tsiku lonse, mu Zimenezo. Paulo anati, “Ngati ine ndikuimba, ine ndiziimba mu Mzimu.” Uhuh. “Ngati ine ndikulalikira, ine ndizilalikira mu Mzimu. Ngati ine ndikuyenda, ine ndiziyenda mu Mzimu. Ngati ine ndikulankhula, ine ndizilankhula mu Mzimu.” Mulole chirichonse chizichitika ndi Mawu ndi Mzimu. Inde, bwana. Ameni! Zonsezo ndi Choonadi cha Mulungu.

<sup>379</sup> Ine ndikumuwona Iye, Mulungu Wamphamvu, wovundukulidwayo. Ine ndikumuwona Iye akukang’anulapo tizikhulupiriro, zipembedzo; akukang’anulapo—otsutsa, mapurogramu amaphunziro, ndi chirichonse; akuyenda chamtsogolo, ataima pamenepo. Inu mukuganiza kuti tizikhulupiriro tingamugonjetse Iye? Inu mukuganiza kuti zipembedzo zingamugonjetse Iye? Inu mukuganiza kuti Mgwirizano wa Mdziko ungate kumugonjetsa Iye? Iye anagonjetsa chirichonse, anadula unyolo uliwonse, anakatsegulako ku gehena; anamatulapo chisindikizo, anakalowako ku malo Oyeretsetsa; anadzivundukulako Yekha kwa ife, kuti ndi Mawu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ameni. Ine ndikunkonda Iye.

<sup>380</sup> Tsopano, mpaka tidzakomane madzulo ano, ife tikufuna kuti tichite chinthu chimodzi, chimenecho ndicho:

Tenga Dzinalo la Yesu,  
 Mwana wachisoni ndi watsoka;  
 Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,  
 O, litenge Ilo kulikonse upita.  
 Dzina lofunika, O nlokoma bwanji!  
 Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo  
 cha Kumwamba;  
 Dzina lofunika... (Eya, ine ndawapeza kale,  
 iwo.) . . . O nlokoma bwanji!  
 Chiyembekezo cha padziko ndi . . . (...? . . .)

<sup>381</sup> Ngati Satana ayesera kuti akuyeseni inu, kuti inu simukuyang’ana pa chinthu cholondola, mumulozere iye ku Mawu monga Yesu anachitira. Mukuona? Mukuona? Ameni!

Pa Dzina la Yesu kugwada,  
 Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,  
 Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka  
 Iye korona,  
 Pamene ulendo wathu watha.




Dzina lofunika, Dzina lofunika!  
 Chiyembekezo cha pa dziko ndi chisangalato  
 cha Kumwamba;  
 Dzina lofunika, O nlokoma bwanji!  
 Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo  
 cha Kumwamba.

<sup>382</sup> Billy adzakhala muno, pafupifupi sikisi koloko, kudzapereka makadi a pemphero kwa iwo amene akufuna abwere mu mzere wa pemphero. Ine ndikuganiza zikhala bwino kuti tichite zimenezo. Ife tinali oti sititero, koma, pokhala kuti ndife unyinj, ife zikhala bwino kuti tichite zimenezo, inu mukuona.

<sup>383</sup> Tsopano muzimukumbukira Iye! Muzimuika Iye nthawizonse mmalingaliro anu, mu mtima mwanu. Kulikonse kumene inu mukupita, mwaona, muzimuika Yesu mmalingaliro mwanu.

Tenga Dzinalo la Yesu (tsopano mvetserani)  
 nawe,  
 Monga chishango ku msampha uliwonse;  
 (chimachitika ndi chiyani?)  
 Pamene mayesero akusonkhanira iwe, (kodi  
 inu muzichita chiyani?)  
 Muzingopuma Dzina loyera ilo mu pemphero.  
 Dzina lofunika, Dzina lofunika, O nlokoma  
 bwanji!  
 Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo  
 cha Kumwamba;  
 Dzina lofunika, O nlokoma bwanji!  
 Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo  
 cha Kumwamba.

<sup>384</sup> Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano. Ine ndiwapempha abusa ngati iwo angabwere ndi kudzabalalitsa gululi. M'bale Neville, Mulungu akudalitseni inu, M'bale Neville. 

*KUVUNDUKULIDWA KWA MULUNGU* CHA64-0614M  
(The Unveiling Of God)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Juni 14, 1964, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A. Unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mu chaka cha 2015 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2017 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)